# DEMOCRATIC PROGRESSIVE PARTY

## KUBWEZERETSA BOMA LA ANTHU, LODALILIKA.

2025-2030

# Manifesto


VOTE
DPP 2025


DPP
BINGU
BINGU

# MKATIMU

MAWU OTSOGOLERA 5
MASOMPHENYA ATHU NDI AMALAWI TONSE 9
CHOLINGA CHATHU 9
LONJEZO LATHU 9
TIYENDE PAMODZI 9
1: PANO TILI PATI? 10
2: MALONJEZO 14
3: KAYENDETSEDWE KA CHUMA 16
3.1 KUKHAZIKIKA KWA CHUMA 17
3.2 THUMBA LA CHUMA 21
3.3 KUKULITSA CHUMA CHATHU 21
3.4 KUGWIRITSA BWINO NTCHITO MISIKA YA NDALAMA 21
4:NSANAMIRA ZA CHITUKUKO 22
4.1 ULIMI WOCHITA MWA BIZINEZI 23
4.2 NTCHITO ZA MAFAKITARE 27
4.3 CHITUKUKO CHA M'MATAUNI 37
4.4 NTCHITO ZOKOPA ALENDO 38
4.5 KUKHAZIKITSA MIZINDA INA 40
4.6 NTCHITO ZA MALO, NYUMBA NDI MADZI 41
4.7 KUPEREKA MPHAMVU KWA ANTHU 43
5: ZOTHEKERA 46
5.1 KUSINTHA MAGANIZIDWE 47
5.2 ULAMULIRO WOTSATIRA MALAMULO, KAYENDETSEDWE KABWINO KA DZIKO NDI NKHONDO YOLIMBANA NDI ZIPHUPHU 48
5.3 KAGWIRIDWE NTCHITO KA BOMA 57
5.4 MAKAMPANI OMWE SIABOMA, MAFAKITALE NDI MALONDA 59
5.5 NTCHITO YOKWEZA MALUSO A ANTHU 63
5.6 NKHANI ZOSAMALA CHILENGEDWE NDI KUPEWA NGOZI ZODZA MWADZIDZIDZI 83
5.7 MABUNGWE OMWE SIABOMA: ATOLANKHANI, MABUNGWE ENA NDI ZIPEMBEZO 85
5.8 NTCHITO ZA MALUSO 89
6: KUMEMEZA AMALAWI NDI ABWENZI ATHU ONSE 90
VOTERANI DPP! BOMA LA A PETER! 92

# MAWU OTSOGOLERA

Chipani cha DPP chabweranso ndi ndondomeko zoyendetsera dziko la Malawi kuchokera chaka chino cha 2025 kufikira chaka cha 2030. Mu ndondomeko imeneyi Chipani cha DPP chikufuna kupitiriza kutukula miyoyo ya a Malawi kudzera mu chuma, ndi zitukuko zowakomera, komanso kulemekeza maufulu a anthu muno m'Malawi. Zonsezi zitsata dongosolo la Malawi 2063, makamaka la mzaka khumi zoyambirira malingana ndi lamulo lokhuza zipani lotchedwa Political Parties (Amendment) Act Yoyamba ya m'chaka cha 2022.

Dziko la Malawi likukumana ndi mavuto ambiri monga njala, nthenda ndi ulova chifukwa choti mizati ina ya chitukuko siili m'malo mwake. Chipani cha DPP ndi utsogoleri wake chibweretsa mayankho a zimenezi chikatenganso boma pa 16 Sepitembala pano. Mzaka zimene DPP inalamulira dziko lino pakati pa 2014 ndi 2020 palibe munthu amene anafa ndi njala m'dziko muno. Choncho kuchokera chaka chino cha 2025 kupita mtsogolo, DPP ipitiriza zimenezi komanso kuonetsetsa kuti chitukuko cha dziko lino ndi chokhazikika.

Mu nthawi ya ulamuliro wa DPP chuma cha dziko chimayenda bwino, ndipo chitukuko chinali chokhazikika. Koma litabwera boma limene lilipoli, chuma ndi chitukuko zonse zaonongeka momvetsa chisoni. Boma la DPP libwezeretsa zinthu m'malo mwake, ndipo lipitiriza kukhala dziko lopanga katundu wosiyanasiyana nkumagulitsa kunja kwa dziko lino, komanso kubweretsa ndalama yakunja imene imafunika pa chitukuko cha dziko. Ifetu ndi a DPP ndipo tikalonjeza zinthu, timakwaniritsa.

Pansi pa ulamuliro wa DPP Malawi sadzakhala chimodzimodzi. Tidzakwaniritsa mfundo yoti Malawi akhale wolemera ndi wodzidalira yekha, komanso dziko lokhala ndi mafakitare opindulira anthu. Tinalonjeza m'chaka cha 2019 kuti Malawi adzakhala pakati ndi pakati pakulemera pofika chaka cha 2030. Panonso tikunena kuti tithamanga ndi masomphenya omwewo kuti dzikoli likhale lokoma ndi lodalirika kwa a Malawi onse. Boma la DPP lidzakwaniritsa malonjezo amene ali m'ndondomeko zimene zili mu manifesto imeneyi.

Chipani cha DPP chayesedwa pa miyeso yosiyanasiyana ndipo chaonetsa a Malawi kuti ndi Chipani chodalirika pa kayendetsedwe ka chuma ndi dziko. Pamene DPP imalowa m'Boma mchaka cha 2014 chuma cha Malawi chinali chitasokonekera:

Kukwera kwa mitengo ya zinthu kunali pa muyeso wa 27 mu 100 iliyonse (27 peresenti). Boma lathu linatsitsa muyesowu mpaka kufika pansi pa 10 peresenti.

DPP inapeza ngongole yaikulu kwambiri mofanana ndi chuma chonse chimene dzikoli chinali nacho.

Ndalama zakunja zinali zochepa zosakwanira kuyitanitsa

katundu kunja kwa dziko ndi mwezi umodzi womwe.
Maiko ndi mabungwe akunja omwe anali kuthandiza dzikoli anasiya chifukwa cha kusakazika kwa ndalama za boma kudzera mu umbava wotchedwa Cashgate, womwe unachitika ndi Boma lanthawiyo.
Titangolowa m'Boma kunabwera namondwe yemwe anakokolola mbeu, nyumba ndi katundu wina wambiri.
Pakutha izi panagwa chilala chomwe chinabweretsa vuto la njala.

Koma tikuthokoza Mulungu kuti pakanthawi kochepa mavuto a njala ndi umphawi anachoka pamene tinagwira ntchito molimbika ndi kubwezeretsa chuma m'chimake pofika chaka cha 2020. Pakadalli pano, dziko la Malawi liri m'mavuto aakulu a za chuma pansi pa ulamuliro wa MCP. Anthu ali m'mavuto osaneneka, ndipo maufulu a anthu akuphwanyidwa chifukwa cha ndale zomwe boma limene lilipoli likutsata. Boma la MCP laonetsera poyera kuti ndi boma lomwe silidziwa chimene likuchita. Ndiponso ndi boma loononga chuma cha dziko. Komanso ndi boma lozunza anthu ake ndinso lopanda umunthu. Boma lachonchi silinakhalepo m'Malawi muno kuyambira pachiyambi.

Pamene tikupita ku zisankho pa 16 Sepitembala 2025, kukwera kwa mitengo ya zinthu kwaposa kale 30 peresenti. Ulova waposa 90 peresenti. Ngongole ya dziko yafika pa 16 triliyoni Kwacha, zomwe ndi zofanana ndi 80 peresenti ya chuma chonse cha dziko la Malawi. Ndalama zakunja kulibe. Chuma cha Malawi n'chosweka. Ndipo dziko la Malawi liri pamoto woopsa. Chipani cha DPP chimalonjeza zinthu zokhazo zimene icho chingathe kuchita. Osati kunamiza anthu. M'chaka cha 2014 tinalonjeza kuti tichepetsa chiwerengero cha mabanja omwe amakhala ndi njala chaka ndi chaka. Ndipo izi zinachitika. Tinalonjezanso kuti tidzakhwimitsa chitetezo cha pa anthu, katundu wawo ndi mabinezi. Izinso zinachitika. Zina zomwe tinalonjeza ndi kuchita zinali izi: kulimbikitsa ntchito za makompyuta ndi ntchito zothandizira anthu kuchita malonda, kukuza ntchito zaumoyo, kukweza ntchito za maphunziro, kulimbana ndi katangale, kusintha kayendetsedwe ka ntchito za boma, kuonetsetsa kuti anthu ali ndi malo abwino ogona, komanso kupereka ndalama kwa anthu osowa ndi okalamba. Tinalonjezanso ndi kukwaniritsa ndondomeko yopereka zipangizo zaulimi zotchipa ndi kumanga ma koleji a zaumisiri ndi luso kumidzi, mwa zinthu zina zambiri.

Ife a DPP tinalonjeza kusintha kayendetsedwe ka chuma kuti chizikula ndi kukhala chokhazikika. Ndipo izi zinachitika, ngakhale panali zosamwitsa zina ndi zina monga mavuto ogwa mwadzidzidzi. Cholinga chenicheni cha bukhu la malonjezanoli (manifesto) ndi kufotokoza mfundo zomveka zokwezera chuma m'Malawi muno, powerengera kwambiri miyoyo ya achinyamata. Boma la DPP lidzatsindikiza mapulogaramu okweza chuma ndi chitukuko muno m'Malawi ndi kuchotsa zotchinga zonse. Nsanamira zitatu izi za mu Ndondomeko ya Malawi 2063 zidzatsatidwa: 1) Kutukula ulimi kuti ukhale monga bizinezi, 2) Ntchito za mafakitare, ndi 3) Chitukuko cha m'matauni.

Mapologalamu ena ochokera mu Ndondomeko ya Malawi 2063 adzathandizira mfundo za m'manifesto iyi, monga: Kusintha kaganizidwe (Mindset Change), Ulamuliro wotsata malamulo (Rule of Law), Chitetezo (Security), Ubale ndi maiko ena (International cooperation and diaspora), Kuchita bwino kwa mabungwe a boma (Public Sector Performance), Kuchita bwino kwa makampani osakhala a boma (Private Sector Dynamism), Kukuza maluso a anthu ogwira ntchito (Human Capital Development), Maphunziro (Education), Umoyo (Health), Achinyamata (Youth), Kukweza ntchito za Amayi (Women Empowerment), anthu omwe alibe kuthekeka (Disadvantaged Persons), Chilengedwe chokhazikika (Environmental Sustainability); mabungwe omwe si aboma (Non-state actors), ndi ntchito zaluso (Creative Arts).

Kudzera mu manifesto iyi, DPP idzapanga zofuna aMalawi, ndipo chitukuko cha dziko lino chidzapita patsogolo mu zaka zochepa. Tidzabweretsa ntchito zokhazikika kwa a Malawi. Ndipo ndalama za boma tidzagawa moyenera m'madera monse m'mene mukufunika chitukuko.

Boma la DPP lidzapereka ndalama zokwana 5 biliyoni kwacha chaka chilichonse pa dera la phungu wina aliyense (konstichuwense) zochitira chitukuko. Izi zikutanthauza kuti wodi (ward) iliyonse idzalandira pafupifupi 2 biliyoni kwacha ndi theka (K2.5 biliyoni) pa chaka. Poonjezera apo, konstichuwense iliyonse idzalandira 100 miliyoni kwacha yoti amayi azipangira mabizinezi. Achinyamata nao mu konstichuwense iliyonse adzakhala ndi thumba la ndalama zokwa 100 million kwacha ya ma bizinezi chacha ndi chaka.

DPP imadziwa kuti a Malawi ali ndi maluso ambiri amene sakugwiritsidwa ntchito mokwanira pa ntchito za chitukuko. Pachifukwa ichi tidzapereka ndalama zokwana 50 miliyoni kwacha ku konstichuwense iliyonse kuti ikhale yoyendetsera masewero ndi maluso ena. Tidzaonetsetsanso kuti nzeru za makina ndi ma kompyuta zogwira ntchito ngati anthu (artificial intelligence) ndi zina zotero zikugwiritsidwa ntchito kwambiri ndiponso moyenera mu ntchito za boma ndi ntchito zina zakunja kwa boma.

Kudzera mu ndondomeko za Mphamvu ku anthu (disentorolaizeshoni / decentralisation) tidzalemba ntchito anthu odziwa bwino ntchito zawo (mapolofeshonolo) osachepera 229 monga ma dairekitala kukagwira ntchito mu makonstichuwense. M'menemo mudzakhalanso ogwira ntchito zosiyanasiyana, monga ma injiniya, madokotala, manesi, maodita, a kafukufuku, antchito za manja, ndi ena ambiri.

DPP ndi chipani cha anthu.


Cholinga cha DPP ndi kukhala ndi ubale wabwino ndi maiko ena akunja kwenikweni pankhani za malonda ndi chuma. Choncho m'manifesto iyi muli mfundo zonse za United Nations, zija amati 2030 Sustainable Development Goals (SDGs), 2063 African Unnion Agenda, Istanbul Programme of Action (IPoA), Vienna Programme of Action (VPoA), Southern African Development Community Regional Indicative Strategic Plan (SADC RISDP), Common Market for Eastern and Southern Africa (COMESA) Treaty, African Continental Free Trade Area (CFTA) ndi zina ambiri. DPP imakhulupirira kuti Malawi sali yekha ngati chilumba; koma ali mbali imodzi ya dziko lonse lapansi.

M'malo mwa DPP, ndili wokondwa kuitana a Malawi onse omwe ali mu dziko muno ndi kunja kwa dziko lino kuti mugwirane manja ndi DPP kuti tigwire ntchito limodzi pa ndale, ndi chitukuko cha chuma ndi miyoyo ya anthu. Ndikuitananso anthu a mitundu yonse monga azungu a ku Ulaya, Amereka, Amwenye, Aluya ndi anthu a mitundu ina yonse amene mumakhala m'dziko muno, kuti tigwirane manja pokweza Malawi. Izi nzofunikira kuti ana athu, ndi zidzukulu zathu ku mibadwo yonse, akhale ndi dziko laufulu ndi lotukuka.

Musaiwalenso kuti Boma la DPP ndi limene linabweretsa mfundo yoti nzika za Malawi zikhoza kukhalanso nzika kumaiko ena, ngati nzika za maiko awiri. Pano mfundo imene ija inakhala lamulo lokhazikika. Pakutsata mfundo za mu Ndondomeko za Malawi 2063, dzikoli lidzatukuka m'nthawi yochepa kwambiri. Mfundozi ndi monga: Kukonda dziko lathu (Patriotism), Kugwira ntchito molimbika ndi mokhulupirika (Integrity and Hard work), Ulimi wa bizinezi (Agriculture commercialization), ndi Kukweza ntchito za mafakitare ndi chitukuko cha m'mtauni (Industrialisation and Urbanisation).



DPP yakonzeka kukweza dziko lino kuchokera pamene liri, kufikira pa mulingo wa Malawi wodzidalira pa ntchito za mafakitare ndi chuma pofika 2030, ndipo pofika m'chaka cha 2063 dziko la Malawi lidzakhala lolemera.
VOTERANI DPP.



**H.E. PROF. ARTHUR PETER MUTHARIKA**
**PRESIDENT, DEMOCRATIC PROGRESSIVE PARTY,**
**PAGE HOUSE, MANGOCHI, MALAWI**

## MASOMPHENYA ATHU NDI AMALAWI TONSE

Malawi wa anthu olemera ndi wodzidalira pa ntchito ndi chitukuko.

## CHOLINGA CHATHU

Cholinga chathu ndi kukhazikitsa ndondomeko zoti Malawi akhale ndi chuma chokwanira ndi kukhala wodzidalira kudzera mu kayendetsedwe ka boma; kuchita zinthu poyera ndi kuonetsetsa kuti aMalawi akutha kupeza zosowa zamoyo wao mosavuta. Izi zidzatheka poika ndondomeko zothandizira kuti anthu azitha kupeza chuma, kugwira ntchito molimbika, ndi kuyambitsa ntchito zopititsa chitukuko cha dziko patsogolo. Boma lathu lidzagawa bwino chuma kwa magulu onse a anthu ndi kukweza ntchito za malonda m'Malawi muno komanso kunja.

## LONJEZO LATHU

Malawi adzakhalanso wopanda njala. Chuma cha Malawi chidzakula ndi kukhala chokhazikika mofulumira. Tidzatukula dziko lathu ndi chuma chopanga tokha ndi cholinga choti tikwaniritse masomphenya okhala dziko lolemera ndi kudzidalira pa ntchito ndi chitukuko, pofika m'chaka cha 2063. Ntchito zathu zamafakitale zidzapita patsogolo pogwira ntchito ndi nthambi zoyendetsa mafakitare. Tidzakwaniritsa masomphenya onse pogwira ntchito ndi nthambi zonse zoyenera pa ntchitoyi.

Chitukuko chathu chidzakhazikika pa zofuna za anthu, ndipo ndale zathu zidzatsamira pa chitukuko basi. Utsogoleri wathu udzakhala wabwino, kwenikweni pokweza chuma cha dziko lino ndipo tidzagwira ntchito ndi a Malawi onse. Kuposa zonse, tikutsindika kuti tidzaonetsetsa kuti malonjezano athu onse akwaniritsidwa. Ndipo a Malawi onse adzapindula ndi ntchito zimenezi, osati anthu ochepa okha ayi. Ngodya zathu zidzapitirira kukhala: Kukonda dziko lathu (Patriotism), Kukhala wodalirika (Integrity) ndi Kugwira ntchito molimbika (Hard work).

## TIYENDE PAMODZI

Ife a DPP timakhulupirira kuti dziko lino kuti lipite patsogolo, pakufunika kuti mitundu yonse ya mu zigawo zonse tikhale ogwirizana. Dziko lino ndi la anthu onse, ndi mitundu yonse, ndipo m'gwirizano ndi wofunika kwambiri. Choncho pakuyenera kuti oyendetsa boma, ndi omwe ali kunja kwa boma azikhala ndi masomphenya ofanana otumikira aMalawi modalirika ndi modzipereka. Kusiyana kwa mitundu ndi zigawo zisatilepheretse kugwira ntchito limodzi potukula dziko lathu lokongola la Malawi.

*Mu umodzi muli mphamvu. Mu mphamvu tipanga Malawi wotukuka kuyambira lero mpaka mibadwo imene ili nkudza.*




# 1

# PANO TILI PATI?

Ndi zomvetsa chisoni kuti mpaka lero Malawi adakali m'gulu la maiko osaukitsitsa padziko lapansi. Izi ndi zosavomerezeka ndipo zikuyenera kusintha. DPP idzasintha dziko lino kuti likhale lolemera ndi kudzidalira pa ntchito ndi chitukuko molingana ndi Ndondomeko ya Malawi 2063.

Kuchokera nthawi ya ulamuliro wa Kamuzu kufikira pano, dziko la Malawi lakhala likudalira ulimi ngati njira yopezera chuma cha dziko komanso ndalama zakunja. Vuto limene liripo ndi loti dzikoli silikwanitsa kutumiza kunja zokololazi zili m'mapaketi oyenera ochokera mu mafakitale. Dzikoli limatumiza zokolola zake kunja monga m'mene takololera. Chifukwa cha ichi katundu wathu amagulidwa motsika mtengo m'misika yakunja. M'chitidwe uwu subweretsa ndalama zakunja zambiri. Vuto lina ndi lakuti ulimi wathu umadalira mvula imene imagwa mwa njomba. Komanso nthawi zina kumakhala chilala kapena kusefukira kwa madzi. Izi zimapangitsa kuti dziko lisakhale ndi zokolola zochuluka.

Ife a DPP tikudziwa kuti chuma cha dziko lino chakhala chikupsyinjika ndi zovuta zambiri. Zina mwa zopsyinjazo ndi izi: miseu ndi milatho yosalongosoka, nyumba zaboma zosakwanira komanso zosayenera; kusatsata ndondomeko za boma popanga zinthu; katangale; kukwera kwa chiwerengero cha anthu; kusakhazikika kwa mfundo zoyendetsera chuma, mavuto ogwa mwadzidzidzi, kudwaladwala ndi kuchepa kwa maphunziro zomwe zimapangitsa ogwira ntchito kugwira ntchitoyo mosakwanira, ndi zina zambiri. DPP ikudziwanso kuti pali mbali zina za chitukuko cha dziko lino zimene zili ndi kuthekela kobweretsa ndalama zochuluka zoyendetsera boma ndi kutukula miyoyo ya a Malawi. Madera amenewa ndi monga mafakitare, zokopa alendo ndi migodi. Koma zimene zikuchitika m'madera amenewa ndi zosakwanira chifukwa cha kuchepa kwa chidwi komanso kulephera kwa boma pa ntchitozi. Enanso mwa mavutowa ndi kuchepa kwa mphamvu za magetsi, kuchepa kwa maluso, kupanda ndondomeko ndi kuchepa kwa mpamba wotukulira mafakitare, zokopa alendo ndi migodi.

Chiwerengero cha anthu m'dziko lino chikuposa 22 miliyoni, ndipo pofika m'chaka cha 2030 chifika pa 24 miliyoni. Pokwana chaka cha 2063 chiwerengero chi chidzafika 45 miliyoni. M'chaka chino cha 2025 chiwerengero cha amayi chili pa 51 mwa anthu 100 aliwonse (51 peresenti) m'Malawi. Poonjezera apo, anthu 51 mwa anthu 100 aliwonse (51 peresenti) m'Malawi ndi ana ochepera zaka 18. Izi zikusonyeza kuti achinyamata ndi ochuluka kwambiri. Komanso aMalawi ambiri amakhala m'madera a kumidzi, komabe pakhala kusintha kwakukulu chifukwa choti chiwerengero cha anthu okhala m'matauni chikukwera ndi 5 peresenti chaka chilichonse. Ndipo pakutha kwa chaka cha 2025, kakweredwe ka chiwerengero cha anthu okhala m'matauni kaposa kakweredwe ka chiwerengero cha anthu okhala kumidzi.

Kudzera mu manifesto yathu ya 2014 mpaka 2019, ife a DPP tinalonjeza kusintha Malawi, ndipo izi zinachitika, ndipo malonjezano ambiri anakwaniritsidwa. Ena mwa malonjezano amene tinakwaniritsa ndi awa:

- Palibe munthu amene anafa ndi njala, ngakhale kuti m'zaka zimenezi kunali chilala ndi kusefukira kwa madzi m'madera ambiri;
- Tinachepetsa chidaliro chathu pa mvula paulimi wathu ndi 13 peresenti, potsegula minda yokwana mahekitala 116,000 ku ulimi wa mthilira;
- Tinatsitsa kukwera kwa mitengo ya zinthu kuchokera pa 27 peresenti kufikira manambala osaposera 10 peresenti, pofika chaka cha 2020;
- Timakhala ndi ndalama zakunja zokwanira kugula katundu wakunja kwa miyezi isanu ndi umodzi, poyerekeza ndi ndalama zimene tinapeza mBoma m'chaka cha 2014, zomwe zinali zongokwanira kugula katundu kunja kwa mwezi umodzi wokha;

- Tinamanga makoleji 20 a zaumisiri ndi luso kumidzi, oti anyamata aziphunzirako ntchito zosiyanasiyana; ndipo m'chaka cha 2020 tinali okonzeka kuti timange makoleji ena 8;

M'zaka zimenezi, achinyamata oposa 6,000 anaphunzira za umisiri ndi maluso osiyanasiyana kudzera m'makoleji amenewa;

Achinyamata okwana 25,000 anali akuphunzira m'masukulu a ukachenjede a boma (Public Universities), poyekereza ndi achinyamata 10,000 okha amene anali m'sukuluzi m'chaka cha 2014 pamene timatenga boma.

Boma la DPP linapanga pologalamu yoti mabanja okwana 22,000 a anthu okalamba, ana amasiye, amayi amasiye, anthu achialubino, ndi anthu aumphawi kwambiri akhale ndi nyumba zokhalamo zabwino. Pologalamu imeneyi imatchedwa Decent and Affordable Housing Program (DAHP), ndipo imadziwika ngati Malata and Cement Subsidy programme.

Chuma cha dziko lino pansi pa ulamuliro wa boma la DPP chimakwera mothamanga kwambiri mu chigawo cha Kummwera kwa Africa (SADC).

Ndipo boma la DPP linakonza ndi kumanga miseu ikuluikulu m'dziko lino, monga miseu ya:

- Chikhwawa – Ngabu – Bangula
- Lilongwe West Bypass
- Zomba – Blantyre;
- Jenda – Edingeni;
- Milepa – Chiradzulu;
- Zomba – Jali – Phalombe – Chitakale;
- Thyolo – Thekerani – Muona – Makhanga;
- Liwonde – Mangochi;
- Lilongwe Old Airport – Kasiya – Kasungu;
- Mzuzu – Nkhatabay;
- Karonga – Songwe;
- Njakwa – Livingstonia;
- Thabwa – Chitseko – Seveni.

Poonjezera apa, boma la DPP linapeza ndalama zoti liyambe kukonza miseu iyi:

- Ndalama zochokera ku China (China Aid): Raundiabauti ya Mchinji mpaka ku Kanengo
- Ndalama zochokera ku European Investment Bank: Mseu wa M1 kuchokera ku Kanengo kupita ku Karonga
- Ndalama zochokera ku Japan (Japanese Aid): Mseu wa Kamuzu Procession

M'chaka cha 2018, Boma la DPP linapezanso ndalama zomangira sukulu 250 za sekondale, kuti konstichuwense iliyonse ikhale ndi sukulu ya sekondale. Nzomvetsa chisoni kuti boma la MCP lalephera kumanga sukulu za sekondale 151 mu pologalamu imeneyi; ndipo ndalama zotsalazo zinabwerera ku Amereka kumene zinachokera.

Kudzera mu pologalamu ya EQUALS ya World Bank tinamanga sukulu za sekondale 100 kumidzi.

Boma la DPP linakuza nyumba zophunzilira, miseu, zipangizo, ndi mapologalamu ena m'makoleji a sukulu za ukachenjede ndi cholinga chofuna kuonjezera ophunzira m'makolejimo. Makolejiwo anali a Chancellor College, Polytechnic, College of Medicine, Bunda College, Kamuzu College of Nursing, Natural Resources College, Mzuzu University ndi Malawi University of Science and Technology (MUST).

M'chaka cha 2019 Boma la DPP linapanga sukulu za ukachenjede zitatu kuchokera ku Yunivesite imodzi ya Malawi. Sukuluzi ndi University of Malawi (imene kale imatchedwa Chancellor College); Malawi University of Business and Applied Sciences (MUBAS), yomwe kale inali Polytechnic; ndi Kamuzu University of Health Sciences (KUHES), yomwe ndi

yophatikiza College of Medicine ndi Kamuzu College of Nursing. Kusintha uku kwapangitsa kuti chiwerengero cha ophunzira M'maYunivesitewo chikule, komanso kuti aphunzitsi achuluke. Ndondomeko ya Kota imene boma loyamba la MCP linakhazikitsa posankha ophunzira m'sekondale ndi Yunivesite m'chaka cha 1987, ife a DPP tinathetsa.

Boma lathu linakonza miseu yaikulu ndi yaing'ono m'mizinda yathu ya Mzuzu, Lilongwe, Zomba ndi Blantyre. Mwachitsanzo, tinakonza mseu wokhala ndi mbali ziwiri zopita kutsogolo ndi mbali ziwiri zopita kumbuyo mu mzinda wa Mzuzu. Tinakonzanso mseu wochokera pa raundiabauti ya pa Nyumba ya Malamulo kukafika ku Bingu National Stadium mu mzinda wa Lilongwe. Uwunso ndi mseu wokhala ndi mbali ziwiri zopita kutsogolo ndi mbali ziwiri zopita kumbuyo.Tinamanganso mseu woyenda galimoto ziwiri mbali iliyonse kuchokera pa Chileka raundiabauti kukafika ku Magalasi mumzinda wa Blantyre. Kudzera m'ndondomeko za Malawi Rural Electrification Program (MAREP) 8, tinapereka magetsi ku malo ochitirako malonda ndi midzi yokwana 473. Izi zinachitika koyamba mu mbiri ya dziko lino.

Boma linamanga labotare ya SQAM ndi maofesi ake ku Blantyre. Cholinga cha malo amenewa ndi kuonetsetsa kuti katundu wopangidwa m'Malawi muno ngakhale kunja aziyesedwako ndi kuonetsetsa kuti ndi wabwino, komanso wosapereka chiopsyezo kwa ogwiritsa ntchito, ndiponso wopangidwa motsatira ndondomeko zokhazikika. DPP inagwiritsa ntchito ndalama za misonkho ya a Malawi, osati ndalama zochokera kwa azungu pomanga malowa.

Mu ulamuliro wa DPP panali zopysinja chitukuko zingapo. Choyamba chinali kukwera kwa chiwerengero cha anthu. Chifukwa cha kuchulukana kunali kovuta kuti phindu limene limapezeka kuchokera muntchito zaboma lifikire aMalawi onse mokwanira. Komabe DPP igwiritsa ntchito kuchulukanaku ngati mwayi watsopano, popeza kuti chiwerengero cha achinyamata osapyola zaka 30 chili pa 70 peresenti ya chiwerengero cha Malawi. Gulu la achinyamata limeneli tidzaligwiritsa bwino ntchito kupanga zinthu ndi kugwira ntchito zimene zingatukule chuma cha dziko lino mofulumira.

Kuyambira m'chaka cha 2025 kufika 2030 boma la DPP lidzapitiriza ntchito za chitukuko kuchokera pomwe linasiyira. Tidzaonetsetsanso kuti ntchito zabwino zimene zinali mu dongosolo la chitukuko pa zaka zisanu zapitazi ziunikidwe bwino ndi kuzipitiliza. Boma lathu lidzapeza ndalama zogwirira ntchito zimenezi ndi kukwaniritsa maloto a aMalawi amene akuvutika kwambiri panthawi ino.

Tidzaonetsetsanso kuti tithane ndi vuto limene liri pakati pathu la kukwera kwa mitengo ya zinthu. Kuti zitheke padzafunika kusunga mwambo pa kayendetsedwe ka chuma. Masomphenya athu ndi oti kukwera kwa mitengo ya zinthu kusadzapyole 10 peresenti, ndipo chuma chathu chidzakhale chokwera ndi 6 peresenti pofika chaka cha 2030. Boma la DPP lakhala likuchita zimenezi, ndipo lichitanso zimenezi.

# 2 MALONJEZO



DPP ikalonjeza zinthu, imapanga zomwezo osati zinthu zosemphana ndi malonjezo. DPP imalonjeza zimene ingathe kuchita, ndipo imachita zimene yalonjeza. Ife a DPP ndi a chitukuko. Ife a DPP ndife okonda dziko lathu. Ife a DPP timagwira ntchito yotumikira aMalawi molimbika, modzipereka ndi modalirika. Ifeyo a Malawi mutidalirenso.

Pamene tikulowanso m'boma, tikhala tikudziwa kuti maiko akunja ndi mabungwe otithandiza akuchepetsa kapena kuchotsa kumene thandizo lao ku Malawi kuno. Ndipo ichi si chachilendo kwa ife, chifukwa pakati pa 2014 ndi 2020 tinayendetsa boma popanda ndalama za maiko ndi mabungwe akunja amene anachoka chifukwa cha kubedwa kwa ndalama m'boma lija limene tinaligonjetsa pachisankho. Koma ngakhale izi zinali choncho, maunduna, madipatimenti ndi mabungwe a boma amalandirabe ndalama zogwirira ntchito zawo mwezi ndi mwezi. Ife a DPP takonzeka kuyendetsa boma ndi ndalama zopeza tokha m'Malawi momwe muno. DPP idzaonetsetsa kuti tilime chakudya chokwanira kuti anthu adye ndi kugulitsa kunja. DPP imakhulupirira kuti chitukuko cha dziko sichingapite mtsogolo ngati anthu ena asiyidwa m'mbuyo.
Pachifukwa cha ichi, tidzakhala ndi chuma chofikira wina aliyense. Ife timakhulupirira mfundo yoti 'Malawi m'modzi, tsogolonso ndi limodzi', ndipo tiyenera kupita patsogolo limodzi monga dziko. DPP idzalimbikitsa chitukuko cha dziko lonse pochoka muumphawi ndi kulowa mu kutukuka.

DPP ndi chipani chotumikira wina aliyense. Pa maphunziro tidzaonetsetsa kuti ana onse, ngakhale awo amene ali ndi maulumali osiyanasiyana, akuphunzira mosasalidwa. Maphunziro amenewa adzakhalanso owathandiza kukhoza bwino, ndi kuwayenereza kugwira ntchito zosiyanasiyana.

Boma la DPP ndi limene linakhazikitsa bungwe lokonza mapulani a dziko (National Planning Commission). Tikalowanso m'boma tidzaonetsetsa kuti bungweli likupatsidwa thandizo loyenera kugwira ntchito zawo kuti likwaniritse zolinga zake. Mwachitsanzo, tidzaika chuma m'maphunziro poonetsetsa kuti sukulu za pulaimale zili ndi sukulu za sekondale pafupi, kuti tifikire mulingo woti ana onse oyenera kupita ku sekondale athe kutero. DPP idzapitiriza kutukula amayi pa bizinezi, utsogoleri, chitukuko ndi ntchito za chikhalidwe. Tidzaika ma pologalamu oti amayi ambiri apite ku Nyumba ya Malamulo ngati aphungu a dera lawo, kulowa nawo mu Kabineti, maofesi a boma ndi mbali zonse za chitukuko. DPP idzapitiriza kukweza achinyamata, kwenikweni powaphunzitsa umisiri ndi maluso osiyanasiyana m'makoleji a zaumisiri ndi maluso a kumidzi. Ife a DPP tidzateteza maufulu ndi zokhumba za anthu achikulire, amasiye ndi anthu ali ndi kuthekeka kosiyanasiyana. DPP idzapitiriza kuonetsetsa kuti Malawi ndi malo amene onse ofuna kuchita malonda, akazembe ndi mabungwe akunja akukhala motetezeka. Onsewa azidzapemphedwa kutenga nawo mbali pa ntchito za chitukuko muno m'Malawi. Boma lathu lidzayendetsa chuma molingana ndi nzeru ndi kafukufuku wokhuzana ndi za chuma amene akuchitika m'sukulu za ukachenjede, ndi mabungwe ena otero.

Tidzasamala chuma cha dziko lino modalirika ndiponso mokonda aMalawi. Kabineti yathu idzakhala yaing'ono ndiponso yoimilira magulu onse a anthu. Alembi a maunduna a boma adzakhala ochepa ndipo odziwa bwino ntchito zawo. DPP idzaunikanso ntchito za mabungwe a boma. Boma lathu lidzapitiriza mfundo zokhuza mgwirizano ndi maiko ena zimene zidzapangitse kuti dzikoli lipitirize kukhalabe loima palokha komanso lotukuka. A Malawi okhala kunja kwa dziko lino adzapatsidwa mwayi wotenga nawo mbali pa chitukuko cha dziko lino. Tidzakhazikitsa nthambi younikira m'mene boma lathu likutsatira mfundo za mu Manifesto yathu (Manifesto Monitoring and Evaluation Unit), ndipo izidzagwira ntchito ndi bungwe la National Planning Commission kuunikira m'mene boma likutsatira Manifesto imeneyi, kuchokera chaka chino cha 2025 kufikira chaka cha 2030.

3

# KAYENDETSEDWE KA CHUMA



Kuti Malawi 2063-MIP 1 ipambane zitengera kukhazikika kwa chuma cha dziko ndi kutengapo gawo lalikulu kwa makampani omwe siaboma pakayendetsedwe ka zachuma. M'zaka zinayi zapitazi chuma cha dziko lino chakhala chosakhazikika. Pakati pa 2021 ndi 2024 kukwera kwa mitengo ya zinthu kunafika pa 25 peresenti ndipo kenako kunakwera kufika pa 34.2 peresenti kumayambiliro kwa chaka cha 2025. Akatswiri a zachuma akuonanso kuti kukwera kwa mitengo ya zinthu kupitirira mpaka mwezi wa Ogasiti 2025. Ndondomeko yobwerekera ndalama ndi yokweranso kuchoka pa 12 peresenti mu 2020 kufika pa 26 peresenti mu 2025. Mu nkhokwe ya ndalama zakunja muli ndalama zochepetsetsa mu zaka khumi zonse zapitazi. Poonjezera apo, ngongole ya dziko ili pa 16 triliyoni, kuchokera pa 4 triliyoni yomwe Boma la DPP linasiya pochoka m'boma. Ngongoleyi yafika mlingo woti ntchito zaboma ngakhale ntchito za makampani a anthu wamba sizikuyenda bwino. Izi zafika apa chifukwa boma lakhala likubwereka ndalama m'mabanki mopyola muyeso, moti ngakhale makampani a anthu wamba sakupeza mwayi wa ngongole yokwanira ku mabankiwa. Chifukwa cha mavuto amenewa, chuma cha dziko lino sichikukula moyenera. Mwachitsanzo, kuchokera mu 2021 kufika mu 2024 chuma chathu chinakula ndi 1.0 peresenti yokha basi. Ndipo zoona zake nzakuti kukula kwa chuma cha dziko lino kunatsika ndi 1.8 peresenti m'chaka cha 2024.

Pofuna kuthana ndi mavuto a zachumawa, boma la DPP lidzagwira ntchito molimbika ndi kuchepetsa kukwera kwa mitengo ya zinthu kuti kusafike 10 peresenti pofika chaka cha 2027. Tikangopanga zimenezi, mudzaona kuti chuma chathu chayamba kukula, ndi kufika ngakhale pa 6 peresenti pakati pa chaka cha 2028 ndi 2030.

### 3.1 KUKHAZIKIKA KWA CHUMA

Boma la DPP lidzaika ndondomeko zothandizira kuti chuma cha dziko lathu chikhale chokhazikika. Ndondomekozi ndi monga izi: kupewa kusakaza chuma chaboma, kutolela misonkho ndi kugwiritsa ntchito kwake, kubweretsa ndalama zakunja, kusungidwe ka chuma, ndi kagwiritsidwe ntchito ka ngongole ya boma.

#### 3.1.1 KUPEWA KUSAKAZA CHUMA CHABOMA

Boma la DPP lidzaika m'malo ndondomeko za kayendetsedwe ka chuma kopanda kusakaza, ndinso kuti dziko lizisungako ndalama zambiri motere: Lidzasunga 500 biliyoni kwacha m'chaka cha 2026; 700 biliyoni kwacha m'chaka cha 2027, ndi 1.5 triliyoni kwacha pa chaka chilichonse kuyambira m'chaka cha 2028 kufikira chaka cha 2030. Mwapadera, boma la DPP lidzachita izi:

- Kusankha Kabineti yaing'ono komanso yoimirira magulu onse a anthu
- Kuchepetsa ndalama zomwe zimagwiritsidwa ntchito ku nyumba zaboma
- Kuimika kaye kugula kwa galimoto zatsopano za ogwira ntchito m'boma
- Kutsatira ndondomeko zogwiritsira ntchito ndalama zaboma za mu Integrated Financial Management Information System (IFMIS) kuti maunduna, nthambi ndi ma kampani a boma azigwiritsa ntchito ndalama zokhazo zimene apatsidwa popanda kusiyapo ngongole.
- Kuika ndondomeko yotchedwa Domestic Revenue Mobilization Strategy (DRMS) yomwe ntchito yake idzakhala kuonjezera ndalama zimene boma limatolera pa misonkho ndi 5 peresenti pa chuma chonse cha dziko (GDP) pokwana chaka cha 2030. Izi zidzachitika pokuza madera amene boma limatolerako ndalama, komanso poonetsetsa kuti anthu ndi mabizinezi ambiri akukhoma misonkho yosiyanasiyana, kusintha kaganizidwe ka anthu pankhani yokhuza misonkho, kulimbikitsa mabungwe aboma panjira zopezera ndalama, kubweretsa njira za makono mu ntchito


FEDERAL RESERVE NOTE
MG 13896379 A
KB 27320920 R
WE TRUST
ONE HUNDRED RAND

za MRA ndi kukonzanso ntchito zina zobweretsa ndalama m'dzikoli, pambali pa misonkho.

- Kuonetsetsa kuti ndalama zonse zaboma zikugwira ntchito moyenera, ndi kusachita ntchito zomwe sizili mu ndondomeko yogwiritsira ntchito chuma cha boma (bajeti)
- Kusintha pologalamu ya Agriculture Input Program (AIP) kuti izitha kuthandiza anthu bwino, chuma chisamasakazike, ndi kuti aliyense athe kukhala ndi chakudya chokwanira chaka chonse komanso kuti ulimi ukhale wopindulira anthu kwambiri.
- Kuunikanso malamulo ochotsa misonkho pagalimoto za ogwira ntchito m'boma, ndi kuchotsa malamulo amenewa pa galimoto zina.
- Kuonetsetsanso kuti mu makampani a boma muli kuchita zinthu poyera ndi mokhulupirika
- Kuchotsa mapulani oti makampani aboma awa apite ku Lilongwe: MACRA, MHC, MBC, Prison Services, NSO ndi ena otero.
- Kukonza kagwiridwe ntchito ka maofesi a boma ndi maofesi a ukazembe
- Kuunika ndi kuchepetsa ndalama zogwira ntchito ku Nyumba ya Malamulo

Tikadzachita izi tidzatha kupulumutsa ndalama zokwana 5.15 triliyoni. Ndalama tidzapulumutsezo zidzagwiritsidwa ntchito yoyamba kubweza ngongole zaboma, ngati njira imodzi yothandiza kuti chuma chathu chichoke kuphompho ndi kuyambanso kuyenda mu mseu woyenera. Ndalama zopulumutsidwazo zidzaikidwa m'mapologalamu oti zizipanga phindu mogwirizana ndi makampani amene si aboma, monga mmene imanenera Ndondomeko ya Malawi 2063-MIP-1.

### 3.1.2 NDALAMA ZA KUNJA ZOKHAZIKIKA

Mu boma la DPP, ndondomeko yosinthira ndalama zakunja idzakhala yokhazikika, komanso yodalirika. Pasanathe miyezi isanu ndi umodzi yakulowa m'boma, ife tidzachita izi:

- Kugwira ntchito ndi bungwe la IMF kuti tikhale ndi pologalamu yotipatsa thandizo (ECF Programme) yoyenera dziko lathu lino la Malawi;
- Kulowa pologalamu ya pakati pa 1.5 biliyoni ndi 2.0 biliyoni dola ya Amereka ndi mabungwe obwereketsa ndalama kuno kum'mwera kwa Africa ndi maiko ena, kuti tikhale ndi ndalama zokwanira za ma dola kunkhokwe yathu ya ndalama zakunja.
- Malamulo onse osakomera anthu omwe ali kunja kwa dziko lino, mabungwe omwe siaboma ndi maofesi a akazembe okhuza maakaunti a ndalama zakunja, tidzawachotsa ndi kuika malamulo okomera aliyense.
- Tidzachotsa lamulo lokakamiza kusintha kwa ndalama zochokera ku kunja

Ndi ndondomeko zimenezi dziko la Malawi lidzakhala ndi ndalama zakunja zokhazikika, ndipo msika wa ndalama zosintha kunja kwa mabanki udzachepa.

### 3.1.3 NDONDOMEKO ZACHUMA

DPP ikudziwa kuti chuma cha dziko lino sichikuyenda bwino, moti pamene tikuyandikira chisankho cha mu Sepitembala 2025 anthu ambiri akulephera kugula katundu amene akumufuna poyerekeza ndi zaka zisanu zapitazo. Tikudziwa kuti kusayenda bwino kwa chuma'ku kwapangitsa kuti ntchito zambiri zamalonda zisamayende bwino. Makampani ambiri omwe siaboma achotsa ntchito anthu ogwira ntchito, ndipo asiya kuika ndalama zokwanira m'mabizinezi'wo. Katundu wogulitsa kunja ndi wochepa, ndipo izi zapangitsa kuti dziko likhale lopanda ndalama zakunja zoyendetsera dziko. Kukwera kwa mitengo ya zinthu kwaposa 30 peresenti, komwe ndi kukwera kwambiri koposa miyeso ya zaka khumi zapitazo. Mwachidule, chuma cha dziko lino chili m'mavuto aakulu koopysa.

Popita mtsogolo, boma la DPP lidzabweretsa mfundo zapamwamba zoyendetsera chuma cha dziko lino kuti ntchito zobweretsa chuma chathu zitsitsimuke, ndi kubweretsa ntchito kwa anthu ambiri ndi kukhazikitsa mitengo ya zinthu. Choncho: Mfundo yoyendetsera ndalama (Monetary Policy) tidzaiika pa mulingo woti tithe kuthana ndi kukwera kwa mitengo ya zinthu m'dziko lino;

- Tidzatsitsa makulidwe a muyeso wa ndalama zotsekeredwa ku banki (Reserve Money growth) kuchokera pa 26 peresenti kufika pa 10 peresenti pofika chaka cha 2028.
- Tidzachepetsa ndalama zobwereketsa boma ku Bank Yaikulu (Reserve Bank) ndi kutsitsa muyeso wa ndalama zochedwa kusintha kuchoka pa 17.9 peresenti m'chaka cha 2025 kufika pa 10 peresenti m'chaka cha 2028.

### 3.1.4 NJIRA ZOYENDETSERA NGONGOLE

Malawi ndi wolemedwa ndi ngongole, ndipo chuma cha dziko lino chatsamwa. Pakutha pa chaka cha 2024 ngongole ya dziko inali pa 16.19 triliyoni (kuimira 86.4 peresenti ya chuma chonse cha dziko lino (GDP). Ngongole zambiri ndi zokhuza mapologalamu a boma ang'onoang'ono, ndipo pafupifupi 38.5 peresenti ya ngongoleyi iyenera kubwezedwa m'chaka chino cha 2025. Izi zikusonyeza kuti dzikoli likudalira ngongole zobweza pafupipafupi monga Treasury Bills ndi njira zina zimene Banki Yaikulu (Reserve Bank) imathandizira boma kuti lilipire katundu ndi ntchito zina za boma. Boma la DPP lidzasamala chuma mosiyana. Mwapadera, boma lathu lidzachita izi:

- Kuonetsetsa kuti ngongole zathu zikutsata ndondomeko zomwe boma lakhizikitsa lotchedwa Medium Term Debt Strategy.
- Kukambirananso ndi otibwereka ndalamazo kuti mabwezedwe a ngongoleyo asasokoneze kayendetsedwe ka chuma chathu.
- Kugwiritsa ntchito kwambiri ngongole zopanda chiongola dzanja chachikulu, zija amati Consessional loans mmalo



mongotenga ngongole zaku mabanki zokha.

- Kuima kaye kwa zaka ziwiri pa migwirizano ina ya ngongole zomwe boma limapereka chikole chake (Public and Publicly Guaranteed Loans) mpaka titaunikanso m'mene ndalamazi zagwiritsiridwa ntchito m'mbuyomo.
- Kumabwereka ndalama zokhazo zimene zingathandize kukweza chuma cha dziko lino podzera m'mafakitale ndi zina, m'malo mobwereka ndalama zomangodya.
- Kukonza njira ina yobwerekera ndalama yotchedwa Medium-Term Debt Strategy ya 2025-2030
- Kuonetsetsa kuti pakutha pa chaka cha 2026 boma lidzakhale litapulumutsa ndi kusunga ndalama zosachepera 270 biliyoni kwacha, imene ili 1 peresenti ya chuma chonse cha dziko (GDP).

### 3.2 THUMBA LA CHUMA

Boma la DPP lidzonetsetsa kuti likugwiritsa ntchito ndalama zimene lapeza, ndi kuchepetsa kubwerekabwereka ndalama, zimene zimasenzetsa mtolo mibadwo yamtsogolo ya a Malawi. N'chifukwa chake Manifesto yathu ikufotokoza zimene tidzachite ndi ndalama zomwe tizidzapeza. DPP ikuyerekeza kuti m'zaka zisanu zikubwerazi, boma lathu lidzakhala ndi ndalama zokwana 28.5 triliyoni. Tikuyerekeza kuti ndalama zopeza mom'muno m'Malawi zidzachuluka ndi 1.5 peresenti ya chuma cha dziko (GDP) pa chaka, kuyambira m'chaka cha 2025. Tikuyembekezanso kuti ndalama zongopatsidwa ndi maiko komanso mabungwe ena zitsika chifukwa cha kutopa kwa maiko ndi mabungwewo, ndi zina zimene zikuchitika padziko lapansi zimene zimakhuza chuma. Pofika chaka cha 2030 ndalama zopeza m'dziko mom'muno zidzakwera kuchokera pansi pa zilo nkufika 2 peresenti ya chuma cha dziko lathu (GDP).

### 3.3 KUKULITSA CHUMA CHATHU

Titakhazikitsa chuma m'malo mwake, boma la DPP lidzathandizira ntchito zikuluzikulu zomwe zaikidwa mu Ndondomeko ya Malawi 2063 makamaka MIP-1, m'mene tidzaika ndalama zokwana 6.35 triliyoni kuchokera mundalama zopeza tokha, kuti ntchitozo ziyambe kubweretsa ndalama zina. Ndalama zimenezi zidzapezeka potsatira mfundo zabwino zoyendetsera chuma. Ndipo ndalama zimenezi zidzaikidwa mu mapologalamu a ntchito zazikuluzikulu. Tidzabwereka ndalama mosamala ndi cholinga choti tizidzatha kubweza ngongoleyo mosavuta, ndi kupewa kutenga ngongole pamene sitinabweze ngongole ina. Choncho boma la DPP lidzaonetsetsa kuti ndalama zathu zopeza mom'muno zikutsala mubanki muyeso wabwino, monga 1 peresenti kuyambira m'chaka cha 2028 kufika 2030.

Madera a zachuma amene tidzatsindikikiza kwambiri kuti chuma chikwere adzakhala awa:

- Kupanga magetsi
- Migodi
- Njanje, miseu, malo omangako mafakitale, malo okonzerako katundu ogulitsa kunja, mabwalo a ndege, madoko, ndi njira zopitira kunyanja yaikulu ya Malawi.
- Ulimi wochita mwa bizinezi kudzera mu thonje, soya, tirigu wokonza bwino ndi chimanga choti a Malawi akhale ndi chakudya chokwanira.
- Kugula katundu wakunja mwadongosolo.
- Kupanga katundu wogulitsa kunja amene maiko ena a dera lino la SADC sangamupange.

### 3.4 KUGWIRITSA BWINO NTCHITO MISIKA YA NDALAMA

Boma la DPP lidzagwiritsa ntchito ndalama zambiri zimene zimachokera kwa anthu opuma pantchito ndi Inshuransi, nkuika ndalamazi m'mapologalamu ndi ntchito zimene zimachulukitsa chuma cha dziko.



4

# NSANAMIRA ZA CHITUKUKO

## NSANAMIRA ZA CHITUKUKO

Potsogozedwa ndi Ndondomeko ya Malawi 2063 boma la DPP lidzakhazikika pa msanamira za chitukuko zinayi izi: Ulimi waphindu ndi wa bizinezi, Chitukuko cha mafakitale, Chitukuko cha m'matauni ndi Kupereka mphamvu kwa anthu.

### 4.1 ULIMI WOCHITA MWA BIZINEZI

Chuma cha Malawi chimadalira kwambiri ulimi, moti ulimi wabweretsa 30 peresenti ya chuma cha dziko (GDP) mu zaka khumi zimene zapitazi. Koma ulimi wathu umachitika ndi alimi ang'onoang'ono ndipo 80 peresenti ya anthu a m'dziko muno amagwira ntchito mu gawo limeneli la chitukuko. Koma ulimi uwu umakumana ndi mavuto ambiri monga kuchepa kwa mitundu ya mbeu, kudalira alimi ang'onoang'ono ndi kudalira kwambiri chimanga.

Boma linakhazikitsa ulimi wa chimanga monga ndondomeko ya boma ngakhale kuti mbeu zina monga chinangwa, mpunga, mbatata ya kholowa, mapira, nthochi, ndi kachewere zimachitanso bwino. Mbeu yaikulu yogulitsa kunja ndi fodya, imene imapyola 40 peresenti ya mbeu zogulitsa kunja. Zina ndi tiyi, shuga, nyemba ndi nandolo, komanso thonje ndi mtedza.

Boma la DPP lidzadzipereka kukweza ulimi m'Malawi muno kudzera mu kuchulukitsa kwa zokolora, kukhazikitsa ndondomeko zoti ulimi ndi malonda okhuza ulimi zikuchita bwino. Choncho tidzaonetsetsa kuti ntchito zachuma zikuchitika mwadongosolo, komanso kuonetsetsa kuti chakudya chikhalepo chokwanira kwa a Malawi, ndi kutinso ntchito za ulimi zizikula ndi kukhazikika. Izi zidzapangitsa kuti ulimi uzibweretsa ndalama zambiri m'dziko muno.

Boma la DPP lidzakweza ntchito za ulimi ndi kugwiritsa ntchito mfundo za sayansi mu ulimi (greenhouse agriculture), ndi ulimi wobweretsa ndalama zambiri kudzera mu ulimi wa ziweto, nsomba, zipatso ndi mtedza. Tidzabweretsa kubiriwira kosintha zinthu (Green Revolution).

Pofuna kukwaniritsa ndondomeko imeneyi boma la DPP lidzachita izi:

- Kulima kwa mitundu yosiyanasiyana ya mbeu zimene zimabweretsa ndalama zambiri, komanso kukwanira kwa chakudya kwa aliyense. Mwa ichi tidzalimbikitsa kubzyala mbeu zapamwamba m'madera omwe mbeuzo zimachita bwino m'dziko muno, ndikugwiritsa njira zaulimi zosiyanasiyana. Mwachitsanzo, tidzalimbikitsa kuti kuchigwa cha mtsinje wa Shire anthu azilima mbeu zokonzedwa bwino za mapira, mawere, ndi mbeu zina zosaona chilala. Tidzalimbikitsanso ulimi wogwiritsa ntchito zinthu zachilengedwe (Conservation agriculture). M'mbali mwa Nyanja ya Malawi, pakati ndi kumtundu kwa mtsinje wa Shire, tidzalimbikitsa kulima mbeu zosaona chilala, mbeu ya mavitamini ya chimanga, mbeu yapamwamba ya mpunga, mbeu ya mbatata yoonjezeredwa mphamvu, mwa zina. Pambali pa izi, anthu azidzalimanso mbeu za chimanga, chinangwa, nandolo ndi nyemba mwa kasakaniza ndi mtedza kapena nandolo.
- Tidzadzutsa gawo lophunzitsa alimi kalimidwe kosiyanasiyana (Extension system). Tidzalemba ntchito akatswiri ambiri kuti azigwira ntchito ndi alimi pa boma komanso EPA iliyonse.
- Tidzadzutsanso malo otchedwa Land Husbandry Training Centre ndi kudzutsanso malo ena omwe ophunzira za kasamalidwe ka nthaka oyendera ndi ogona komweko azikaphunzirako. Tidzatsegulanso ma ofesi ndi nyumba zogonamo ogwira ntchito onse a m'ma EPA.
- Tidzaphunzitsa ogwira ntchito zophunzitsa alimi pafupipafupi, kuti akathe kuphunzitsa alimi nzeru zatsopano

za ulimi;

- Tidzalimbikitsa kafukufuku wokhuzana ndi ulimi kuti alimi athu ayambe kugwiritsa ntchito njira zamakono zochitira ulimi wa mbeu ndi wansomba;
- Tidzaunikanso ndondomeko ya maphunziro a alimi (Extension Policy);
- Tidzaonjezera ndalama zopita ku ulimi ndi zipangizo zothirira mbeu, ndipo tidzaonjezeranso minda imene mumachitika ulimi wa bizinezi kuchokera pa 20 peresenti kufika pa 40 peresenti pofika chaka cha 2030.
- Tidzaonetsetsanso kuti alimi a mitundu ndi magulu onse akupeza mbeu yapamwamba ndi zina zofunikira paulimi munthawi yake;
- Tidzakonza dongosolo labwino lothandizira kuti alimi asamagule pa mitengo yokwera mbeu ndi zipangizo zofunikira pantchito yao.
- Tidzakhazikitsa fakitale yopanga fetereza m'Malawi mom'muno kuti mtengo wa fetereza utsike.
- Tidzaunikanso ndi kukonza dongosolo la Farm Inputs Subsidy Programme (FISP) yothandizira alimi ang'onoang'ono okhala m'makalabu odalirika
- Tidzakhazikitsa mabungwe obwereketsa ngongole kwa alimi okhala m'magulu (Cooperatives); ndi kuonetsetsanso kuti alimi akuluakulu ndi eni minda ikuluikulu (maesiteti) akupeza mwayi wangongole ku mabanki;
- Tidzaika ndondomeko zoonetsetsa kuti alimi akupeza mbeu ndi zipangizo za ulimi pamtengo wabwino, komanso mosavuta.
- Tidzapereka chiongola dzanja kwa alimi amene adzapanga chisankho cholima mbeu zomwe sizilimidwa wamba mMalawi muno koma zili ndi kuthekeka kobweretsa ndalama zambiri m'dziko muno, monga chamba chogwiritsa ntchito m'mafakitale, maluwa, zipatso, mpunga ndi tirigu, mtedza, thonje, makadamiya ndi ziweto, monga zimene afotokoza mu National Export Strategy II.
- Tidzapititsa mtsogolo ulimi wamthirira kuti tichepetse





khalidwe lodalira ulimi wamvula wokha. Izi tidzachita pophatikiza ndalama zochokera ku maiko ena ndi ndalama zochokera mthumba la boma. Tidzaika ngongole zoti alimi akuluakulu ndi eni maesteti azitha kupeza mosavuta. Mwa ichi boma la DPP lidzaonjezera minda ya ulimi wa mthirira kuchokera mahikitare 116,000 m'chaka cha 2025 kufika mahikitare 147,000 m'chaka cha 2030.

- Tidzakhazikitsa minda iwiri yachitsanzo ya boma. Munda uliwonse udzakhala waukulu ma hekitare 12,500. Pa mahekitare onse 25,000 amenewa, mbeu zothandizira kuchotsa njala zidzalimidwa pa mahekitare 16,000 ndipo zolima zina zobweretsa chuma chambiri zidzalimidwa pa mahekitare 9,000.
- Tidzakopa makampani osakhala aboma kulima mbeu zogulitsa pa mahekitare 60,000 pofika chaka cha 2030.
- Tidzakonzanso bungwe la ADMARC kuti lizigwira ntchito zake bwino m'Malawi muno komanso kukhala ndi misika ya kunja kwa dziko lino.
- Tidzadzutsa msika wa Commodity Exchange kuti ntchito zake zikhale zapamwamba polingalira kaso la katundu, magwiridwe a ntchito ndi kupereka malipiro.
- Tidzaonetsetsa kuti nkhokwe zathu zosungiramo chimanga zikusunga chimanga chosachepera ma tani 150,000 nthawi zonse.
- Tidzalimbikitsa kafukufuku ndi ntchito za ulimi wogwirizana ndi kusintha kwa nyengo.
- DPP ikudziwa kuti ulimi wogwiritsa ntchito makina ndi zipangizo zamakono sukugwiritsidwa ntchito mokwanira, osati chifukwa choti alimi sakufuna kutero ayi, koma kuti zili dele chifukwa choti makinawa ngochepa, komanso kuti ndi okwera mtengo moti alimi ambiri sangakwanitse kuwagula. Choncho boma lathu lionetsetsa kuti zipangizo zaulimi zimenezi zikupezeka mosavuta.
- Tidzakonza dongosolo lokopa a malonda kuti azitha kuitanitsa zipangizo zamakono za ulimi mosavuta, monga zipangizo zolimira minda, kuthirira, kulimbana ndi udzu, mayendedwe, kuthana ndi tizilombo ndi matenda a m'munda, kukolora ndi kusamala zokolora. Nthawi yomweyo, boma la DPP lidzakonza ndondomeko zoti tizitha kupanga zipangizo zaulimi zotchipa ndi zoyenera alimi ang'onoang'ono kudzera mu PPP.
- Tidzalimbikitsa ndi kuthandizira kukhazikitsidwa kwa minda yoti alimi azikaphunzirako kalimidwe kabwino (Anchor Farms), ndi kukhazikitsa nkhokwe zachimanga za m'magulu pamudzi uliwonse.
- Tidzaonjezera misika yogulitsako zokolola zapadera zimene zimabweretsa ndalama zambiri m'dziko pochita izi:
- Kukhazikitsa misika yatsopano
- Kukonza misika imene ilipo kuti izitha kulandira zokolola zambiri komanso kufikira madera ambiri; kukuza malo osungira zokolora, ndi kuonetsetsa kuti pali kulumikizana kwabwino pakati pa onse okhuzidwa ndi ntchitozi, ndi zina zotero.
- Kulima kwa kontirakiti, ma sikimu a anthu olima malo ena ndi njira zina zogwirizana ndi machitidwe a malonda a zaulimi
- Tidzalimbikitsa ulimi wansomba pakati pa alimi a minda ing'onoing'ono, minda yokulirapo ndi alimi a maesiteti pomanga madamu m'madera a kumidzi, komanso kuonetsetsa kuti zakudya zansomba zikupezeka;
- Tidzaonjezera ulimi wa ziweto popanga zina mwa izi:
- Kulimbikitsa anthu a kumidzi kutengapo mbali mu ulimi wa ziweto;
- Kuika ndondomeko zoti alimi azichita ulimi wa ziweto zopatsirana monga ngombe, mbuzi, nkhosa ndi nkhuku m'minda ya boma
- Kugwiritsa ntchito makina amakono pochulukitsa ziweto ndi kukonza zonse zochokera mu ziweto zisanagulitsidwe
- Kukhazikitsa zipangizo kapena makina okonzera mkaka ndi zina zochokera ku zoweta tisanazitengere kumsika

## 4.2 NTCHITO ZA MAFAKITARE

DPP ikukhulupirira kuti kukolola mbeu simapeto a zonse. Tikukhulupirira kuti kukhala ndi mafakitale amphamvu ndi kulumikizana ndi ena pakutukula chuma, ndi chinthu chofunikira kwambiri. Pachifukwa ichi DPP idzaika patsogolo ndi kuthandizira makampani omwe siaboma kuti akhale maziko a chuma cha dziko, kupezeka kwa ndalama zakunja ndi kubweretsa ntchito m'dziko muno. Boma la DPP lidzaika patsogolo ntchito za mafakitale zisanu ndi imodzi m'mene dziko la Malawi limachita bwino poyerekeza ndi maiko ena. Izi ndi monga; mafakitale a zinthu zochokera mu ulimi, mafakitale a zovala, mafakitale okonza miyala ya migodi, mankhwala a mzipatala, zamagetsi ochokera ku zachilengedwe ndi zamakina. Mbali iliyonse yamafakitale idzakhazikitsidwa kudzera mu Special Economic Zones (SEZs) kumene kumakhala njira zamtengatenga zapamwamba, mphamvu zamagetsi odalirika, ndi kayendetsedwe ka mabizinezi kabwino.

Tidzaika malo muzigawo okonzerako mbeu ngati soya, tirigu, mpunga, tiyi, ethanol, nsomba, nyama, zipatso ndi ndiwo zamasamba ndi makadamiya kuti zikhale muyeso wotumiza kunja kwa dziko lino. Mafakitale a zovala adzayambitsidwanso kudzera mu mafakitale otchedwa Cotton-to garment production parks, potero achinyamata ambiri adzapeza ntchito. Ndondomeko yathu ya migodi (Mineral beneficiation policy) idzaletsa kutumiza kunja miyala ya graphite ndi miyala ina yosowa ndi yamtengo wake (rare earths), ndi choling choti Malawi azipeza phindu lalikulu pa chuma chake chachilengedwe.

Mafakitale a mu zigawo'wa adzayendetsedwa potsatira mfundo zisanu za SEZ. Lilongwe lidzakhala likulu la mafakitare a zinthu zochokera mu ulimi; Blantyre idzakhala likulu la mafakitale a zovala ndi zinthu zina zapamwamba. Mzuzu idzakhala likulu la mafakitale a za mitengo, miyala ya migodi ndi mphamvu zamagetsi ndi makompyuta. Mangochi idzakhala



likulu la mafakitale a nsomba ndi zokopa alendo. Ndipo Karonga idzakhala likulu la malonda a migodi ndi mtengatenga ndi ntokoma. Malo amenewa (SEZ) azidzapereka nthawi yopuma pa misonkho (tax holidays) kwa omwe aika ndalama zawo m'ntchito zimenezi, kusalipira msonkho pa katundu wakunja wokhuzana ndi ntchito zimenezi ndi kupatsidwa mwayi woyamba wogwiritsa ntchito minda. 30 peresenti ya malo amenewa idzaperekedwa kwa achinyamata amene akutenga nawo mbali m'ntchito zimenezi. Poonjezera apo oyambitsa ntchitozi adzapatsidwa nthawi yogwira ntchito m'malowa osalipira malipiro a pamalo (renti). Malo onse asanu adzakhala ndi sukulu yake ya pamwamba yophunzitsirapo achinyamata maluso oyenerera bizineziyo.

DPP idzaika m'malo ndondomeko zamakono za mgwirizano zoti zitukule nsanamira ndi mafakitale a SEZ. Mgwirizano umenewu udzakhala woti Boma lidzapereka malo ogwirira ntchito; pomwe makampani omwe siaboma adzaika ndalama ndi maluso awo mu pologalamuyi. Kudzera mu dongosolo loti mwini ndalama amange fakitale, ndikuigwiritsa ntchito kwa kanthawi kenako ndikuipereka ku boma (Build-Operate-Transfer), makampani omwe siaboma adzamanga malo obweretsa magetsi, miseu, ndi malo osungiramo madzi ndi kugwiritsa zinthuzi kwa kanthawi kochita kugwirizana, kenako nkuzipereka kwa anthu/boma. Ma tenanti akuluakulu m'malo athu a SEZ adzapatsidwa zinthu zowakopa kuti agwire ntchito m'malowa, ndipo tidzawalimbikitsa kulemba ntchito achinyamata ndi kugwiritsa ntchito ma banki a m'Malawi mom'muno. Mgwirizano uliwonse udzakhazikika pa mfundo za kuchita zinthu poyera ndinso kupereka malipoti ku boma mu nthawi yake kudzera pa kompyuta pa malo otchedwa SEZ Transparency Portal.

Pozindikira kuthekera kumene kulipo kwa a Malawi okhala kunja kwa dziko lino, DPP idzakhazikitsa pologalamu yokambitsana ndi anthu okhala kunja kwa dziko lino. Tidzalola a Malawi okhala



kunja kuika ndalama zawo, pa chiongola dzanja chabwino, m'mabizinezi a SEZ kudzera mndondomeko yatsopano ya Malawi Growth Programme. Padzakhalanso ndondomeko ina yotchedwa Expert Return imene idzabweretsa a Malawi akunjawa m'dziko muno kudzaphunzitsa aMalawi maluso osiyanasiyana kwa kanthawi kochepa asanabwerere kunja. Awo amene adzaphunzitse anthu maluso awo sitidzawadula misonkho pa malipiro awo ophunzitsira aMalawi. Ku Malawi Investment and Trade Centre (MITC) kudzakhala ofesi/desiki yothandizira kulembetsa mabizinezi ndi ntchito zina mofulumira. Chaka chilichonse padzakhala nthumwi zolumikizitsa a Malawi akunja ndi a Malawi a m'dziko muno pankhani za kuika ndalama m'malonda.

Pofika chaka cha 2030 ndondomeko ya mafakitale ya DPP idzabweretsa zipatso zolozeka, monga; kubweretsa kwa ntchito zam'mafakitale mokondera achinyamata ndi 70 peresenti; kuchuluka kwa katundu wopangidwa mmafakitale wotumizidwa kunja, kuchepa kwa katundu wogulitsidwa kunja asanaonjezeredwe maonekedwe. Izi zidzachitika chifukwa choti tidzapititsa patsogolo ntchito zokonza katunduyo asanatumizidwe kunja.

### 4.2.1 NTCHITO ZA MIGODI

Bukhu la Malawi 2063 linatsindika kuti migodi ndi mbali imodzi ya chuma cha dziko lino limene lingathandize kupititsa mtsogolo chitukuko cha mafakitale m'dziko muno. Pdakali pano migodi ikubweretsa chuma chochepa cha 1 peresenti mu chuma cha dziko lonse (GDP), koma migodiyi itatukulidwa ikhoza kumabweretsa chuma chofika 20 peresenti pa GDP. Zinthu zikuluzikulu zimene zikulepheretsa kukula kwa ntchito za migodi ndi izi: kafukufuku wosakwanira, zipangizo zosakwanira pa malo oyesera miyala (labotare), zipangizo zosakwanira zounikira ntchito za migodi, kuchepa kwa mauthenga kwa anthu, kuchepa kwa maluso pakati pa a Malawi, kusakhala ndi malo m'maboma ndi m'malire a dziko lino owona za migodi, ndi kuchepa kwa maluso opangira migwirizano kapena makontarakiti ndi makampani omwe ali ndi chidwi mu ntchito za migodi m'Malawi muno.

Komabe ubwino umene ulipo ndi woti ndondomeko zoyendetsera migodi, zimenenso ndi zovomerezeka ndi Malamulo a dziko lino zilipo m'Malawi muno. Izi ndi monga Mines and Minerals Act, Artisanal and small scale mining policy. Kudzera mu Manifesto iyi, boma la DPP lidzachita izi:

- Kuchita kalondolondo wa miyala yapamwamba ndi yofunikira yonse (Onani tebulo yoyambayo) pansi pa kampani yaboma yotchedwa Malawi Mining Company (MAMICO). Miyala yotere ndi iyi: 1) Miyala ya zitsulo zosowa (rare earth metals) monga tantalum, zircon, niobium zimene zimapezeka m'mapiri a Kanyika ku Mzimba, m'mapiri a Songwe, ku Phalombe, Makanjira ku Mangochi, ku Kanga Nkude ku Balaka
- Migodi ya grafaiti ku Malingude m'boma la Lilongwe ndi ku Ilomba ku Chitipa
- Miyala ya rube ku Chimwazulu ku Ntcheu
- Bokosaiti ku Mulanje
- Malasha ku Karonga ndi malo ena ambiri, zomwe zikusonyeza kuti dzikoli liri ndi malasha ambiri
- Rutile yemwe akupezeka ku Kasiya ku Lilongwe
- Kuchita kafukufuku kawirikawiri wa miyala yosowayi, ndi miyala ina ya mtengo wake.
- Kuika mfundo ndi ndondomeko zoyendetsera migodi ndi kuonetsetsa kuti pali maluso othandizira kuti ntchito za migodi ziziyenda bwino. Miyala imeneyi izidzakonzedwa bwino isanagulitsidwe kunja kuti izikhala ndi mtengo wa pamwamba, komanso m'malo motumiza kunja tizitha kupanga zitsulo zina mom'muno mMalawi (steel manufacturing).
- Kuonetsetsa kuti tili ndi mapu oonetsera malo amene muli miyala ya migodi ndi kukhazikitsamo migodi kudzera mu mgwirizano wochita ndi makampani a anthu omwe siaboma

(PPP). Kukonza miyala isanagulitsidwe kunja kudzathandiza kuti a Malawi, kwenikweni achinyamata adzapeze ntchito zambiri ndi kuphunzira maluso a ntchitozi.

- Kuonetsetsa kuti dziko likuphika mphamvu za magetsi okwanira kuti ntchito za migodiyi zikhale zosavuta, komanso kuti eni makampani ya migodiyi adzaloledwa kupanga mphamvu ya magetsi yogwiritsa ntchito pa migodiyo.
- Kulimbikitsa makampani kupanga zipangizo za migodi ndi katundu wina wogwiritsa ntchito m'malabotale, fakitale ndi mminda ikuluikulu.
- Anthu a zaluso ndi alimi ang'onoang'ono adzavomeredwa ndi boma ndi kuwalumikizitsa ndi makampani amene angawathandize kutukula ntchito zawo za migodi.
- Powathandizira kuti ntchito zawo ziziyenda bwino ndi kukhala zokhazikika, boma lathu lidzaika ndondomeko zabwino zokhuzana ndi umoyo wa ogwira ntchito, kusamala zinthu za chilengedwe mderalo, ndi kusaika miyoyo ya ogwira ntchito pa chiopsezo
- Kuthandizira kupeza misika ya miyala ndi zina zochokera mu mafakitale amenewa.
- Kuonetsetsa kuti katundu wa m'mafakitale amenewa akukonzedwa bwino kuti azikabweretsa ndalama zambiri pamsika.
- Kuika ndalama zoyambira kampani ya Malawi Mining Investment Company (MAMICO) zosachepera 500 biliyoni kwacha ndi cholinga chofuna kutukula chuma cha m'migodi. Izi zidzathandizanso kuti boma lidzathe kuyendetsa bwino kagawidwe ka ntchito za migodi kwa makampani osiyanasiyana, ndikupeza phindu la ndalama zochuluka kudzera m'migodi.

### 4.2.2 NTCHITO ZA MTENGATENGA

DPP ikudziwa kuti njira imodzi yofunikira yotsegulira misika ya malonda a kumidzi ndi kubweretsa chitukuko chamatauni, ndi kukhala ndi mayendedwe abwino panseu, panjanje, pandege ndi pamadzi. Njira za mtengatenga izi zidzathandiza kutsekula madera onse a kumidzi ndi kutsegula dziko lathu ku misika ya maiko ena, ngakhale kuti sitiri pafupi ndi Nyanja yaikulu. Pakudalira miseu yokha pamalonda, dziko lino limalipira ndalama zambiri pantchito zamtengatenga, komanso ntchito zambiri zimachedwa. Boma la DPP lidzagwiritsa ntchito ndondomeko kapena pulani yokhuzana ndi zamtengatenga yotchewa National Transport Master Plan, imene DPP inakonza ndi kukhazikitsa. Boma la DPP lidzachita zotheka kuti pakhale kulumikizana kwa njira za mtengatenga, pakhale kuchepa kwa ndalama zolipira mayendedwe, ndi kuchita malonda mwampikisano wabwino, podzera mu izi:

***Kulumikiza doko la Nacala ndi doko la Beira***

Madoko a Beira ndi Nacala m'dziko la Mozambiki adakalibe njira zodalilika zomwe dziko la Malawi limafikira kunyanja yaikulu. Pofuna kutsindika njira zimenezi boma la DPP lidzachita zinthu izi:

- Kuika ndalama mu ntchito zokonza ndi kukuza njanje ya Liwonde mpaka ku Nacala ndi cholinga chokonza mayendedwe ofikira ku Nyanja yaikuluyi
- Kukhazikitsa doko lopanda madzi (dry port) pa Liwonde ndi lina ku Blantyre kumene ntchito za kasitomu zizidzachitika pa katundu wopita kapena wobwera ku Beira kapena ku Nacala
- Kupitiriza ntchito yokonza doko lamkati mwa dzikoli, ku Nsanje kudzera mu zokambirana ndi anthu ndi magulu oyenera kuti ntchitoyi itheke, poyang'ana zinthu zimene zinali zotchinga. Loto la doko la Nsanje lidakalipobe m'boma la DPP.

***Kuika sitima ya panyanja yolumikiza Quelimane ndi Beira***

Doko la Kilimane lili ndi kuthekeka kothandiza Malawi kufukira doko lalikulu la Beira. Chifukwa cha ichi, boma la DPP lidzachita izi:

- Kukhazikitsa mgwirizano pakati pa boma la Mozambiki ndi


302

Malawi woika masitima ang'ongonoang'ono oti aziyenda pakati pa Kilimane ndi Beira, komanso Nacala
- Kuika mseu wabwino pakati pa Kilimane ndi Blantyre umene ungadzakhale nseu wina ndiponso wachidule polowetsa ndi kutulutsa katundu kunja kwa dziko lino.

***Kukonzanso Njira za njanje***

Ntchito yokonza miseu ya Nacala ndi Sena idzakhala pa ndandanda wa ntchito zofunika kwambiri kuti dziko la Malawi lilumikizidwe ndi malile a Mozambiki panyanja yaikulu

- Tidzalimbikitsa njira za njanje zochokera ku Blantyre ndi Lilongwe ndi njanje zina zoyandikana nazo
- Tidzalimbikitsa mgwirizano wa pakati pa boma ndi mabungwe omwe siaboma kudzera mu ndondomeko ya Public Private Partnership (PPP) ndi cholinga choti ndalama zogwirira ntchitozi zikhale zopezeka ndi kukwanira nthawi zonse
- Tidzamanga njanje kuchokera ku Tazara kufika pa doko la Chilumba pa Nyanja ya Malawi

***Mayendedwe a panjanje***

- Tidzalingalira mapulani oika sitima ya pamtunda yokwera anthu yoyenda molingana ndi nseu waukulu wa M1 kuchokera ku Blantyre mpaka ku Lilongwe
- Tidzaikanso sitima (kochi) yokwera anthu, yoyenda pa njanje imene ilipo kale pakati pa Nsanje mpaka ku Mchinji kudzera ku Liwonde, Salima ndi Lilongwe

***Mayendedwe a panyanja***

- Kukhazikitsa kulumikiza kwa mayendedwe a pamadzi mkati mwa dziko lino, monga kulumikiza Makanjira, Monkeybay, Chipoka, Nkhatabay, Likoma, Chizumulu ndi Chilumba
- Kuika sitima zonyamula katundu ndi kukonzanso madoko ake panyanja ya Malawi ndi pa chilumba cha Likoma
- Kulimbikitsa makampani omwe siaboma kutenga nawo gawo pa ntchito za mtengatenga wa panjanje kapena pamseu
- Kukhazikitsa mayendedwe abwino kuchokera ku Dar es Salaam ndi Mbambabay ndi Chilumba mpaka Nkhatabay, njira ija imene imatchedwa Mtwara Transport Corridor.

***Mayendedwe a m'mlengalenga***

- Tidzaonetsetsa kuti Malawi akhale dziko limene anthu oyenda pa ndege adzafuna kufikako, ndipo tidzachita zoti makampani ambiri a ndege azigwiritsa ntchito mabwalo athu a ndege
- Tidzakuza mabwalo a ndege a Chileka ndi Kamuzu ndi kuika miyeso yoyenera pa dziko lapansi (international standards)
- Tidzakhazikitsa mzinda pa bwalo la ndege liri lonse (Airport City)
- Tidzamanga bwalo lina la ndege ku Mzuzu, ndi kukonza bwino mabwalo a ndege a Karonga, Mangochi ndi Salima

***Mayendedwe a panseu***

- Tidzaonjezera ntchito zokonza miseu
- Tidzapereka mphamvu kwa anthu a m'maboma ndi m'zigawo kuti aziyendetsa ntchito za malo otolera misonkho ya panseu (Tollgates)
- Tidzaonetsetsa kuti udindo wokonza miseu ya m'maboma ili m'manja mwa khonsolo ya pa boma poonjezera ndalama zimene zimapita ku bomalo kudzera mu Constituency Development Fund (CDF)
- Tidzalimbikitsa njira za kaphatikiza pakagwiritsidwe ntchito ka miseu, njanje ndi mayendedwe a pamadzi
- Tidzakonza ntchito za mmalo otulukira ndi kulowera mdziko lino kuti ntchito za malo amenewa zizichitika mofulumira

Boma la DPP lidzamanga miseu yolumikizana monga iyi:

- Mangochi-Makanjira
- Rumphi-Nyika-Nthalire-Chitipa
- Likuni-Malingunde-Chileka
- Dzaleka-Ntchisi-Mpalo-Malomo

- Tsangano-Neno-Mwanza
- Chitipa-Mbilima
- Nsanama-Nayuchi
- Lirangwe-Namatunu-Chingale-Machinga
- Rumphi-Nyika Turnoff-Hewe
- Thyolo-Khonjeni Luchenza
- Salima-Nkhotakota Lakeshore
- Mzimba-Ezondweni-Njakwa
- Thabwa-Mkhate-Fatima East Bank
- Zomba-Liwonde
- Salima-Mangochi
- Balaka - Chilipa -Mangochi
- Golomoti - Monkeybay Turnoff
- Chikwawa - Thyolo - Mulanje

Boma la DPP lidzamanganso miseu yodzera kuseli kwatauni (bypass) monga iyi:

- Mzuzu West Bypass
- Lilongwe Eastern Bypass
- Blantyre Ring Bypass

***Malo amodzi ochitirapo zinthu zambiri mmalo olowera ndi kutulukira m'dziko lino***

Titatha kumanga malo amodzi ochitirapo zinthu zambiri m'malo otulukira ndi kulowera pa Mchinji-Mwami, Mwanza-Zobue ndi Dedza-Calomue, boma la DPP lidzamanga malo ngati omwewa pa Songwe-Kasumulu, Muloza-Milanje ndi Chiponde-Mandimba.

***Kukonza miseu ya mkati mwa mizinda***

DPP idzakonza miseu ya mkati mwa mizinda yathu yonse kudzera mu pologalamu ya City Roads Modernization m'mizinda ya Mzuzu, Lilongwe, Zomba ndi Blantyre. Poonjezera apa, boma la DPP lidzapitiriza kuika milatho ya m'mwamba ndi miseu yomangidwa pamwamba pa miseu ina kuti vuto la kuthinana kwa magalimoto pa miseu ya m'tauni ndi m'mizinda, lichepe kapena kutheratu. Komanso boma lathu lidzakonza malo onse mokwerera mabasi m'mizinda yonse inayi ndi m'matauni athu awiri.



***Miseu ya kumudzi***

Boma la DPP lidzapitiriza kumanga miseu m'madera a kumudzi n'cholinga choti alimi azitha kutengera mbeu zawo ku misika ya m'tauni mosavuta ndi mofulumira.

***Ntchito za mtokoma***

Boma la DPP lidzakonza ntchito za mtokoma poonetsetsa kuti pali chitetezo pa kutumiza ndi kulandira kwa makalata ndi katundu wa anthu. Tidzaonetsetsanso kuti anthu akulandira zinthu zawo m'nthawi yake. Komanso ntchito yomwe tinayamba kale yoika ma adiresi molingana ndi magawo a dziko lino tidzaipitiriza.

**4.2.3 MPHAMVU ZOGWIRITSIRA MAGETSI NDI ZINA**

Boma la DPP limazindikira kuti chitukuko cha mafakitale, cha anthu, ndi chuma chimadalira mphamvu zochokera ku magetsi amene ali otsika mtengo, odalirika, komanso olingana ndi makono.
Tikudziwa kuti 86 peresenti ya mphamvu yonse imene dzikoli limagwiritsa ntchito imachokera ku mitengo ndi makala. Mphamvu yokwana 10 peresenti imachokera ku mafuta; ndipo mphamvu yochokera ku magetsi ndi yokwana 3 peresenti, pomwe mu malasha muli 1 peresenti yokha.

Nyumba za anthu ndi zimene zimagwiritsa mphamvu yambiri yokwana 81 peresenti, ndipo ntchito za mayendedwe zimagwiritsa ntchito 9 peresenti. Mafakitale amagwiritsa ntchito 8 peresenti, pomwe mbali zina za chitukuko monga zamalonda ndi ulimi zimagwiritsa mphamvu yokwana 2 peresenti ya mphamvu imene ilipo mMalawi.

Nthambi ya mtengatenga kuno ku Malawi imadalira mphamvu zochokera m'mafuta ochokera kunja kwa dziko lino moti 45 peresenti ndi Peturo ndipo 54 peresenti ndi dizilo. Gasi amagwiritsidwa ntchito pa mulingo wa 0.08 pa barelo patsiku pomwe dziko lapansi likugwiritsa ntchito gasi pa mulingo wa 57.49 pa barelo patsiku. Kuyambira m'chaka cha 2021 boma la Kongeresi lalephera kuitanitsa mafuta m'Malawi muno chifukwa cha kusowa kwa ndalama zakunja, zimene zachitika chifukwa cha kusadziwa kayendetsedwe ka chuma ndi kuba.

Magetsi ndi mphamvu yoposa mphamvu zina chifukwa choti savuta kugwiritsa ntchito, komanso kuti amagwiritsidwa munjira zosiyanasiyana monga kuunikira mnyumba, kuphikira ndi kuyendera. Koma mdziko muno magetsi akupezeka mosakwanira. M'chaka cha 2024 tinali ndi magetsi okwana 25.9 peresenti, ndipo 11.3 peresenti ya magetsiwa anali ochokera pa mawaya a ESCOM, pomwe 14.6 peresenti imachokera ku mphamvu ya dzuwa ndi zipangizo zina zam'manja. Mphamvu zonse zimene timagwiritsa ntchito m'Malawi muno ndi 581.5 Megawatts (MW) zomwe zimachokera ku:

- Makina opanga magetsi kuchokera kumadzi (Hydro), pa mulingo wa 398.5MW,
- Mphamvu yochokera mu kutentha kobwera ndi kuyenda kwa zinthu za sayansi monga ma atomu ndi zina zotero (Thermal), pa mulingo wa 53.7MW,
- Mphamvu ya dzuwa (Solar), pa mulingo wa 102.3MW
- Mphamvu yamagetsi yochokera kunja (Imports), pa mulingo wa 27MW.

Koma magetsi amene akupangidwa pano ali pa mulingo wokwana 380MW. Koma panthawi imene anthu ambiri amafuna kugwiritsa ntchito magetsi (peak demand) pamafunika mphamvu yokwana 508MW. Zikuoneka kuti pokwana chaka cha 2030 pazidzafunika mphamvu yokwana 774MW ndipo pofika chaka cha 2042 padzafunika mphamvu ya magetsi yokwana 1,914MW.

Pakufunika kudziwa kuti pafupifupi magetsi onse amene amapangidwa m'Malawi muno (97 peresenti) amapangidwa mu mtsinje wa Shire kummwera kwa dziko lino. Ndipo nyengo zikavuta, monga chilala ndi kusefukira kwa madzi dera limeneli magetsi amakhuzidwa. Komanso magetsi amenewa amagawidwa ku madera onse mdziko muno kudzera m'mawaya a 66 KVA. Pakutero, 5.4 peresenti ya mphamvuyo imatha kuonongeka. Padakali pano kubweretsa magesti kumalo omwe kudalibe nkotsika pa mulingo wa 20 peresenti pa chaka. Ndipo anthu kapena malo atsopano amene amapatsidwa magetsi ndi 45,000 okha pa chaka, poyerekeza ndi malo 205,000 amene amafuna magetsi pa chaka.

Pachifukwa cha ichi, boma la DPP lidzachita izi pothana ndi

mavuto okhuza magetsi:

- Kusintha chuma cha magetsi kuchokera ku mphamvu zodalira zinthu zachilengedwe ndi kubweretsa mphamvu zochokera ku makina a kompyuta ndi zina zotero.
- Kukweza ntchito zogwiritsa gasi (LPG), kugwiritsa ntchito mbaula zosadalira nkhuni, ndi njira zina zophikira ndi kubweretsa moto wogwiritsira ntchito.
- Kulimbikitsa kupanga ndi kugwiritsa ntchito ethanol ndi dizilo wopangidwa mu zinthu zopezeka mdziko muno pakuphikira, ndi kuika m'magalimoto. Koma tidzaonetsetsa kuti pakutero, sitikuchepetsa chakudya cha anthu.
- Kuchepetsa mitengo yogulira zipangizo zophikira ndi gasi kuti anthu a kumidzi ndi m'matauni athe kukwanitsa kuphika ndi zipangizo za magetsi
- Pofuna kuonetsetsa kuti tiri ndi njira zambiri zopangira mphamvu yamagetsi ndi kuonetsetsa kuti zinthu zikuyenda bwino ku mbali imeneyi, boma la DPP:
- Lidzagwira ntchito ndi magulu omwe siaboma otchedwa Independent Power Producers (IPPs) kuti akaike ndalama zawo mu ntchito za magetsi opangidwa ndi mphamvu ya madzi, mphamvu ya dzuwa, mphamvu ya mphepo, gasi, malasha ndi zina zotero.
- Lidzakhazikitsa malo anayi mzigawo zonse za dziko lino komwe mphamvu ya magetsi izidzagawidwa ndi kupita ku madera ozungulira chigawocho, komanso kukonza magetsi akawonongeka
- Tidzapereka magetsi kwa anthu kapena malo atsopano 1 miliyoni mu zaka zisanu zokha.
- Tidzaonjezera mphamvu zamagesti kuti ifike 1,500 MW popanga zinthu izi:
- 300 MW ya mphamvu za malasha pa Kammwamba (kuti tisangodalira magetsi opangidwa mumtsinje wa Shire okha ndi chigawo cha kummwera)
- 309 MW ya mphamvu ya magetsi opangidwa ndi madzi pa Mpatamanga ndi damu loti lithandize kusunga madzi komanso kuthandiza kuti mtsinje wa Shire uziyenda bwino
- 261 MW ya mphamvu ya magetsi opangidwa ndi madzi pa Fufu (kuti tisangodalira magetsi opangidwa mumtsinje wa Shire okha)
- 190 MW ya mphamvu ya magetsi opangidwa ndi madzi ochokera mu mtsinje wa Songwe
- Tidzathandizira makampani opanga mphamvu zamagetsi omwe siaboma kuti akapange magetsi okwana 100MW kuchokera ku mitchini ya mphepo ku Mzimba ndi Chitipa.
- Poonjezera apa boma la DPP lidzabweretsa magetsi ena motere:
- 41 MW ya mphamvu ya magetsi opangidwa ndi madzi pa Bongozi
- 100 MW ya mphamvu ya gasi
- 200 MW kapena kuposa apo yamagetsi a mphamvu ya dzuwa kuchokera ku Nkhatabay, Rumphi, Karonga, Salima, Dedza, ndi Mangochi.
- Tidzabweretsa mphamvu ina ya magetsi yokwana 120 MW kuchokera ku Mozambiki ndi Zambia, komanso nthawi yomweyo tizidzatha kugulitsa magesti kumaiko ena kudzera mumgwirizano wathu ndi maiko otizungulira kudera lino la Africa (Southern Africa Pool).
- Kukonza makina a EGENCO amene amapanga mphamvu zokwana 441MW, ndikuika makina ena atsopano pa Wovwe, Nyika, Mbongozi, Thyolo, Dwambazi, Chasombo ndi Chizuma.
- Kukhazikitsa ntchito yolumikiza Malawi ndi Tanzania kuti tizitha kugula ndi kugulitsa nawo magetsi ku misika ya kum'mawa kwa Africa (Eastern Africa Power Pool).
- Kukhazikitsa ntchito yolumikiza Phombeya ndi Nacala kuti tizitha kugula ndi kugulitsa nawo magetsi ku misika ya kumpoto kwa dziko la Mozambiki.
- Tidzakhazikitsa msika wogulitsa magetsi wotchedwa Power Market Limited ndi cholinga chofuna kuchotsa zipysinjo zimene anthu amakumana nazo podalira kugula magetsi ku Escom kokha. Kudzera mu Power Market Limited tizidzathanso kugula ndi kugulitsa mphamvu za magetsi




kunja kwa dziko lino mosavuta.

- Tidzakweza kagawidwe ka magetsi kufikira 132 KVA motere: Kummawa (Eastern Backbone), ndi Kumadzulo (Western Backbone), Golomoti – Monkey Bay, Nkhotakota – Serengeti – Chinyama – Kanyika line, Lilongwe Loop, Mzimba – Dwangwa line, Phombeya – Liwonde, Kanyika – Chatoloma line, Nkula - Blantyre West – Phalombe – Zomba.
- Tidzalimbikitsanso pologalamu ya Malawi Rural Electrification Program (MAREP) kuti tionjezere kupezeka kwa magetsi kwa anthu okhala kumudzi kapena malo ochitira malonda. Misonkho yotsika idzaikidwa mmalo ndi cholinga choti anthu amene amapeza ndalama zochepa akathe kukwanitsa kukhala ndi magetsi.
- Tidzagwiritsa ntchito makoleji a umisiri ndi maluso (Community Colleges) kuphunzitsa anthu umisiri ndi maluso osiyanasiyana ndi kupanga mabizinezi, pa kapangidwe ndi kagwiritsidwe ntchito ka mphamvu za magetsi za mitundu yosiyanasiyana. Pochita izi tidzalingalira za kusiyana kwa abambo ndi amayi ndi zinthu zina za chikhalidwe chathu monga a Malawi.

#### 4.2.4 NTCHITO ZA MAKOMPYUTA NDI NZERU ZA MAKOMPYUTA ZOFANANIRAPO NDI NZERU ZAMUNTHU

Pansi pa boma la DPP Malawi adzalowa mu nyengo ina yokhuzana ndi makompyuta zomwe zidzasinthe dzikoli kukhala lotsogola pa za makompyuta ndi sayansi, komanso lakutha kupikisana ndi maiko ena pa machitidwe a za makompyuta, ndi maluso ena a sayansi okomera magulu onse a anthu. Pokhazikika pa mfundo za kupezeka kwa ntchito za kompyuta paliponse, kagwiritsidwe ntchito kabwino ka makompyuta, ndi kupereka mphamvu kwa anthu, boma la DPP lidzaika dziko la Malawi pa gulu la maiko khumi otukuka pa ntchito za makompyuta muno mu Africa.

Pofika chaka cha 2030, boma la DPP lidzachita izi:

- Kupereka intaneti kwa 80 peresenti ya anthu m'dziko muno. Dziko la Malawi lidzakhala ndi malo osachepera 2,500 komwe kudzakhale intaneti monga misika, sukulu, zipatala ndi madepoti a basi.
- Kuika ndalama mu National Cloud Data Center kumene kuzikhala data ya boma' ndipo malowa adzathandizira ntchito yokonza nzeru za makompyuta zofananirapo ndi nzeru za munthu (Artificial Intelligence), ndi kukhazikitsa maziko a tsogolo la dziko pa nzeru zimenezi za AI.
- Tidzakonzekeretsa mizinda yathu ku zachitukuko zimene zikudza ndi makompyuta ndi sayansi pokhazikitsa mizinda ya nzeru (Smart Cities) ku Lilongwe, Blantyre ndi Mzuzu kumene ntchito za kompyuta zidzayendetsa ntchito zapanseu, zolondera malo ndi kutaya kwa zinyalala. Ili lidzakhala gawo longoyesera (pailoti)
- Tizabweretsa ntchito zokwana 150,000 zokhuzana ndi makompyuta ndi kubweretsanso mabizinezi okwana 5,000 ochokera mu ntchito za makompyuta
- Tidzakhazikitsa sukulu yapamwamba yoteteza ntchito za makompyuta ya Cybersecurity Academy ndi kupanga ubale ndi sukulu yapamwamba yotchedwa African Institute for Mathematical Sciences (AIMS), IBM, ndi Google kuti achinyamata athu azikaphunzirako maluso amenewa.
- Tidzaonetsetsa kuti nzika iliyonse ili ndi chiphatso cha pakompyuta chokhala ndi zomwe angafune kudziwa zokhuzana ndi umoyo, maphunziro, ndalama za pafoni, zaulimi ndi zina zotero
- Tidzaonetsetsa kuti ntchito zaboma zosachepera 70 peresenti zikupezeka pa tsamba za kompyuta ndi nzeru za makompyuta zofananirapo ndi nzeru za munthu (AI) ndi cholinga choti anthu asamavutike popeza ntchitozo komanso kuti pazikhala kuchita zinthu poyera.
- Kukhazikitsa ndondomeko ya National Artificial Intelligence and Digital Innovation Policy yomwe idzagwire ntchito molumikizana ndi African Union Digital Transformation Strategy ndi ndondomeko za UNESCO AI Ethics.
- Tidzaunikanso ndondomeko ya kayambidwe ka ecosystem policy kuti tilole mfundo zoyendetsera ntchito za chuma choyendera makompyuta
- Tidzakhazikitsa zipangizo za nzeru za makompyuta zofananirapo ndi nzeru za munthu pa ulimi, zomwe zizidzatha kupereka chidziwitso kwa alimi pa zinthu zokhuza nyengo, mitengo ya zinthu ndi nthaka, pompopompo.
- Tidzaika zipangizo zothandizidwa ndi makompyuta m'zipatala za kumidzi ndi cholinga choti pazikhala posavuta kulumikizitsa odwala ndi madokotala odziwa ntchito yawo komanso kuti azitha kudziwa mofulumira nthenda imene munthu akudwala, ndi kuthandiza chidziwitso ngati ogwira ntchito akuchepa ku madera a kumidzi.
- Tidzakhazikitsa malo a boma pamene pazidzapezeka chilichonse chimene anthu afuna kudziwa pompopompo kuti anthu azitha kudziwa zimene boma likupanga ndi ndalama zaboma ndi kumvanso mfundo zimene anthu akunena pa zinthu izi.
- Tidzaika mu maphunziro a ku sukulu ya pulaimale zinthu monga coding, robotics, ndi digital citizenship. Ndipo mu maphunziro a ku sekondale ndi makoleji, tidzaikamo mapologalamu okhuzana ndi nzeru za makompyuta zofananirapo ndi nzeru zamunthu.
-

### 4.3 CHITUKUKO CHA M'MATAUNI

Malawi ndi limodzi mwa maiko amene ali ndi chiwerengero cha anthu a m'tauni chokwera cha 20 peresenti amene akukhala m'mizinda ya Blantyre, Lilongwe, Mzuzu ndi Zomba. Chiwerengerochi chimakwera ndi 5 peresenti pa chaka. Mwa ichi, kukuyerekezedwa kuti chiwerengero cha anthu okhala m'tauni chidzaposa chiwerengero cha anthu okhala kumidzi pakutha pa chaka chino cha 2025.

DPP imakhulupirira kuti anthu amapita kukhala kumene kwapita chitukuko.Choncho pofuna kuchepetsa chiwerengero cha anthu osamukira m'matauni ndi m'mizinda, tiyenera kutenga chitukuko nkupita nacho kumidzi. Masomphenya okhala ndi matauni abwino ngakhale kumidzi, ndi kukhala ndi malo okopa alendo kumene kuli zinthu zothandiza miyoyo ya anthu kukhala yokoma ndi yapamwamba, ndi otheka.

Pachifukwa ichi, DPP idzachita izi:

- Kupitiriza ndi pologalamu ya chitukuko cha kumidzi yotchedwa Rural Growth Centres potsiriza malo amene tinayamba kale ku Nambuma, Chitekesa ndi Nthalire, tisanayambe kutsegula malo ena atsopano m'maboma ena.
- Kuonetsetsa kuti m'chigawo chilichonse muli ntchito zowatumikira anthu monga sukulu za pulaimale ndi sekondale, misika, zipatala, maofesi a ntchito zaboma, malo okonzerapo katundu wa m'minda asanagulitsidwe, polisi, madzi, magetsi ndi miseu yokonzedwa bwino, yoti anthu azigwiritsa ntchito chaka chonse
- Kuika ndalama mwadala mu mafakitale a zinthu zakumunda zimene zidzakhala zokonzedwa bwino zisanapite pamsika, pamene tikupititsa patsogolo kugulitsa katundu kunja kwa dziko lino ndi kuchepetsa katundu woitanitsa kunja
- Kupitiriza ndondomeo zophunzitsa achinyamata athu umisiri ndi maluso osiyanasiyana kudzera mu makoleji akumidzi
- Kulimbikitsa dongosolo lobwezera chuma chochokera ku khonsolo, polipira misonkho ya malo ndi misonkho ina yonse kukhonsolo
- Kugawa bwino maofesi a boma ndi makampani a boma m'mizinda ya Mzuzu, Lilongwe, Blantyre ndi Zomba
- Kusanduliza Mangochi kukhala mzinda; ndi Cape Maclear kukhala malo okopa alendo
- Kuunikanso lamulo la maboma aang'ono (Local Government Act of 1998) kuti livomereze ndi kuchitapo kanthu pa chitukuko cham'maboma
- Kuonetsetsa kuti ntchito za m'matauni zikuyendetsedwa ndi kukonzedwa bwino.

## 4.4 NTCHITO ZOKOPA ALENDO

Dziko la Malawi limadziwika monga Warm Heart of Africa chifukwa cha nsangala ndi kukonda alendo kwa a Malawi. Pophatikiza ichi ndi malo okopa alendo amene alipo, dziko la Malawi likhoza kukhala malo aakulu a alendo muno mu Africa ndi dziko lonse lapansi. Zinthu zimene tili nazo ndi:

- Zokopa alendo pa Nyanja ya Malawi ndi chilengedwe chozungulira nyanjayi
- Zokopa alendo za nyama zakutchire ndi malo ena ochititsa chidwi
- Zokopa alendo zachikhalidwe chathu monga zipilala ndi ziliza za mbiri yadziko lino ndi zina
- Zokopa alendo kudzera mu misonkhano, kuyenda, ndi zochitika zina zimene pachingerezi akuti MICE (Meeting, Incentive travel, Conferences and Events)

Ku Malawi kuli ndi kuthekeka kwakukulu kumbali ya zokopa alendo koma chitukuko cha mbali imeneyi chikubwerera m'mbuyo chifukwa cha zopyinja zambiri. Panopa mbali yokopa alendoyi imabweretsa ndalama zokwana 7 peresenti ya chuma cha dziko (GDP), koma mbali imeneyi itatukulidwa ikhoza kubweretsa chuma chokwana 15 peresenti. Bungwe la National Planning Commission (NPC) linafufuza ndi kupeza kuti zinthu izi ndi zomwe zikupysinja mbali imeneyi: njira za mtengatenga zosakwanira, zokopa alendo zosakonzedwa bwino, malo ogona alendo osakwanira komanso mitengo yake yokwera; kusalumikizika bwino kwa lamya la makompyuta (intaneti), kusowa kwa anthu ndi makampani amene angaike ndalama mu dera limeneli, ndi kuchepa kwa kuchemerera malonda a zokopa alendo, mwa zina zambiri. Boma la DPP lidzagwira ntchito molimbika kuti litukule ntchito zamtengatenga, malo ogona alendo, ndi kuchemerera malonda a zokopa alendo kuti tikope alendo ochuruka ndi kuti kucheza kwao ku Malawi



kuzikhala kokoma. Pakutero chuma cha anthu wamba ndi dziko chidzatukuka. Masomphenya athu ndi oti Malawi akhale pamwamba muno mu Africa pankhani yokopa alendo. Cholinga chathu nchoti kukopa alendo kukhale kochitira ubwino aliyense ndi kubweretsa chuma kwa a Malawi pamene tikukopanso alendo pa dziko lonse lapansi ndi anthu ofuna kuchita malonda mdziko muno. Izinso zipangitsa kuti tikhale ndi chitukuko chokhazikika ndi kubweretsanso ndalama yakunja ndinso kuti dziko lizitukuka.

Pachifukwa cha ichi DPP idzachita izi:

- Kupititsa patsogolo ntchito zokopa alendo mu Africa ndi dziko lonse kudzera mu kampeni ya 'Dziwani kuti kuli Malawi', pachingerezi, "Discover Malawi."
- Kuonetstetsa kuti aMalawi akutha kuyendera malo okopa alendowa pokhazikitsa thumba la ndalama lapadera lothandizira ana asukulu ndi anthu ena ochepekedwa pa ndalama.
- Polimbikitsa kagwiridwe ntchito ka ukadaulo ndi kuika njira zabwino zothandizira makampani kulemba ntchito mmalo awo okopa alendo.
- Kulimbikitsa anthu ndi makampani akunja ndi a mom'muno kuika ndalama zawo mu ntchito zokopa alendo pochita zina mwa izi: kulipira misonkho kudzera pa lamya wa kompyuta, kupanga mgwirizano pakati pa mabungwe a boma ndi mabungwe omwe siaboma, ndi kutukula misika yakunja komwe anthu azikagulitsako katundu opanga okha ndi katundu wa chikhalidwe chathu.
- Tidzaonetsetsa kuti chiphaso chathu cha Visa chikuthandizira ntchito zimenezi kuyenda bwino.
- Tidzaonetsetsa kuti anthu wamba akupindula ndi mbali imeneyi kudzera mu dongosolo loika patsogolo anthu akuderalo lotchedwa "Community First Investment" ndi "Local Business Prioritisation."
- Tidzaika malo ochitirapo zokopa alendo ku Nkhatabay, pachilumba cha Likoma, Salima ndi Mangochi molingana ndi ndondomeko zimene zili mu Malawi National Tourism Investment Masterplan.
- Tidzakhazikitsa malo a padera ochitirako chitukuko cha zokopa alendo ku Nankumba ndi Cape Maclear.
- Tidzawirikiza chitetezo cha nyama zakuthengo m'malo otetezedwa a Nyika, Vwaza, Kasungu, Lengwe ndi Mwabvi, komanso tidzapitiriza kutukula malo osungirako nyama ku Majete, Liwonde ndi Nkhotakota.
- Tidzatukula ntchito zokopa alendo zokhuza mapiri (Mountain Tourism).
- Tidzakuza zipangizo za malo okopa alendo, monga izi;
- Kukonza miseu ya bitumen yopita ku malo okopa alendo ku Rumphi, Nyika, ndi Chitipa
- Kukuza mabwalo a ndege a Chileka ndi Kamuzu, ndi kumanga bwalo landege latsopano pa Mzuzu
- Kukonza mabwalo a ndege ku Karonga, Mangochi ndi Salima
- Kuika sitima zothamanga pa Nyanja ya Malawi
- Kuonetsetsa kuti magetsi ndi okwanira kwa alendo odzacheza ku malo amenewa
- Kuyamba kuyendetsa ndondomeko ya Malawi Tourism Authority
- Kulimbikitsa kumanga kwa sitima za pamadzi zing'onozing'ono.

## 4.5 KUKHAZIKITSA MIZINDA INA

DPP imakhulupirira kuti kutukuka kwa mizinda yachiwiri ndi matauni a kumudzi ndi njira yabwino yothandizira kukula kwa chuma cha anthu kumudzi ndi kukweza miyoyo yawo ya tsiku ndi tsiku. Njira iyi tinayamba kale kuitsata mzaka za pakati pa 2014 ndi 2019 kudzera m'pologalamu yopambana ya Rural Growth Centres ku Nambuma ku Dowa, ku Nthalire ku Chitipa, ku Chitekesa ku Phalombe, kwa Chapananga ku Chikwawa, kwa Mkanda ku Mchinji ndi ku Neno. Mizinda imeneyi inayamba ndi kumanga kwa misika ya makono pa Nsanje, Chinakanaka, ndi

pa Mulanje Mission; ndiponso mabwalo a mpira anamangidwa pa Karonga, Rumphi, Kasungu, Mangochi, Mulanje, Ntcheu ndi Zomba.

M'zaka za 2025 mpaka 2030 tidzalimbikira kukweza malo otchedwa "growth centres" kuti afike pa mulingo wa mizinda yachiwiri. M'malo amenewa mudzapezeka zinthu zokweza miyoyo ya anthu monga zipatala, nyumba zogonamo anthu zabwino, sukulu za mkomba phala, sukulu za pulaimale ndi sekondale, makoleji a zaluso, madzi abwino, miseu ya bitumeni, misika, mabwalo oseweramo, magetsi ndi lamya wa pakompyuta (intaneti). Pokonza mizinda yachiwiriyi, boma la DPP lidzapereka chitukuko malo onse mdziko muno mofanana, ndi kuchepetsanso chiwerengero cha anthu mmizinda yaikulu kapena yoyamba (ya Blantyre, Lilongwe, Mzuzu ndi Zomba).

### 4.6 NTCHITO ZA MALO, NYUMBA NDI MADZI

DPP imazindikira kuti malo, nyumba ndi ntchito za madzi ndi zofunikira kwambiri ku chitukuko cha dziko lina lilrilonse, ngakhale Malawi. Koma pali zovuta zambiri zimene zimapysinja ntchito zimenezi kuno ku Malawi.

#### 4.6.1 ZITUKUKO ZA MALO

Nkhani za malo zafika povuta kwambiri. Malawi ndi limodzi mwa maiko omwe ali ndi anthu mothinana kuno kummwera kwa chipululu cha Sahara ndi chiwerengero cha anthu 139 pa kilomita iliyonse. Chikhalirenicho malo ndi chinthu chofunikira kwambiri ku chitukuko ndi kukula kwa dziko pa mulingo wa 40 peresenti wa chuma cha dziko (GDP), chakudya cha dziko, kulembedwa kwa anthu pantchito ndi ndalama zobwera m'dziko chifukwa cha malonda omwe timagulitsa ku maiko ena. Dziko la Malawi likukumana ndi mavuto ambiri pakagwiritsidwe ntchito ka malo. Zina mwa zovutazi ndi kusadziwika bwino kwa nthawi imene munthu angakhale ndi umwini wa malo, makalata osakwanira pa nkhaniyi, ndi mikangano pakati pa anthu okhala kumidzi ndi kutauni yokhuza malo. Poonjezera apo, malo okwana 60 peresenti ali mmanja mwa mafumu, komanso makalata ake a malowa ndi ochepa; zomwe zimabweretsa mpungwepungwe ndi mikangano yokhuza malire. Mavuto amene alipo ndi awa: mikangano, mfundo zofooka zoyendetsera ntchito za malo, kuika matauni m'malo ochitirapo ulimi, kufulumira kwa kukula kwa matauni ndi kukondera pa kugawa malo pakati pa amayi ndi abambo.

Pa zaka zisanu zikubwerazi, DPP ili ndi ndondomeko zamphamvu zothana ndi mavuto amenwa motere:

- Kupereka umwini wa malo polimbikitsa maufulu okhala ndi malao kwa nzika zonse, kwenikweni kwa amayi ndi magulu ena amene amakumana ndi mavuto ambiri
- Kugwiritsa ntchito makompyuta popereka malo kwa anthu ndi kufupikitsa dongosolo loperekera malo kuti ziphuphu zithe ndipo mikangano ichepe
- Kuika misonkho yachilungamo kuti anthu azikapindula ndi malowo
- Kugawa bwino malo m'magulu awa: malo okhala anthu, malo opangirako malonda, malo ochitirako ulimi ndi malo opangirako mafakitale
- Kulimbikitsa kasungidwe ka malo kuti asaonongeke kudzera mu kudula kwa mitengo ndi kukokoloka kwa nthaka
- Kuthandizira mapulani a malo a kumudzi ndi kutauni kuti malowo akakhoze kukwanira pa chiwerengero cha anthu ndi kukula kwa chuma
- Kukhazikitsa makhoti apadera oti azikaweruza milandu ya malo kuti milanduyo izitha mofulumira
- Kuunikanso malamulo a malo amene anatha ntchito ndi cholinga choti mfundozo zikagwirizane ndi mmene zinthu ziliri makono ano pachuma ndi miyoyo ya anthu

#### 4.6.2 ZITUKUKO ZA NYUMBA

Kumidzi, kumene anthu okwana 82 peresenti amakhala, kulibe nyumba zogonamo zabwino. Ngakhale izi zili choncho, vutoli silili kumidzi kokha, m'matauni mulinso vutoli chifukwa choti anthu ambiri akuchoka kumudzi ndi kudzakhala m'tauni. Ndipo izi zikupangitsa kuti pakhale kulimbirana malo ndi nyumba zogona. Nchifukwa chake pali kuchuluka kwa madera a nyumba zosayenera kugona anthu, kumanga nyumba pa malo a boma ndi mikangano yosiyanasiyana. Kafukufuku akusonyeza kuti 76 peresenti ya anthu okhala mu Lilongwe amakhala m'nyumba zosayenera kugonamo anthu, ndipo anthu amenewa alibe zinthu zoyenera pamoyo wao, komanso nyumbazo nzosakwanira.

M'chaka cha 2014 tinalonjeza kuti tidzatsata ndondomeko zochotsa zipsyinjo zolepheretsa anthu kukhala ndi nyumba zabwino poika pologalamu ya Malata ndi Simenti sabuside ndi cholinga choti ngakhale anthu opeza ndalama zochepa athe kumanga nyumba zabwino. Pologalamu imeneyi inakumana ndi zopsyinja zambiri kuchokera kwa otsutsa boma, amene sanafune kuti tiziika ndalama mu pologalamu imeneyi. Zopysinjazo zili choncho, boma lathu linakwanitsa kumanga nyumba zokwana 22,000 za amayi amasiye, ana okhala okha, anthu osauka kwambiri ndi okalamba.

Kuyambira m'chaka cha 2025 kufika 2030 boma la DPP lidzapanga izi:

- Kupitiriza ndi pologalamu ya Malata ndi Simenti Sabuside.
- Kupereka nyumba zotchipa koma zolimba kudzera mu bungwe la Malawi Housing kuti aMalawi azikhalamo namalipira kapena kugula kumene nyumbazo. Izi zidzapangitsa kuti a Malawi omwe amapeza ndalama zochepa athe kukhala ndi nyumba.
- Kumangira nyumba anthu ogwira ntchito zaboma, apolisi ndi asilikali ankhondo, zomwe okhalamowo azilipira renti yosaposera 20 peresenti ya malipiro awo mpaka atagula nyumbayo ngati angaifune.
- Kuika ndondomeko zoti zizitsatidwa pomanga nyumba.
- Kukhazikitsa malo otchedwa National Spatial Data Centre.
- Kuchita mgwirizano ndi kukopa makampani ndi anthu omwe siaboma kuti athe kumanga nyumba zoti anthu wamba azikachita renti m'matauni ndi madera a kumidzi.
- Kuika ndondomeko zothandiza anthu kuchoka pakukhala pa lendi ndi kugula nyumba nkukhala zawo.
- Kukhazikitsa National Housing Fund yomwe izidzapereka ngongole zofewa zomangira nyumba.
- Kutukula malo amene anthu akugona nyumba zosalongosoka poika miseu yabwino, madzi abwino ndi ntchito zina zotumikira anthu.
- Kukhazikitsa ndondomeko za mamangidwe zogwirizana ndi zinthu zachilengedwe mderalo, komanso kugwiritsa ntchito mphamvu ya dzuwa, kukolola madzi amvula pomanga nyumba zatsopano.

### 4.6.3 ZITUKUKO ZA NTCHITO ZA MADZI

Dziko la Malawi likukumana ndi zovuta zambiri poyesa kupereka madzi kwa anthu onse, ngakhale kuti tili ndi madzi ochuluka. Ngakhale kuti 80 peresenti ya anthu ali ndi mwayi wopeza madzi abwino, kuchuluka kwa chiwerengero cha anthu ndi kuchepa kwa zipangizo zoperekera madziwo ku midzi, kumachepetsa kupezeka kwa madzi abwinowo. Uve ndi kuipa kwa madzi kumabweretsa mavuto pa umoyo wa anthu, monga matenda odza kamba komwa madzi oipa ndi imfa za ana ang'ono. Mavuto aakulu amene alipo kumbali ya madzi ndi awa: kusapezeka kwa madzi abwino m'madera ena, kusemphana kwa chiwerengero cha anthu ofuna madzi ndi kuchuluka kwa madzi abwinowo, kuchepa kwa zipangizo zoperekera madzi, kuchepa kwa ukhondo, mtundu wa madzi amene ali mdera, kasamalidwe ka madzi, utsogoleri pa ntchito yopereka madzi, kuchepa kwa ndalama zoyendetsera ntchito za madzi, kuonongeka kwa chilengedwe, ndi zina zotere.

Kuchokera chaka cha 2025 kufikira chaka cha 2030, boma la

DPP lidzachita izi:

- Kuika ndalama zokwanira mu ntchito za madzi monga madamu, mijigo ndi madzi a m'mipopi.
- Kukonza zipangizo za madzi ndi cholinga choti pasakhale madzi otaika kapena kuperewera kwa madzi
- Kuonetsetsa kuti madzi akugulitsidwa pamtengo wabwino ku makomo amene amapeza ndalama zochepa
- Kuteteza malo amene pamachokera madzi ndi kulimbikitsa anthu a deralo kuteteza malo ozungulira pamene pakuchokera madzi
- Kulimbiktsa njira zothandiza kuti kusintha kwa nyengo kusaononge kapena kuthetsa madzi mdera
- Kupanga ndondomeko zabwino zokhuza madzi ndi kuzigwiritsa ntchito

## 4.7 KUPEREKA MPHAMVU KWA ANTHU

Boma la DPP lidzaonetsetsa ndi kukhazikitsa ndondomeko za mphamvu ku anthu monga mfundo yeniyeni yobweretsa chitukuko, kuchepa kwa umphawi ndi kubweretsa ntchito m'dziko muno poonetsetsa kuti anthu onse akutengapo mbali, ndi kumidzi komwe. Tidzachotsa mphamvu kuchokera ku likulu la dziko lino ndi kupereka mphamvuzo ku maboma.

Pofuna kukwaniritsa lonjezo limeneli, boma lathu lidzathana ndi zovuta izi: Ndalama zosakwanira, kuchepa kwa kuthekera kwa anthu ndi kufooka kwa ntchito za m'maofesi a m'maboma; kufooka kwa mabungwe ena a ndale; kulephera kuchita zinthu poyera ndi modalilika, kuchepa kwa malamulo oyendetsera ndondomekozo, kusalumikizana kumene kulipo pakati pa nthambi zaboma, ndi kusakwanira kwa zipangizo zogwirira ntchitoyi.

Choncho utsogoleri wa DPP udzaunika ndi kukonza ntchito za mphamvu ku wanthu ndi cholinga choti pakhale ndalama zokwanira, kuchepa kwa upangiri kumene kulipo kuthe, komanso kuti pakhale malamulo othandizira kuti ntchitoyi iziyenda bwino, mwa zina.

Pachifukwa cha ichi, boma la DPP lidzachita izi:

- Kuonjezera ndalama zogwilira ntchitoyi poika ndalama zosachepera 5 biliyoni kwacha pa konstichuwense iliyonse pa chaka;
- Kukonzanso ndondomeko zoyendetsera ndalama zopita ku konstichuwense (CDF) ndi cholinga choti ikhale yobweretsa chitukuko chooneka ndi chosintha deralo, ndi anthu okhala kumeneko. Tidzachotsa mphamvu ya ndale pa kayendetsedwe ka thumba limeneli.
- Kuika malamulo oyenera, othandiza kuti CDF yatsopanoyi iziyendetsedwa bwino
- Kukuza ntchito za CDF kuti mukakhalenso ntchito ngati izi, kumanga sukulu za ana a mkomba phala, kumanga sukulu za pulaimale ndi sekondale, zipatala za m'madera, kukonza miseu, kukhazikitsa ma sikimu a madzi, kumanga ma steshoni a polisi, kumanga misika ndi malo ophunzitsirako maluso osiyanasiyana, kupereka ma basale kwa ana osauka ndi kulimbikitsa maphunziro  a ntchito zamanja.
- Kuika ndalama mu maphunziro ndi kulimbikitsa maofesi ochita ntchito za mphamvu ku wanthu, ndi cholinga choti akathe kugwira ntchito zao bwino
- Kuonetsetsa kuti makhonsolo ali ndi njira zokhazikika zopezera ndalama zogwirira ntchitoyo powalola kugwiritsa ndalama zamisonkho zomwe amatolera ku khonsoloko, ndi powapatsa ndalama zoonjezera kuchokera ku likulu la boma
- Kupanga ndi kuunikanso malamulo okhuzana ndi ntchitozi kuti pakhale chidziwitso cha nthambi zosiyanasiyana za boma ndi mmene zimagwirira ntchito zawo
- Kukhazikitsa ndondomeko zamphamvu zoonetsa udindo wa aliyense amene akugwira ntchito imeneyi, monga kuwerengera kwa chuma chimene chikulowa ndi kutuluka



(oditi), kumva maganizo a anthu, mabungwe apadera ounika mmene ntchitozi zikuyendera, pofuna kuonetsetsa kuti makhonsolo akuchita zinthu zothandiza anthu m'deralo
- Kusasala magulu a anthu ena popanga ziganizo ndi kuonetsetsa kuti anthu akutumikiridwa m'madera onse
- Kulimbikitsa zokambirana pakati pa likulu la boma ndi maboma ang'ono ndi mbali zonse zimene zimatengapo gawo, ndi cholinga choti pasamakhale kuchita zinthu zofanana
- Kukonza kagwiridwe kantchito ndi makompyuta ndi zipangizo zina zamakono ndi cholinga choti pazikhala changu ndi kuchita zinthu poyera
- Kuika ku Unduna wa maboma aang'ono magawo oona za zipangizo zogwirira ntchito (Infrastructure Services Unit) ndi gawo loona za m'mene anthu angagwirire ntchito mwapamwamba (Performance Improvement Support Unit)
- Kukonza ntchito za makhonsolo a m'mizinda ndi cholinga chokweza kapezedwe ka ndalama, kaperekedwe ka thandizo kwa anthu, komanso kuti aziima paokha
- Kumanga misika yapamwamba kwambiri m'mizinda ya Blantyre, Lilongwe ndi Mzuzu ndi cholinga chotukula umoyo ndi ukhondo m'misikayi;
- Kuika dongosolo loti chitetezo cha m'makhonsolo chikhale champhamvu ndi chokomera anthu okhala kumeneko, ndi anthu a bizinezi ndi mabizinezi awo
- Kulimbikitsa khalidwe la kuchita zinthu poyera ndi mokhulupirika pakati pa anthu ogwira ntchito m'makhonsolo
- Kuika mayendedwe abwino pokhazikitsa kampani ya mabasi (public liability company) omwe akakhale ndi mitundu yosiyanasiyana molingana ndi miseu imene akuyenda, komanso eni ma minibasi ndi ma takisi adzakhala ndi magawo (shares) mu kampani imeneyo
- Kuonetsetsa kuti anthu ogwira ntchito m'makhonsolo akugwira ntchito yawo mwaukadaulo poonetsetsa kuti anthu akulembedwa ntchito kapena kukwezedwa pantchito molingana ndi maphunziro, maluso ndi kagwiridwe kawo kantchito
- Kupitiriza kumanga maofesi a makono ku makhonsolo a kumidzi kapena matauni
- Kuphunzitsa makhansala kuti azitha kulondoloza ndi kuchita ntchito zachitukuko bwino
- Kubweretsanso zipangizo zochitira ntchito m'makhonsolo monga mathekitare ndi makatapila
- Kuunikanso ndondomeko zoperekera ndalama ku khonsolo ndi cholinga choti ndalama zambiri ziziikidwa mu ntchito zachitukuko, ndipo zogwiritsa ntchito nthawi yomweyo zizikhala zochepa

5

# ZOTHEKERA



## 5: ZOTHEKERA

### 5.1 KUSINTHA MAGANIZIDWE

Kusintha kaganizidwe ndi mfundo yoyamba yopangitsa kuti Malawi 2063 itheke. Kaganizidwe kamakhuzana ndi zikhulupiriro, m'mene munthu amadzionera yekha, ndi mmene akuoneranso anthu ena; m'mene munthu amadzionera kufunika kwake, ndi m'mene amaoneranso kufunika kwa anthu ena, ndi dziko lomuzungulira iye. Choncho kusintha kwa kaganizidwe kumeneku kukuyenera kuchitika paliponse monga, pa munthu mwini, malo ozungulira, ndi m'dziko lake, ndi cholinga chofuna kukhazikitsa chikhalidwe cha kudzidalira kodzipangira chuma.

DPP yaunguza ndi kuzindikira kuti dziko la Malawi lapanika mu chikhalidwe cha chuma cha chikale m'mene ndalama ndi yovuta, komanso anthu ambiri saika kufunika kwa ndalama patsogolo. Mwachikhalidwe, a Malawi ambiri amaona kuti kulemera ndi kudya, ndipo chikhalidwe ndi ana. Pali miyambi itatu imene imatambasula bwino za kaganizidwe kameneka: kulemera ndi kudya, khalidwe ndi chuma, ndi ana ndi chuma. DPP imakhulupirira kupezeka kwa chakudya pakati pa anthu, khalidwe labwino, komanso umoyo wa ubereki. Koma chimene chilipo ndi chakuti ku Malawi kuno sitikutha kuona kuti chakudya, khalidwe labwino ndi umoyo wa ubereki ndi zabwino pophatikizanso ndi kukhala ndi ndalama. M'maiko amene amati ndalama ndiye kutukuka, amaika patsogolo umisiri ndi maluso osiyanasiyana ndi maphunziro.

Kaganizidwe kathu kachikaleka kamapangitsa kuti anthu azifuna kukhala ndi umwini pa zinthu za wena. Kaganizidwe kamenakanso kamakokomeza chikhalidwe chodalira kwambiri anthu ena powatchula kuti ma biggie. Enanso amalanda nazo katundu wa amayi amasiye. Khalidwe lathu pa zakudya ndi lokanika chifukwa timalimbikira kudya zakudya zachikhalidwe monga nsima basi, ndi kuganiza kuti tikati chakudya ndicho nsima basi. Poonjezera apo, kusankhana mitundu kumapangitsa kuti tisalingalire za kuthekera kwa munthu. Ndipo anthu ambiri amaikidwa pa mipando ikuluikulu poonera kumene akuchokera kapena mtundu, m'malo moona kuthekera kwao. Ndipo zonsezi zikupangitsa kuti dziko lino lizibwerera m'mbuyo mmalo mopita patsogolo. Timaona kuti pali zambiri zimene ena amachita zongofuna kudzipambanitsa okha mmalo moyang'ana kupambana kwa dziko. Ngati dziko, masomphenya athu amakhala a zinthu zapafupi osati zinthu zopita nazo patali.

Kaganizidwe kathu pa kukula kwa chiwerengero cha dziko kuyenera kusintha ndithu. Pamene kuthekeka kwa kubereka pakati pa a Malawi kuli pa 3.8 peresenti, ndiponso pamene ana akubadwa 1,400 patsiku, dziko lino liri pa chiopsezo cha umphawi ndi kusatukuka. Kumene tikupitaku sitimanena kuti ana ndi chuma, chifukwa zimenezi zikutanthauza kuti posachedwapa padzafunika kumanga ma bloko a makalasi ophunziramo 22,000 patsiku, pongoyerekeza chabe, mwa zina zimene zidzafunike pa miyoyo ya anthu. Choncho boma la DPP lidzaika ndondomeko zothandiza kuti chiwerengero cha anthu chikhale pa muyeso woyenera. Zina mwa ndondomeko zimenezi ndi monga maphunziro a munthu aliyense ndi njira za kulera.

Pali kaganizidwe konena kuti mwamuna salira. Uku ndi kusamvetsetsa kwa kuthekera kwa anthu amuna, pothana ndi zipsyinjo zimene amakumana nazo. Kotero kuti kaganizidwe kameneka nthawi zina kamathera mu kudzipha. Kafukufuku akusonyeza kuti anthu 80 mwa 100 (80 peresenti) aliwonse omwe amadzipha ndi amuna. Mwachitsanzo, mwa anthu 153 amene adzipha m'chaka cha 2025 pakati pa mwezi wa Januwale ndi Malichi, 125 ndi amuna. Chifukwa cha kaganizidwe koti amuna salira, amuna ambiri samatha kugawana ndi anzawo mavuto awo kuti athandizidwe kapena kukasuma kwa adindo oti awathandize.

DPP ikudziwa za kufunika kwa kusintha kaganizidwe

polimbana ndi miyambo ndi zikhulupiriro zina zomwe zingakhale zotchinga potukula dziko lino. Choncho DPP idzakokomeza kapangidwe ka chuma monga mwala wapongodya posintha dziko lino, ndi cholinga choti tichoke pa kuchepetsa umphawi ndi kufikira muyeso womanga Malawi wopanga zinthu, ndiponso wotukuka. Pakufunika kuchoka pa kaganizidwe kodalira chithandizo kuchokera ku mabungwe ndi maiko ena, ndi kufika pa muyeso woika patsogolo malonda, kugwiritsa ntchito chidziwitso cha makono chokhuzana ndi chuma, popanda kutayiratu chikhalidwe chonse.

DPP ili ndi mayankho ogwirika amene angathandize kuti kaganizidwe kosinthika kakhalepo pakati pa a Malawi onse, kudzera mu maphunziro a aliyense, kusintha kwa kayendetsedwe ka maphunziro a ana, kugwira ntchito ndi anthu a kumidzi, ndi kuchita zinthu mwa chitsanzo pakati pa atsogoleri athu. Ndondomeko za kusinthaku zikutsogozedwa ndi mtsogoleri amene anayamba wachitapo zinthu izi pamene anali mtsogoleri wa dziko lino. Iye anapangapo izi, kusanduliza masomphenya kukhala zinthu zogwirika. Ndiponso ndi munthu amene amadziwa kulumikizana kwa kaganizidwe kabwino ndi kupanga zinthu zooneka, ndi chitukuko cha dziko. Mtsogoleri ameneyi si wina ayi, koma Professor APM.

Choncho DPP kuchokera mwezi wa Sepitembala 2025 kufika chaka cha 2030 idzachita izi:

- Kupititsa patsogolo utsogoleri wamasomphenya ndi kasinthidwe ka dziko womwe sudzalola kuchita zinthu mongoyesera, kapena ndale zongopangira malonda;
- Kupititsa patsogolo malonda ndi maiko ena osati kupempha chithandizo;
- Kuika ndondomeko zabwino zothana ndi kuchulukana kwa anthu;
- Kukhazikitsa mzimu wa kukonda dziko ndi kugwira ntchito mokhulupirika pena paliponse;
- Kupititsa patsogolo mfundo za chipembezo pogwira ntchito ndi atsogoleri a zipembezo potumikira anthu;
- Kukhazikitsa pakati pa anthu kufunikira kwa kukhala ndi ndalama pa chuma cha dziko ndi chitukuko cha anthu onse;
- Kutakasa mzimu wa kugwira ntchito molimbika ndi kudzidalira pakati pa anthu powayamikira ndi kuwathokoza moyenera;
- Kulimbikitsa kaonedwe ka zinthu polimbikitsa maganizo ndi kafukufuku yense amene ali ndi kuthekeka kotukula dziko lino;
- Kulimbikitsa kulima mbeu zakudya zamitundumitundu ndi kaphikidwe ka chakudya kamakono kuti anthu azikhala a thanzi.

## 5.2 ULAMULIRO WOTSATIRA MALAMULO, KAYENDETSEDWE KABWINO KA DZIKO NDI NKHONDO YOLIMBANA NDI ZIPHUPHU

Ulamuliro wotsatira malamulo a dziko ndi maziko olimba a fuko limene muli olamulira ndi olamuliridwa okhala ndi maufulu ofanana pamaso pa malamulo. Ndondomeko ya Malawi 2063 ikunena kuti dziko lino lidzakhala ndi boma loyendetsedwa bwino, ndiponso lotsatira ulamuliro wotsata malamulo a dziko. Koma m'zaka zinayi zapitazi m'dziko muno mwachitika zinthu zambiri zophwanya ulamuliro wabwino ndi kuthetsa ziphuphu. Izi ndi monga kulowetsa ndale mu ntchito za chilungamo, kukondera poweruza milandu, ndi kupereka dala ndalama zochepa ku mabungwe olimbana ndi ziphuphu. Boma la Kongeresi lachita zambiri zopangitsa kuti nsanamira za demokalase monga Nyumba ya Malamulo, bungwe lothetsa ziphuphu (ACB), bungwe lomva madandaulo a anthu wamba la Ombudsman ndi bungwe lolimbikitsa maufulu a anthu la Malawi Human Rights Commission, pongotchula mabungwe ochepa, zikhale zopanda mphamvu. Bomalinso linapangitsa kuti mabungwe amenewa asamalumikizane bwino pogwira ntchito zawo.

Poonjezera apo, boma ili lakhala losasamala malamulo a dziko lino mu njira zambiri. Mwachitsanzo, lapangitsa kuti bungwe la Ombudsman likhale lopanda mphamvu posalabadira ziweruzo zimene zimachokera ku bungweli. Izi sizikupereka chiyembekezo choti anthu angalandire chilungamo, komanso ndi zosamveka kuti boma likulimbana ndi mabungwe ake omwe. Zaonekanso kuti boma ili liribe chidwi chopeza njira zamakono zolimbana ndi khalidwe la ziphuphu. Zamveka kuti Kabineti inakana njira yothana ndi ziphuphu younika m'mene anthu akukhalira pamoyo wao wa tsiku ndi tsiku (lifestyle audit). Ichi ndi chidziwitso choti bomali liribe chidwi pa ganizo lofuna kuthetsa ziphuphu.

**5.2.0 Nthambi za kayendetsedwe ka boma ndi ntchito zawo**

DPP ikukhulupirira kuti mabungwe onse okhuzana ndi kulimbikitsa malamulo a dziko, kupititsa patsogolo ndi kuteteza maufulu a anthu mdziko muno, kulimbana ndi ziphuphu ndi uchifwamba wochita kukonza, ayenera kugwira ntchito mopititsa patsogolo ulamuliro woopa malamulo.

**5.2.1 Ofesi ya Mkulu woona za malamulo**

Mkulu woona za malamulo muno mMalawi (Attorney General) ndi mlangizi wamkulu wa boma pa nkhani za malamulo. Pa lamulo lalikulu loyendetsera dziko lino (Constitution) Attorney General ndi Mlangizi pa za malamulo ku nthambi zonse zitatu za boma monga Nyumba ya Malamulo (Parliament), Oweruza milandu (Judiciary) ndi Ofesi ya Pulezidenti ndi Kabineti (Executive). Mwatsoka, pa ulamuliro wa Kongeresi Ofesi ya Attorney General yasanduka ofesi yochita za ndale m'malo mopereka uphungu ku nthambi zonse za boma mosatengera ndale.

Boma la DPP lidzakambirana ndi nthambi zitatu za boma kuti ntchito za Ofesi ya Attorney General zisinthe ndipo ofesiyo ikhale yolangiza nthambi zonse zitatu za boma, osati kutumikira chipani cholamula. DPP ikukhulupira kuti Ofesi ya Attorney General idzalandila ulemu ngati ili yoima payokha ndiponso kutumikira nthambi zonse zitatu za boma. Ndipo ngati nkofunikira DPP idzapempha Nyumbba ya Malamulo kuti ipange lamulo lofotokoza ntchito ya Ofesi ya Attorney General ndiponso kukhazikitsa Ofesi ya Wachiwiri wa Attorney General ndi cholinga choti Ofesi iliyonse ikachite ntchito zotumikira nthambi zonse zitatu za bomazi.

**5.2.2 Apolisi**

Apolisi ali ndi udindo pa malamulo a dziko lino woteteza munthu aliyense m'Malawi muno. DPP idzachita chotheka kuti Polisi ikhale yoima payokha pogwira ntchito zake, ndipo pakutero idzapereka chikhulupiriro mwa a Malawi. DPP idzaonetsetsa kuti a Polisi akutumikira a Malawi onse osati zolinga za anthu ochepa, kaya a ndale, mtundu umodzi ndi ena otero. Tidzaonetsetsa kuti pali kuthetsa kwa uchifwamba, kubweretsa bata ndi mtendere, ndi kuteteza anthu onse okhala m'Malawi.

**5.2.3 Ofesi ya Wamkulu woyang'anira za milandu**

Boma la DPP lidzaonetsetsa kuti Ofesi ya Wamkulu woona za milandu (Director of Public Prosecution) ikugwira ntchito yake mosaopa, komanso mosakondera. Boma la DPP lidzachotsa mchitidwe wina uliwonse wa tsankho popereka chilungamo. Pa chifukwa cha ichi, tidzalingalira kubweretsa lamulo lothandiza kuti Wamkulu woona za milandu azigwira ntchito yake momasuka, osati mwa mantha, ndipo mopanda kusokonezedwa ndi anthu andale, ndi kuti anthu azikamudalira. Boma la DPP lidzaonetsetsa kuti pali mgwirizano pakati pa Ofesi ya Wamkulu woona za milandu ndi nthambi zina zolimbikitsa anthu kutsatira malamulo, ndi nthambi yolimbana ndi umbanda.

### 5.2.4 Bungwe lofufuza za milandu yokhuzana ndi kubedwa kwa ndalama

Boma la DPP limaona kuti bungwe lofufuza milandu yokhuzana ndi kubedwa kwa ndalama (Financial Intelligence Authority) ndi lofunika polimbana ndi kuba kwa anthu a m'maofesi ndi mabungwe ena a boma. Komanso bungweli ndi lothandiza kubweretsa mwambo pa kayendetsedwe ka chuma muno mMalawi. Boma la DPP lidzalimbikitsa ntchito za bungwe la FIA polimbana ndi milandu ya kuba ndi katangale. Izi tidzachita poonetsetsa kuti bungwe la FIA ndi Financial Crimes Division la ku khothi lalikulu likupatsidwa ndalama zokwanira kuti mabungwewa agwire ntchito zawo moyenera ndi mokwaniritsa chiyembekezo cha a Malawi.

### 5.2.5 Bungwe la maufulu a anthu ndi Ofesi yomva za madandaulo a anthu

Mabungwe awiri amenewa amagwira ntchito yaikulu pokweza ndi kuteteza maufulu a anthu. Boma la DPP lidzapereka thandizo loyenera ku mabungwe awiriwa ndi cholinga choti aMalawi akakhale ndi kugwiritsa ntchito maufulu awo, molingana ndi Malamulo a dziko lino (Constitution). Choncho boma la DPP lidzaika ndalama zokwanira mu ndondomeko ya chuma zopita ku mabungwe amenewa, ndi cholinga choti ntchito zawo zisaime chifukwa cha kuperewera kwa ndalama.

### 5.2.6 Bungwe lolimbana ndi mchitidwe wa ziphuphu

Boma la DPP lidzatsata mfundo yoti pasakhale kulolera ziphuphu mpang'ono pomwe. M'chaka cha 2019 boma la DPP linayambitsa lamulo lolimbikitsa ntchito za Ofesi ya Mkulu wa bungwe lolimbana ndi mchitidwe wa ziphuphu (Anti-Corruption Bureau). Lamuloli linali lokhuza kasankhidwe ka Mkulu ameneyi. Boma la DPP lidzapitiriza mfundo imeneyi ndi cholinga chofuna kuthana ndi chipysinjo cha ziphuphu. Boma lathu lidzaika mmalo njira zodziwa mofulumira ngati mchitidwe wa ziphuphu ukuchitika, komanso padzafunika kufufuza mofulumira ndi kuonetsetsa kuti milandu yokhuza ziphuphu ikuweruzidwa mofulumira. Tidzaonetsetsanso kuti lamulo lake lothandizira izi liripo.

Tikangolowanso m'boma, ife a DPP tidzalimbikitsa ulamulliro wabwino ndi kulamulira motsata malamulo pochita izi:

- Kuika njira zamakono zothana ndi mchitidwe wa ziphuphu kudzera mu ntchito za makompyuta mu maofesi onse a boma, kuopa mchitidwe wongogwiritsa ntchito maganizo a munthu
- Kukhazikitsa oditi ya chikhalidwe cha anthu ogwira ntchito m'boma, kafukufuku wa m'mene ndalama zikugwirira ntchito m'mapolojeketi a boma, ndi ntchito zonse zokhuzana ndi kugula kwa katundu ndi ntchito zina. Tidzaonetsetsa kuti ndondomeko zonse zikutsatidwa;
- Kulimbikitsa maphunziro okhuzana ndi ziphuphu, pozindikira kuti kupewa nkosalowa mthumba kusiyana ndi kufufuza, kapena kuweruza nkhani za ziphuphu
- Kuika chikhalidwe cha kukhulupirika kuyambira pachiyambi: kuphunzitsa achinyamata zokhuzana ndi chikhalidwe, kukhupirika ndi kuipa kwa ziphuphu. Sukulu ndi makoleji akhale ndi maphunziro ophunzitsa za kuipa kwa ziphuphu
- Kulimbikitsa mgwirizano pakati pa mabungwe olimbana ndi ziphuphu monga ACB, FIA ndi Ofesi ya Director of Public Officers Declarations
- Kuonjezera akatswiri ndi ndalama zogwirira ntchito ku ACB, ndi kuonetsetsa kuti mkulu wa ACB ndi akuluakulu onse akusankhidwa m'maudindowa chifukwa choti ali ndi zowayenereza, komanso kuti sakusokonezedwa ndi anthu a ndale
- Choncho DPP idzaunikanso ndondomeko za kasankhidwe ka anthu oti ayesedwe mayeso pa udindo wa mkulu wa ACB popeza kuti ndondondmeko zimene zilipo pano ndi zosavuta

kulowa ndale.

- Kuonjezera maluso a anthu ogwira ntchito ku bungweli ndi ndalama zogwirira ntchito
- Kuonetsetsa kuti pali kafukufuku ndi kuzengedwa kwa milandu yonse yokhuzana ndi ziphuphu ndi kuba kwa ndalama za boma m'zaka zapitazi ndi milandu ina imene inaimikidwa pa zifukwa zosiyanasiyana
- Kuika patsogolo njira zoti amene anaba ndalama za boma abweze
- Kuika ndalama zokwanira mu ndondmeko za boma zothandiza kuti mkulu wounika za kayendetsedwe ka ndalama za boma (Auditor General) azigwira ntchito yake m'nthawi yake ndi kuturutsa malipoti m'nthawi yakenso
- Kudzutsa lamulo loona za ntchito za chilungamo lotchedwa Judicial Service and Adminstration Act ndi kukonzanso ntchito za bungwe loima palokha lomva za madandaulo a anthu lotchedwa Independent Complaints Commission
- Kubwezeretsa ulemu wa nthambi zonse za boma ndi ndondomeko zake poonetsetsa kuti akuluakulu otsogolera mabungwewa akusankhidwa mwa ndondomeko, ndi kuti ali ndi zinthu zowayenereza, osati potengera ndale
- Kulimbikitsa mchitidwe wotsatira malamulo mu ntchito zonse za boma
- Kupereka kuthekera ku Ofesi ya mkulu wowerengera ndama za boma (Auditor General) kuti azitha kuwerengera ndalamazo munthawi yake ndi kuturutsa malipoti munthawi yakenso
- Kuthandiza anthu amene alibe ndalama zokwanira kukhala ndi anthu owaimirira pa milandu (maloya), polemba maloya a boma okwanira ndi kulimbitsanso ntchito za Legal Aid Bureau kumene maloya a boma amapezeka. Tidzaikanso ma ofesi a zachilungamo ku maboma onse ndi cholinga choti anthu azikapeza chithandizo pa ntchito za chilungamo mosavuta.



### 5.2.2 CHITETEZO

Dziko la Malawi likukumana ndi nkhani za chitetezo zovuta kuzimvetsa. Pali zina zachidziwikire komanso zina zachilendo zimene zikuopseza chitetezo cha dziko la Malawi. Zinthu izi ndi monga chisokonezo chochokera kwa anthu ovutitsa, kuzembetsa anthu, kuonongeka kwa zinthu zachilengedwe, miliri, umbanda wa mommuno komanso wina wochokera kunja. Poonjezera apo, kuvuta kwa ntchito za chitetezoku kwabweranso ndi kuthamanga kwa ntchito za makompyuta ndi makina amakono. Zonsezi zikuonjezera mavuto a chitetezo m'dziko lino.
Kuyambira m'chaka cha 2020 mchitidwe wa umbanda wakwera mMalawi muno ndi 10 peresenti, kwenikweni chifukwa cha kusowa kwa ndalama pakati pa anthu. Kuphwanya nyumba ndi maofesi ndi kuba koopseza ndi zida kwakula. Mavuto ena ndi kugwirira azimayi ndi ana, ndi mchitidwe wophana umene wakula ndi 15 peresenti. Pamene izi zili choncho, mchitidwe wotenga malamulo m'manja podzera mukulanga munthu akagwidwa, wakulanso. Izi zafika pamenepa chifukwa cha kuchepa kwa anthu a chitetezo (apolisi) amene ali pa chiwerengero cha wa polisi mmodzi pa anthu 1,262. Koma ndondomeko za bungwe la maiko onse la United Nations linaika kuti pazikhala wa polisi mmodzi pa anthu 500. Ziwembu zabweretsa mavuto ooneka ndi maso, a m'malingaliro ndi a mumtima. Koma milandu ya panseu yachepa ndi 20 peresenti chifukwa choti a polisi a pamseu ndi ochuluka kwambiri.

DPP ikudziwa kuti padzafunika njira zamakono zothana ndi mavuto amene alipo pano. Komanso padzafunika kulumikizana kwabwino pa mabungwe omwe siaboma amene amaona za izi, pofuna kuti dzikoli lipite patsogolo. Choncho cholinga cha DPP ndi chofuna kupereka chitetezo kwa anthu onse, chuma chawo, zipangizo zothandizira kuti dziko liyende bwino, ku madera onse a dziko lino.

Pofuna kuthana ndi mavuto a chitetezo amene dziko lino likukumana nawo makono ano, pakufunika kulumikizitsa mabungwe kapena maofesi onse okhuzana ndi ntchito za chitetezo. DPP ikudziwa kuti sipangakhale chitukuko ngati palibe chitetezo. Ndiponso sipangakhale chitetezo ngati palibe chitukuko. Choncho mpofunika kuti nthambi zonse za chitetezo monga Malawi Defence Force, Malawi Police Service, Prison Service, Immigration ndi National Intelligence Service zigwire ntchito limodzi pothandiza boma kuti likwaniritse zolinga zake. Boma la DPP ndi lokonzeka kuchotsa mchitidwe wotsogoza ndale m'mabungwe onse a chitetezo, kupereka zipangizo zoyenera kwa ogwira ntchito zimenezi, ndi kulemba ntchito anthu a chitetezo okwanira.

#### Asirikali a nkhondo

DPP ili ndi chikhulupiriro pa asirikali ankhondo monga nthambi ya boma imene inakhazikitsidwa m'malamulo athu a dziko, pa sekishoni 159 kuti ikathe kulimbikitsa ndi kuteteza dziko la Malawi ndi zokhumba zake kwa adani a dziko lino, a mkati kapena kunja kwa dziko. Posachedwapa tinaona asirikali akuthandiza a polisi pa ntchito yopulumutsa anthu, katundu ndi kupereka chilimbikitso kwa anthu amene akupanga mabizinezi nthawi ya ngozi zogwa mwadzidzidzi. Koma anthu ena a ndale akhoza kutengerapo mwayi wogwiritsa ntchito asirikaliwa pantchito za ndale. Ndiye m'malo moteteza anthu nkumanka nazunza anthu omwe iwo ayenera kuwateteza. DPP idzachotsa mchitidwe umenewu.

Kuyambira chaka cha 2025 mpaka 2030 boma la DPP lidzachita izi:

- Kukonza kuthekera ndi ukadaulo wa malo a chitsanzo ku Malawi Defense Force monga – National Defense College, MDF Command and Staff College (MDFCSC) ndi Malawi Armed Forces College (MAFCO) kuti asirikali akathe kutumikira mokwanira ndi moyenera anthu a dziko lino.

- Kukhazikitsa gulu lapadera (Special Forces Unit ) komanso kukweza kuthekera kwa nthambi imeneyi kumbali ya chiwerengero, makina ogwiritsa ntchito ndi ntchito za makompyuta kuti akathe kuthandiza anthu bwino nthawi ya ngozi zogwa mwadzidzidzi
- Kukweza chikoka pakati pa asirikali powaphunzitsa bwino za ntchito yawo, kuwagulira ma uniform , kuwapatsa zida zoyenera, ndi kutukula ndondomeko zawo zapantchito ndi zinthu zina zokhuza miyoyo yawo
- Kuima nawo pa ntchito zimene akugwira mmalo amene ali mmbali mwa dziko lino ngati ku Nsanje, Mulanje, Blantyre, Lilongwe, Mchinji, Likoma, Chitipa and Karonga, ndi ena otero.
- Kuthandiza asirikali pamene ali kuthandiza a polisi kukhazikitsa bata ndi kuthana ndi umbanda, motsatira malamulo a dziko lino.
- Kuonetsetsa kuti ntchito zina za asirikali zikumawabweretsera ndalama ndi cholinga choti azitenga nawo mbali pa kukweza chuma cha Malawi.
- Kukonza nyumba za asirikali zimene zilipo, ndi kumanga nyumba zatsopano zokwana 2000
- Kumanga chipatala chapamwamba chomwe chidzakhale ndi zipangizo zapamwamba
- Kuthandiza asirikali kutenga nawo mbali pa pologalamu ya bungwe la United Nations Organisation Stabilisation Mission ku DRC (MONUSCO) Force Intervention Brigade (FIB), Southern Africa Mission ku DRC (SAMIDRC) ndi nthambi yoona za asirikali mmaiko ena (military observer mission).

**Apolisi**



DPP idzathandiza apolisi kukwaniritsa masomphenya oti azigwira ntchito yao mwaukadaulo kuti m'dziko muno mukhale chitetetzo kwa aliyense kudzera mu kulepheresa ndi kufufuza bwino za umbanda, kumanga ndi kupititsa kumakhoti onse ochita zimenezi; kukhazikitsa bata ndi mtendere; kuteteza miyoyo, katundu ndi maufulu a anthu ndi kulimbikitsa anthu kusunga malamulo amene ali mbali immodzi ya ntchito yawo. Mwachindunji, DPP idzachita izi:

- Kuonetsetsa kuti kukonzanso kwa ntchito za apolisi kwachitika, ndi kugulira apolizi zipangizo zoyenerera ndi kagwiridwe ntchito katsopano.
- Kupanga polisi kukhala yokhala bwino ndi anthu ndiponso kuti anthu aziikhulupirira. Tidzaika ndondomeko zoti apolisi ndi anthu wamba m'madera onse azigwira ntchito limodzi pothana ndi mavuto a umbanda
- Kupereka ndalama zokwanira ku bungwe lomva madandaulo a anthu la Independent Complaints Commission (ICC) of Police ndi cholinga choti azitha kumva ndi kuthandiza pa madandaulo omwe anthu amakhala nawo okhuza apolisi. Izi zidzathandiza kuti pakhale kudaliridwa, ukadaulo, kusunga mwambo, kutsatira malamulo a dziko lino ndi kusaphwanya maufulu a anthu pogwira ntchito zawo.
- Kukhazikitsa magulu a apadera mu Polisi yomweyo oti azitha kugwira ntchito bwino m'mizinda yathu
- Kuthandiza mizinda ya Mzuzu, Lilongwe, Mangochi, Blantyre ndi Zomba kuti ikhale ndi maofesi a polisi a iwo okha, ndi cholinga choti azikatha kukwaniritsa zosowa zawo pa chitetezo cha mizinda yawo
- Kuonjezera zipangizo zothandizira mmiseu yathu kupewa ngozi poikanso ma kamera a CCTV. Ndipo tidzaikanso dongosolo loti anthu azilipira chindapusa kudzera m'makompyuta osati kupereka ndalama pamanja kwa apolisi, ndi cholinga chochepetsa nthawi, ndalama ndi katangake
- Kupeza njira zina zopimira madalaivala ngati aledzera mowa mmalo mwa makina opimira a breathalysers
- Kuthandiza apolisi kuzama pa njira zokhazikitsa bata pakati pa anthu
- Kupititsa patsogolo luso la apolisi pankhani zopeza, kufufuza ndi kupititsa milandu yosiyanasiyana ku khoti
- Kukonza nyumba za apolisi ndi kumanga zina zatsopano zokwana 4,500
- Kulimbikitsa mgwirizano pakati pa apolisi m'dera lino la kummawa kwa Africa ndi maiko enanso

**Bungwe loyang'anira ndende**

Ndende zathu kuno ku Malawi ndi zodzadza ndi akaidi. Ndende zathu zinamangidwa kuti zithe kusunga akaidi 10,000, koma pano zikusunga akaidi okwana 15,000. Tili ndi ndende 23 koma zimenezi sizikukwanira ayi, ndipo ndende zambiri ndi zakale kwambiri. Mwachitsanzo ndende yaku Zomba ndi yakale kwambiri, yomwe inamangidwa m'chaka cha 1935. Boma la DPP lidzathetsa mavuto a ndende monga kudzadza kwa ndendezo, kusadya mokwanira kwa akaidi ndi kufa kwa akaidi kumene kukuchitika. Mwatchutchutchu, boma la DPP lidzachita izi:

- Kukonza ntchito za ndende kuti zikhale malo othandizira akaidi kusintha chikhalidwe ndi kuthandiza pa chitukuko cha dziko lawo, ndi kulimbikitsa chitetezo cha anthu ndi katundu. Ndipo chidwi chathu chidzakhala pa kuthandiza akaidi kusintha chikhalidwe ndi kuti abwelerenso kumadera amene anachokera.
- Kumanga ndende zatsopano ku Phalombe, Salima, Mchinji, Rumphi ndi Monkeybay
- Kulimbikitsa ntchito za chilungamo monga kusintha khalidwe la akaidi, kulimbikitsa dongosolo lokhululukira akaidi kapena kulolera kuti akaidi azigwira chilango pochokera kwawo osati m'ndende.
- Kuthandiza ndende zathu kulima zakudya zoti akaidi azidya ndi kuti chotsalacho azigulitsa ndi kuchitira chitukuko pa

ndendepo

- Kukonza nyumba zimene zilipo kale ndi kumanganso nyumba zatsopano 1,500
- Kusamutsa ndende za Maula, Chichiri ndi Zomba kuchoka pakati pa tauni ndi kuzimanga kunja kwa malo a bizinezi
- 

**Ntchito za Uteketefi ndi ukazitape**

DPP imadziwa kuti bungwe la National Intelligence Service (NIS) limene limanunkhiza zinthu zaupandu zisanachitike ndi lofunika kwambiri ku chitukuko cha dziko lino, chifukwa limapereka upangiri wothandiza kuti atsogoleri apange ziganizo zabwino mu nthawi yake, ndi kuonetsetsa kuti dziko ndi lotetezedwa kwa adani, ndipo chitukuko ndi mtendere zikupita mtsogolo.

- Boma la DPP lidzaonetsetsa kuti bungwe la NIS ndi mbali ya chitetezo cha dziko ndipo silidzakhala lokondera mbali imodzi. Ndipo nthawi yomweyo nthambiyi idzakhala yogwira ntchito mwachinsinsi.
- Bunngwe la NIS lidzakhala ndi zipangizo zoyenerera kuti lizikatha kupereka upangiri wofunikira ndi woona ku nthambi za chitetezo za dziko lino ndi kukwaniritsa zolinga za nthambiyo.

**Ntchito za Kulowa ndi kutuluka mdziko ndi Unzika**

Boma la DPP lidzathandizira nthambi ya Kulowa ndi kuturuka m'dziko ndi unzika kugwira ntchito yawo moyenera, popereka ziphatso zoyendera kunja kwa dziko lino kwa amene ali ndi zowayenereza kulandira ziphatsozo. Izi zidzathandiza pa chitetezo ndi chitukuko cha dziko lino. Padakali pano ntchito yopereka ziphatsozi yasokonekera kwambiri. Bungwe la Kulowa ndi kuturuka mdziko ndi Unzika linasiya kupereka ziphatsozi ku Mzuzu, Mangochi ndi Blantyre. Poonjezera apo, ziphatso zimene zikupangidwa ndi zopanda kaso ndipo zochititsa manyazi kwambiri, moti nzika zina za Malawi zikukanizidwa kulowa m'maiko ena pogwiritsa ntchito ziphatsozi. Poonjezera apo, anthu ena omwe si a Malawi, anthu ambanda ndi ena otero anapatsidwa ziphatso zimenezi, chimene chili chinthu chomvetsa chisoni kwambiri.

Choncho Boma la DPP lidzachita izi:

- Kubwezeretsa kudalirika ndi kaso zimene zinalipo kale pa ntchito za ziphatso
- Kuonetsetsa kuti anthu omwe si aMalawi asakhale ndi ziphatso zimenezi koma aMalawi okha
- Kutsegulanso nthambi za Mzuzu, Mangochi ndi Blantyre kuti ziyambenso kupereka ziphatsozo
- Kuonjezera malo ena anayi kumene anthu azikatengerako ziphatso zosiyanasiyana, kuti pakhale changu ndi kuchepetsa mitengo yopezera ziphatsozi
- Kukonzanso nyumba za ogwira ntchito ndi kumanganso nyumba zina zatsopano 4,500

### 5.2.3 MGWIRIZANO NDI MAIKO ENA NDI NZIKA ZOKHALA KUNJA KWA DZIKO LINO

Boma la DPP lidzadziwika ndi utsogoleri wogwiritsa ntchito mfundo zofanana ndi mfundo zimene maiko onse a demokalase amagwiritsa ntchito. M'zaka zisanu zikudzazi boma la DPP lidzapitiriza kulimbikitsa ubale ndi maiko ena popititsa chitukuko cha dziko lino patsogolo. Mu zaka zisanu zimenezo, boma la DPP lidzachita izi:

- Ubale wakuchita malonda ndi maiko ena ndi kukulitsa misika ya malonda ndi ntchito za dziko lino
- Kuonjezera anthu ndi mabungwe ofunika kugwira ntchito m'dziko muno ndi kutukula chuma chathu
- Kupeza ngongole kuchokera ku maiko ndi mabungwe osiyanasiyana pa mgwirizano wa dziko ndi dziko, kapena dziko ndi maiko ambiri
- Kuonjezera ntchito zokopa alendo
- Kukhala ndi kuthekeka kokhala ndi zinthu zothandizira pa

chitukuko monga mphamvu za magetsi, madzi, katundu wosakonza mmamfakitare (raw materials) ndi mafuta
- Kuzamitsa mgwirizano pa maphunziro ndi chikhalidwe pakati pa a Malawi ndi anthu a maiko ena
- Kulimbikitsa mgwirizano ndi maiko ena pantchito za kafukufuku wa sayansi ndi makina opangira zinthu kuti chidziwitso cha aMalawi chikhale chachikulu polimbana ndi mavuto osiyanasiyana amene amawakhuza
-

Pamwamba pa ubale wa chitukuko ndi maiko ena, boma la DPP lidzachita izi:
- Kulimbikitsa chitetezo cha dziko lino poteteza malire, ulemu wa dziko lino ndi chitetezo cha anthu ake ku ziwembu zochokera kunja kwa dziko lino
- Kulimbikitsa bata m'dera lino potenga nawo mbali mzokambirana zodzetsa bata ndi mtendere ndi kuletsa kusamvana pakati pa maiko
- Kuchita mgwirizano ndi maiko amene tili nawo zolinga zofanana kuti tipititse patsogolo zolinga zathu
- Kutengapo mbali pa mabungwe akunja amene ali ndi zolinga zofanana ndi zolinga za dziko lino
- Kulimbikitsa ndi kuteteza ufulu wa chibadidwe ndi ulamuliro wotsata malamulo
- Kupereka chithandizo kwa anthu amene akhuzidwa ndi ngozi zakugwa mwadzidzidzi
- Kuteteza zachilengedwe pochita zinthu ngati izi: kupeza njira zolimbana ndi kusintha kwa nyengo ndi kulimbikitsa chitukuko chokhazikika poonetsetsa kuti pali kulumikizana kwa chuma ndi zofuna za anthu ndi chilengedwe, komanso zofuna za anthu ku mibadwo imene ilinkudza
- Kulimbikitsa mgwirizano wa boma ndi boma linzake pa za ogwira ntchito ku maiko ena mu ntchito zokomera maiko athu

DPP idzapitiriza kulimbikitsa za malonda ndi mabungwe komanso maiko akunja ndi cholinga choti thandizo lochokera kunja lizingokhala lochitira ntchito zazikuluzikulu. Ndalamazo zidzakhalanso zokhazikitsa ntchito zachuma mdziko lino, ndi ntchito zina zokhuza miyoyo ya anthu. Boma la DPP lidzakambirana ndi mabungwe ndi maiko akunja pa mfundo zokomera mbali zonse monga, kuvomereza ndondomeko zokonzedwa mdziko lino, ndi kupewa mchitidwe wongotenga ndondomeko zimene amagwiritsa ntchito kwina nkumati zigwiranso ntchito mdziko muno mofanana. Tidzaonetsetsanso kuti mfundo za chuma ndi chitukukozi zikhale zokomera anthu wamba.

Ife tikudziwa kuti Malawi si chilumba chokhala pachokha ndipo msika wake ndi waung'ono umene sungathe kukopa makampani ndi mabungwe ofuna kuika ndalama zawo mu kupanga kwa chuma mokwanira. Ichi ndi chifukwa chake boma la DPP linatsogolera zokambirana zimene zinayambitsa gulu la maiko 54 lotchedwa African Continental Free Trade Area (AfCFTA) lomwe linayamba kugwira ntchito zake pa 1 January 2021. Choncho DPP idzapitiriza kulumikiza a malonda athu ndi misika ya malonda monga COMESA, SADC ndi bungwe lija la COMESA-EAC-SADC Tripartite FTA mmene muli maiko 26, ndi cholinga chofuna kukhazikitsa maziko a kukula kwa chuma ndi chitukuko.

Boma la DPP lidzagwiitsa ntchito zinthu zimene maiko ena alibe pa mfundo yoti maiko ndi osiyana koma ofanana mu lamulo la maiko onse lotchedwa Law of Nations. Mwatchutchutchu, DPP idzaonetsetsa kuti ubale wa Malawi ndi maiko ena ukhale wokomera anthu ake, ndi wothandiza kutumiza katundu wake kunja, ndi kutengapo mbali pa misika ya m'maiko ena. Pansi pa ulamuliro wa DPP, dziko la Malawi lidzapitiriza kulemekeza mgwirizano umene unakhazikitsa bungwe la African Union (AU) pamalonda ndi ntchito zina. Tidzalimbikitsa kuti Malawi azitenga nawo mbali pa ntchito zachuma zochitika m'dera lino la Africa, ndi maiko ena onse kumene Malawi anasainilako mgwirizano.

Boma la DPP lidzapitiriza kuunika migwirizano imene ilipo ndi maiko ena, ndi cholinga chofuna kulimbikitsa ubale ndi mabungwe ndi maiko ena.

Boma la DPP lidzaunikanso maofesi ake aukazembe kunja kwa dziko lino; kuonanso chiwerengero ndi ukadaulo wa ogwira ntchito kumeneko. Tidzatseka maofesi amene sakupindulira dzikoli ndi kutsegula maofesi amene akhoza kupindulira dzikoli. Kuti tikwaniritse mfundo zimenezi, boma la DPP lidzakhazikitsa ntchito zaukazembe wamphamvu ndi cholinga choti dziko la Malawi likathe kukweza ntchito za ukazembe wachitukuko ndi kupeza phindu lambiri pokhala membala wa magulu a maiko osiyanasiyana.

Poonjezera apo, boma la DPP lidzaphunzitsa bwino akazembe ake, kuti akagwire ntchito yawo mwaluso ndi ukadaulo mmaofesi a ukazembe kumene akatumizidwe. Boma lidzakhazikitsanso ndondomeko zabwino zothandiza munthu kukwera pantchito za ukazembe.

**AMalawi okhala kunja kwa dziko lino**

DPP imayamikira zinthu zabwino zimene aMalawi okhala kunja kwa dziko lino amachita. Mu kampeni yathu ya 2014 tinalonjeza kuti tidzabweretsa ndondomeko zoti munthu akhoza kukhala ndi unzika wa maiko awiri. Izi zinachitika mu ulamuliro wa DPP pakati pa 2014 ndi 2020. DPP inachotsa malamulo akale ndi kuika lamulo limeneli. Tinalonjezanso kuchotsa zopsyinja a Malawi akafuna kutumiza ndalama ku Malawi kuchokera kunja. Boma la DPP linasintha malamulo, ndipo pano m'Malawi aliyense akhoza kutsegula akaunti yosungiramo ndalama zakunja (Foreign Currency Denominated Accounts (FCDAs) mu banki ina iliyonse m'Malawi muno. Pofuna kuthandiza aMalawi okhala kunja kwa dziko lino, tinatsegula ofesi ya Diaspora (Diaspora Unit) ku Unduna woona za maiko akunja. Pano ofesi ya kazembe iliyonse ili ndi mbali yokhuza nkhani za anthu okhala kunja, ngati malo oyambirira kufunsako thandizo pankhani za anthu akunja. Popita mtsogolo, boma la DPP lipitiriza kuchita zinthu zokomera anthu okhala kunja kwa dziko lino, ndi kuchotsa zipsyinjo zina zilizonse zopinga anthu amenewa, kuti azitengapo mbali pa chitukuko ndi zochitika za m'dziko lawo.

## 5.3 KAGWIRIDWE NTCHITO KA MAOFESI A BOMA

Ndondomeko ya Malawi 2063 ikunena za a Malawi a mtendere, okonda ndi kunyadira dziko lawo; amenenso ali odzikhulupirira pa zimene angathe kuchita pomanga dziko la Malawi. Ntchito za boma ziyenera kukhala ndi anthu odziwa ntchitozo kuti akathe kutumikira anthu bwino. DPP imadziwa udindo wa ntchito za boma kuti ndi zimene zimapangitsa boma kuti litumikire anthu ake bwino.

**Nyumba ya Malamulo**

DPP imakhulupirira kuti udindo waukulu wa Nyumba ya Malamulo ndi kuonetsetsa kuti Ofesi ya Mtsogoleri wa dziko ndi nduna zake akugwira ntchito zawo moyenera ndi motsata malamulo. DPP idzaonetsetsa kuti Nyumba ya Malamulo ikugwira ntchito yake moyenera ndipo kuti nthambi zina za boma sizikusokoneza ntchito za Nyumbayi. Patatha zaka makumi atatu tili mu ulamuliro wa demokalase DPP ikudziwa kuti Nyumba ya Malamulo imagwira ntchito yolumikizitsa a Malawi onse. DPP idzaonetsetsa kuti malamulo amene Nyumba ya Malamulo ikupanga ndi okomera ndi kutumikira aMalawi, popanda kusankhana mitundu kapena zinthu zimene ali nazo.

**Ofesi ya Mtsogoleri wa dziko ndi nduna zake**

Boma lathu lidzaika m'malo ndondomeko ndi malamulo amene akuimilira zolinga ndi zokhumba za aMalawi. Pozindikira kuti chuma choyendetsera dzikoli chimakhala chosakwanira,

komanso potengera izo zimene tidaziona tikulamulira, boma la DPP lidzakhala ndi kabineti yaing'ono. Ndipo kabinetiyo idzathandizidwa ndi ogwira ntchito za boma a luso ndi osakondera pogwira ntchito zawo. Ndipo tidzaonetsetsa kuti boma likuchita zinthu zooneka ndi maso, osati zongokambapo ayi. Boma la DPP lidzakhazikitsa chikhalidwe chochita zinthu mwa njira yovomerezeka ndi motsata malamulo. Padzakhala kalondolondo wa ntchito za mabungwe onse a boma amene ali pansi pa Ofesi ya Pulezidenti ndi Kabineti, kuti zinthu zizichitika motsata malamulo.

**Oweruza milandu**

DPP imadziwa udindo wa anthu oweruza milandu poteteza ufulu wa demokalase umene unadza m'dziko lino m'chaka cha 1994. DPP idzateteza ndi mtima wake wonse udindo wa oweruza milandu pakutanthauzira ndi kuteteza malamulo a dziko la Malawi ndi kuonetsetsa kuti maufulu a aMalawi akutetezedwa ku mphamvu za boma. Nthawi yomweyi tidzaonetsetsa kuti oweruza milandu akuchita izi mokomera nzika zake. DPP ikutsimikiza kuti anthu oweruza milandu ndi manthu wa ndondomeko zothetsera mikangano pakati pa anthu komanso nsanamira yoteteza ndi kutsatira malamulo a dziko lino.

**Kagwiridwe Ka Ntchito Za Boma**

Boma la DPP limadziwa kuti ntchito za boma ziyenera kugwiridwa molingana ndi mfundo za boma. Pogwira ntchito pamafunika kudaliridwa ndi anthu, kuchita zinthu poyera, kusintha miyoyo ya anthu, kusakondera, chilungamo, kufikirika ndi zina zotero. Ntchito za boma zomwe zikamayenda motsata ndondomeko ndi malamulo zimathandiza kuchepetsa ziphuphu kumabungwe a boma. Chipani cha DPP chikutsimikiza kuti chidzaonetsetsa kuti mabungwe a boma akugwira ntchito motsata malamulo, ndi kuti nthambi iliyonse ya boma ikugwira ntchito yake popanda kusokonezana, kuopsezana kapena kukakamizana kuchita zinthu zophwanya ndondomeko kapena malamulo.

DPP idzaonetsetsa kuti nthambi iliyonse ya boma monga Ofesi ya Pulezidenti, Nyumba ya Malamulo ndi Oweruza milandu akugwira ntchito zawo motumikira a Malawi. Ndipo kuti pakutero, nthambi iliyonse ndi yoima payokha ngakhale pali kulumikizana pa kagwiridwe ka ntchitozo. Ntchito za boma zambiri sizikuyenda bwino ngakhale kuti ntchito zina zachitika pa zaka zingapo zapitazo. Ntchito yosintha kagwiridwe ka ntchito m'boma kamene kanachitika zaka zisanu ndi chimodzi zapitazo m'boma la DPP ndi zomwe zikuoneka. Zimene boma la Kongeresi lachita sizikudziwika ngakhale kuti lipoti lake linalembedwa ndi kukaperekedwa kwa Mtsogoleri wa dziko lino. DPP idzapitiriza pamene inalekera ndipo, mwa zina, idzaunikanso malipiro a ogwira ntchito za boma.

Kuyambira m'chaka cha 2025 kufikira 2030 ndi kupyola apo, boma la DPP lidzachita izi:

- Kutumikira anthu ake bwino ndi kuonetsetsa kuti ntchito zaboma ndi zopatsa chikoka kwa anthu, moti anthu azikaona mboma ngati malo omwe munthu akhoza kugwirako ntchito
- Kuunikanso m'mene ntchito za boma zimayendera ndi kuunikanso chiwerengero cha ogwira ntchitozo ndi cholinga chofuna kuchepetsa kuonongeka kwa ndalama za boma, pamene tikukweza patsogolo kagwiridwe ka ntchitozi
- Kukweza malipiro a anthu ogwira ntchito m'boma molingana ndi mitengo ya zinthu, potsatira kugwa kwa mphamvu ya ndalama yathu ndi kukwera kwa mitengo ya zinthu m'boma liripoli
- Kukweza pantchito ogwira ntchito onse amene kukwera kwao pantchito kunaima pa zifukwa zina
- Kulemba ntchito aphunzitsi ndi ogwira ntchito m'zipatala amene ali ndi zowayenereza kugwira ntchitozi, koma akulephera kulembedwa ntchito chifukwa cha ndondomeko

zosamveka ndi zipsyinjo zina
- Kuyambitsa ngongole za nyumba kwa anthu ogwira ntchito m'boma.
- Kupereka sikimu ya kuchipatala kwa onse ogwira ntchito m'boma ndi omwe anapuma pa ntchitozi
- Kuchepetsa nthawi imene imakhalapo kuti munthu alandire ndalama zake akapuma pantchito
- Kuika anthu oyenerera m'malo oyeneranso kuti pakhale kagwiridwe ntchito kaukadaulo ndi kuthandiza anthu mofulumira m'boma
- Kuunika ndi kukonzanso kayendetsedwe ka ntchito za boma
- Kulimbikitsa kagwiridwe ntchito kaukadaulo ndi changu pokhala ndi ndondomeko zabwino zoyesera anthu kuti akwezedwe pantchito zawo
- Kukonza ndi kumanga maofesi a ntchito zaboma atsopano ndi cholinga chofuna kuchepetsa ndalama zimene zimaonongeko chifukwa cha kukonza maofesi akale, komanso ndi cholinga chofuna kuti malowo azipereka chikoka kwa anthu onse
- Kupereka mwayi kwa ogwira ntchito wopitiriza maphunziro awo ndi cholinga chokweza magwiridwe a ntchito zawo
- Kupereka ndalama moyenera ndi munthawi yake ku mabungwe onse a boma kuti azitha kugwira ntchito zawo bwino.
- Kuphunzitsa ogwira ntchito m'boma molingana ndi maudindo awo powatumiza ku Malawi School of Government ndi koleji ya Mpemba Staff training.

## 5.4 MAKAMPANI OMWE SIABOMA, MAFAKITALE NDI MALONDA

DPP imakhulupirira kuti mafakitale amphamvu ndi makampani omwe siaboma ndi manthu wa kukula kwa chuma, kupezeka kwa ntchito, kuchulukitsa kwa misonkho yomwe boma limatolera ndi kuchuluka kwa ndalama zakunja zobwera m'dziko lino. Panopa ntchito za mafakitale ndi makampani osakhala a boma zikuvutika chifukwa cha kuonongeka kwa ntchito za mtengatenga (transport system), kusowa kwa luso la ntchito zamalonda, kusowa kwa maluso oyenera ku ntchito zokhuza mafakitale, kusapezeka kwa ndalama zopangira bizinezi, kapena kudula kwa mitengo yopezera ngongole, ndondomeko zoyendetsera chuma zosakhazikika, misonkho yokwera kwambiri, kusakhazikika kwa mphamvu ya magetsi ndi kudula kwa mitengo yopangira bizinezi.

Chotsatira chake nchoti ntchito za mafakitale zikubweretsa ndalama zochepa mu thumba la chuma cha dzikoli (GDP) pamuyeso wa 9.3 peresenti basi. Muyeso umenewu sungathandize kuthetsa umphawi m'dziko lino. DPP ili ndi cholinga chokweza muyeso umenewu kufika pa 15 peresenti mzaka zisanu zikubwerazi. Tidzachita izi pokonza ndondomeko zoti mabizinezi azichitika motakasuka kuti ntchito za makampani omwe siaboma zizikula, malonda ndi maiko akunja apite patsogolo, komanso kuti makampani akhale ndi chidwi chopanga zinthu mwampikisano.

### Kukuza makampani omwe siaboma

Kuchokera m'chaka cha 2025 kufikira chaka cha 2030, DPP idzachita izi:
- Kufufuza kuti iwone zinthu zimene zikulepheretsa kuti chuma chathu chisamayende bwino. DPP idzaikanso zipangizo ndi zoyenereza kuchita malonda.
- Kudzutsa ntchito za mafakitare motsogozedwa ndi ntchito za ulimi wogulitsa zokolola zoti zadutsa m'mafakitare ndi ntchito za migodi mothandizidwa ndi nthambi zosiyanasiyana zogwira ntchito zawo mwaukatswiri.
- Kuika malamulo oyenera, kupititsa patsogolo ntchito za makompyuta ndi njira zina zamakono, kuika anthu odziwa bwino ntchito m'malo oyenera m'mabungwe a boma. Padzakhala chiyembekezo choti anthu amenewa adzakwanitsa kugwiritsa ntchito ndondomeko zabwino

zokopa anthu ndi makampani akunja kapena mommuno kutenga nawo mbali pa chitukuko cha dziko lino.

**Ntchito za mafakitare**

DPP idzachotsa zotchinga zimene zilipo ku ma bizinezi ang'onoang'ono ndi akulu omwe kuti mitundu yonse ya bizinezi itenge nawo gawo pa chitukuko. Choncho DPP idzachita izi:

- Kukhazikitsa malo apadera opangirako malonda omwe akutchedwa Special Economic Zones (SEZs), komwe kudzakhala chilichonse chokhuzana ndi kupanga zinthu zogulitsa mom'muno kapena kunja kwa dziko lino, mmalo awa: Luwinga ku Mzuzu, Magwero ku Lilongwe, Chigumula ndi Matindi ku Blantyre
- Kuika ndalama zotukulira ntchito yopanga magetsi ndi kukuzanso mbali zina zobweretsa mphamvu yogwiritsira ntchito, pambali pa magetsi.
- Kulumikizitsa achinyamata omwe asulidwa ku makoleji a zaumisiri ndi luso kumidzi, ndi anthu ena amene ali ndi maluso ena mu mabizinezi ang'ono, a pakati ndi pakati ndi makampani akuluakulu
- Kukhazikitsa mafakitare m'malo osiyanasiyana owotcherera zitsulo, kuchita ntchito za ukalipentala, ntchito za mawailesi, kusoka zovala, kupanga nsapato, kupanga zikwama, mafuta ndi ntchito zina m'malo monga: Ndirande, Bangwe, Chirimba, Chilomoni, Machinjiri, Mchesi, Chinsapo, Area 23, Area 25, Kauma, Area 36, Matawale, Chikanda, 3 Miles, Mchengautuwa, Luwinga ndi Karonga.
- 
- Kudzutsanso njira zokopera anthu a bizinezi kuti adzatenge nawo mbali pa chitukuko kudzera mu pologalamu ya Malawi Investment Fora m'mene tinaikamo kampeni yotchedwa Takulandirani Tourism Expos pamene DPP inali m'boma. Dziwani kuti kudzera mu kampeni ya Takulandirani Tourism Expos dziko la Malawi linafika pa muyeso wa nambala 3 muno mu Africa. Ndi zomvetsa chisoni kuti pano Malawi salinso pa nambala 3, ayi. Maiko ena anatiposa.
- Kukhazikitsa kampani yaboma yothandiza kubweretsa ndi kukhazikitsa makampani ena omwe siaboma mu madera ofunikira monga kukonza zokolola za kumunda zisanagulitsidwe, migodi, mphamvu zogwiritsira ntchito, mankhwala a mchipatala, ndi zina. Pologalamu imeneyi idzapatsidwa ndalama zosachepera 500 biliyoni kwacha.
- Kukonzanso malo ochitira bizinezi. Kuti izi zitheke tidzatsitsa kukwera kwa mitengo ya zinthu kuti isafike pa 10 peresenti, ndondomeko yobwerekera ndalama zaboma idzakhala pa 12 peresenti, tidzakhala ndi muyeso wosinthira ndalama zakunja wokhazikika, ndipo misonkho yathu idzakhala yabwino kwa onse amene akufuna kutenga nawo mbali ya chitukuko kudzera mu mabizinezi.
- Kupereka chitetezo chokwanira pa ufulu wokhala ndi katundu, komanso kuthetsa mofulumira ndi mwachilungamo mikangano iliyonse yokhuza malonda ndi ogwira ntchito m'makampani.
- Kukhazikitsa ntchito za migodi ya miyala yosowa monga tantalum, zircon ndi nobium amene akupezeka ku mapiri a Kanyika ku Mzimba, ku mapiri a Songwe ku Phalombe, ku Makanjira ku Mangochi, ku Kangankunde ku Balaka, rube ku Chimwazulu ku Ntcheu, grafaiti ku Malingunde ndi rutile ku Kasiya, sodality ndi granaiti ku Ilomba ku Chitipa ndi kutsegulanso mgodi wa Yureniyamu ku Kayelekera ku Karonga.
- Kuika ndalama zosachepera 500 biliyoni kwacha zogwirira ntchito mu kampani ya Malawi Mining Investment Company (MAMICO).
- Kulimbikitsa ndi kukuza ntchito za Development Finance Institutions (DFIs) monga Malawi Agricultural and Industrial Investment Corporation (MAIIC) ndi Export Development Fund (EDF) kuti zikathe kuthandiza kuyamba kwa mabizinezi akuluakulu ndi katundu wogulitsa kunja kwa dziko lino.
- Kukhazikitsa Community Credit Fund (CCF) ndi cholinga choti anthu ambiri akathe kupeza nawo mwayi wa ngongole

wothandizira kuchita mabizinezi ang'onoang'ono ndi mabizinezi a gulu (cooperative societies).

- Kuyambitsa dongosolo lothandiza anthu ogwira ntchito m'makampani a boma amene amabwereketsa ndalama monga MAIIC, CCF and EDF kuti anthu ogwira ntchito m'mabungwewa azikachita mabizinezi.
- Boma la DPP lidzachotsa zotchinga zomwe zikupangitsa kuti anthu opuma pantchito asalandire ndalama zawo mofulumira, ndi kuikanso ndondomeko zothandiza anthu wamba kupanga mafakitare a katundu wosiyanasiyana.
- Kumemeza a Malawi kuti alowe mu mabungwe osungitsako ndalama otchedwa Savings and Credit Cooperatives (SACCOs) ndi kukhazikitsanso ma banki a kumadera amene kukukhala anthu (Community Banks) ndi Cooperative Bank kuti anthuwa azikapeza ndalama zogwirira ntchito za mabizinezi ang'ongoang'ono ndi okulirapo msinkhu, ndi mafakitale.
- Kulimbikitsa ndi kukonzanso ntchito zopangira katundu ndi cholinga choti katundu wopangidwa muno m'Malawi akafikire miyeso yapamwamba imene inaikidwa pa katundu wogulitsa mdziko muno, komanso maiko akunja. Chifukwa cha ichi DPP idzaika ma labotare opimira katundu wopangidwayo ku Mzuzu ndi ku Lilongwe, ndi kukhalanso ndi ma labotare oyendayenda kuti azikatumikira mbali zomwe zili kutali ndi ma labotare a ku Mzuzu ndi Lilongwe.
- Kulimbikitsa a Malawi kuti atenge mbali pantchito za chuma pokhazikitsa mafakitale a kumidzi; ma skimu othandiza ma bizinezi ndi ndalama za ngongole, ndondomeko yoti boma liziwagula katundu ndi ntchito zawo, komanso njira zolumikizitsa mabizinezi osiyanasiyana kuti akhale okhazikika. Mwa ndondomeko ya boma, boma la DPP lidzaunikanso ndi kupanga chiganizo pa katundu wobwera m'dziko muno pamene makampani a mom'muno akupanganso katundu yemweyo. Katundu uyu ndi monga mipando, mabedi, matebulo ndi zinthu zina zopangidwa ndi zitsulo.

**Za malonda**

Boma la DPP lidzachita izi:

- Kukhazikitsa misika yapadera ya zogulitsa zakumunda momwe mudzakhala zipangizo zamakono ndi zothandiza kuti zokolora zakumunda zisaonongeke monga ma firiji ndi mwina mosungiramo katundu mmalo awa: Jenda, Lizulu, Tsangano Turn-off, Bvumbwe, Khwisa ndi Salima.
- Kuthandizira alimi kupeza misika ikuluikulu yogulitsako zokolola zawo kudzera mu mgwirizano wa za malonda mchigawo chino cha Africa monga SADC FTA, COMESA FTA ndi African Continental Free Trade Area (AfCFTA); kugwiritsa ntchito mgwirizano wa boma ndi boma linzake, komanso mwayi wochita mgwirizano ndi maiko otukuka amene amachita malonda paokha, monga Amerika, India ndi China; komanso bungwe lija lalikulu lochita malonda osiyanasiyana lotchedwa World Trade Organization ndi migwirizano ina ya zamalonda.
- Kupereka milozo ku maofesi athu a ukazembe pantchito zawo. Milozo iyi ndi monga kupeza misika ya zinthu zimene timapanga ku Malawi m'maiko amene akuimilira dziko linowo.
- Kudzutsanso mikumano ya anthu ochita malonda (thiredi feya) m'Malawi mom'muno, komanso mkumano wa zogulitsa zakumunda, ndi mkumano wa zamalonda m'chigawo chino cha Africa, ndi mkumano wa ochita za malonda ang'onoang'ono (SMEs).
- Kuyamba kuyendetsa ntchito za malo amodzi a kumalire a dziko lino (one-stop-border posts (OSBP) ku malo atatu amene izi sizinayambe kuchitika chifukwa chosowa zipangizo. Malowa ndi pa Songwe, Muloza ndi Chiponde.

## 5.5 NTCHITO YOKWEZA MALUSO A ANTHU


Whose rights?
What was the
Conflict?
the girl

### 5.5.1 MAPHUNZIRO

Ndondomeko ya Malawi 2063 ikukhumba kuti dziko la Malawi likhale ndi chuma chochokera mu maphunziro, ndi kuti dziko la Malawi likhale ndi anthu ogwira ntchito mwa chidwi komanso pa muyeso wa magwiridwe ntchito a anthu onse pa dziko lapansi. Tikudziwanso kuti Malawi ali ndi achinyamata ochuruka kwambiri, omwe ndi chuma chapamwamba cha dziko lino. Choncho chiwerengero chimenechi nchofunika kuchitukula kudzera mu maphunziro, maluso osiyanasiyana ndi umoyo wabwino kuti achinyamatawa athe kuthandiza kusintha chuma cha dziko lino.

Boma la DPP linaika patsogolo maphunziro ndi maluso kuchokera m'chaka cha 2014 kufika chaka cha 2019, poika ndalama zochuluka mu maphunziro a achinyamata. Koma panopa ndalama zopita ku maphunzirozi zatsitsidwa mpaka muyeso wochepera 20 peresenti m'zaka zisanu zapitazi. Boma la DPP lidzapitiriza ndi pologalamu ya sukulu zaulere ku pulaimale, ndi kuikanso pologalamu ya sukulu za sekondale zaulere. Ndipo ana oyenera kupita m'sukulu zimenezi adzakakamizidwa kukaphunzira m'sukuluzo. Nkhani yoti sukulu za sekondale zikhale zaulere inayamba m'chaka cha 2018 pamene boma la DPP linachotsa ndalama ophunzirira amalipira (tuition fees), ndalama zogwirira ntchito zina ndi zina pasukulu ( general purpose fund) ndi ndalama ya mabuku (text book revolving fund) m'sukulu za sekondale. Choncho boma la DPP lidzakhazikitsa zaka khumi ndi ziwiri (12) za sukulu yaulere m'mene muli zaka zisanu ndi zitatu (8) za pulaimale ndi zaka zinayi (4) za sekondale pofika chaka cha 2030. Izi zidzachitika potsatira mfundo yoti pasakhale mwana wosapita ku sukulu.

**Sukulu za mkomba phala (sukulu za mkaka)**

Kuchokera chaka cha 2025 kufika chaka cha 2030, boma la DPP lidzachita izi:

- Kuphunzitsa ndi kuyembekezera kuti aphunzitsi onse a m'sukulu za mkomba phala akhale ndi ziphatso zophunzitsira monga setifiketi, dipoloma kapena digiri.
- Kulumikiza sukulu ya mkomba phala iliyonse ndi pulaimale sukulu
- Kuika dongosolo loti malipiro a aphunzitsi m'sukulu za mkomba phala azichokera ku khonsolo ya kudera lomwelo

**Maphunziro a sukulu za ku pulaimale**

- Kuyendetsa maphunziro aulere komanso okakamiza ku sukulu za pulaimale molingana ndi malamulo a mu Education Act.
- Kuthetsa malipiro a mtundu uliwonse ku sukulu za pulaimale monga ndalama za chitukuko cha pasukulu, ndi malipiro a chiphatso ndi malipiro ena onse okhuzana ndi kulemba mayeso a boma opangidwa ndi bungwe la Malawi National Examinations Board.
- Kuyambitsa kalasi yokonzekeretsa ana (Preparatory Class) m'sukulu zonse za pulaimale za boma.
- Kumanga sukulu zatsopano, kukuza ndi kukonzanso sukulu zomwe zilipo kale ndi kumanga zipinda zophunzirira zoonjezera.
- Kuika zipangizo zobweretsa madzi ndi kuchita ukhondo msukulu za pulaimale ndi kumanga zipinda zoti atsikana azikasinthiramo zovala
- Kumanga malo oti ophunzira amene ali ndi zovuta zosiyanasiyana (Special Needs) azikaphunziriramo m'zigawo zonse zisanu ndi chimodzi za maphunziro
- Kumanga nyumba za aphunzitsi zomwe angagwiritse ntchito amene ali ndi ulumali kumidzi
- Kuchulukitsa sukulu za pulaimale kumene amadyako phala (school feeding programme) poonetsetsa kuti anthu a

kuderalo akutengako mbali pogwira ntchitoyi.

- Kulimbikitsa maphunziro okomera aliyense ngakhale amene ali ndi ulumali polowetsa maphunziro amenewa mu makoleji ophunzitsira aphunzitsi, komanso kuphunzitsa aphunzitsi ena ukadaulo wa maphunziro a mtundu uwu.
- Kuunika ndi kukonzanso maphunziro a sukulu za pulaimale kuti akathe kukwaniritsa maphunziro ndi maluso amene akufunikira mu nthawi ino, poikamo nzeru ndi maluso a zokonzakonza, zamakono, zamabizinezi ndi maphunziro a anthu onse.
- Kukweza ziphatso zolowera uphunzitsi wa ku pulaimale kufika pa dipuloma. Poonjezera apo boma la DPP lidzapanga kuti maphunziro omwe aphunzitsi amaphunzira ali pantchito (CPD) akhale chinthu chokhazikika.
- Kulemba aphunzitsi ntchito kuphatikizapo onse amene anakhoza mayeso auphunzitsi koma akungokhala, kuyambira a IPTE 14 mpaka IPTE 18. Izi zidzathandiza kuchepetsa chiwerengero chimene ana amaphunzitsidwa ndi mphunzitsi m'modzi.
- Kupereka m'sukulu zathu zipangizo zophunzirira ndi kuphunzitsa zokwanira, monga mabuku a ophunzira ndi mabuku a mphunzitsi, makompyuta ndi zipangizo zomwe ana a maulumali osiyanasiyana amagwiritsa ntchito.
- Kuchulukitsa sukulu zimene zingamagwiritse ntchito ma tabuleti pophunzira. DPP inayesera kale njira imeneyi kudzera m'pologalamu ya Unlocking Talent.
- Kuonetsetsa kuti sukulu zonse zili ndi magetsi ndi lamya wa pakompyuta
- Kukhazikitsa Siteshoni ya kanema wa maphunziro pamwamba pa wailesi ya maphunziro (EBS)
- Kukweza pologalamu ya masewero mu sukulu za pulaimale. Boma la DPP lidzakuzanso ndi kukonza zipangizo za masewero m'sukulu za pulaimale.
- Kuonetstetsa kuti aphunzitsi onse akukopeka ndi ntchito yao, akulipidwa mu nthawi yake, akukhala m'nyumba zabwino, ndipo akupatsidwa chikoka choti agwire ntchito zawo bwino. Poonjezera apo, boma la DPP lidzaika dongosolo la ngongole zopasilana (revolving fund)
- Kuonetsetsa kuti maphunziro akuyenda ndipo ana akuchita bwino polimbikitsa ntchito za ma Insipekitala ndi alangizi a m'sukuluzi ndi kugwira ntchito modalirika m'sukulu za pulaimale.
- Kukweza ntchito za maluso a manja (TEVET) mu sukulu za pulaimale.

**Maphunziro a ku sekondale**

Pofuna kukweza chiwerengero cha ana opita ku sukulu za sekondale pakati pa atsikana ndi anyamata ndi kuonjezera kaso la maphunzirowo, boma la DPP lidzachita izi:

- Kukhazikitsa maphunziro aulere
- Kuunikanso lamulo limene linakhazikitsa maphunziro la Education Act kuti lizikamba za maphunziro aulere komanso okakamiza ku sukulu za sekondale
- Kumanga sukulu za sekondale zatsopano m'madera omwe muli chosowa
- Kuonjezera zipangizo zophunzirira ku sukulu za sekondale za m'madera (Community Day Secondary Schools) ndi kusintha sukuluzi kukhala ngati sukulu zina za boma. Zipangizozi ndi monga zipinda zophunziramo, ma labotare, makompyuta ndi nyumba zowerengeramo ndi kusungamo mabuku.
- Kukhazikitsa sukulu zotsegula kawiri patsiku (Double shift secondary schools ) m'malo amene zikufunikira
- Kukuza sukulu zophunzira ana ali kwao ndi kugwiritsa ntchito intaneti m'sukulu zambiri za sekondale ndi kukonzanso kayendetsedwe ka sukuluzo
- Kukonzanso sukulu za sekondale zonse zakale
- Kuika zipangizo za madzi abwino ndi ukhondo mu sekondale zonse ngakhale za ku madera (community day secondary schools)
- Kuthetsa zotchinga atsikana kuphunzira ku sekondale pomanga nyumba zogonamo pasukulu, kupereka ndalama

za basare kapena kuthandiza atsikana osowa ndi ndalama zoti ziwathandizire pa sukulu, ndi kuletsa zikhalidwe zoipa zonse zimene zimapsyinja atsikana kumidzi

- Kumanga nyumba zabwino za aphunzitsi kwenikweni kumadera a kumudzi
- Kuunika ndi kukonzanso maphunziro a sukulu za pulaimale kuti akathe kukwaniritsa maphunziro ndi maluso amene akufunikira mu nthawi ino, poikamo nzeru ndi maluso a zokonzakonza, zamakono, zamabizinezi ndi maphunziro a anthu onse.
- Kukweza ntchito za maluso a manja (tevet) mu sukulu za sekondale zonse ngakhalenso kusukulu za ku madera zoyendera (Community Day Schools).
- Kuphunzitsa ndi kulemba ntchito aphunzitsi a ku sekondale ambiri
- Kupereka m'sukulu zathu zipangizo zophunzirira ndi kuphunzitsa zokwanira, monga mabuku a ophunzira ndi mabuku a mphunzitsi, makompyuta ndi zipangizo zomwe ana a maulumali osiyanasiyana amagwiritsa ntchito.
- Kulimbikitsa ntchito zoyendera ndi kulangiza aphunzitsi m'sukulu zonse
- Kuonetsetsa kuti sukulu zonse zili ndi madesiki ndipo palibe mwana wokhala pansi m'kalasi.
- Kuonetsetsa kuti sukulu iliyonse ili ndi magetsi
- Kuonetsetsa kuti sukulu iliyonse ili ndi intaneti
- Kumanga ma labotare a zinthu zokhuza makina ndi makompyuta mu sukulu zoyendera kumadera (Community Day Secondary Schools)
- Kuika maphunziro onse a ku sekondale pa kompyuta
- Kulimbikitsa maphunziro a sayansi, masamu ndi za makina (STEM) pokulitsa ma labotare a sayansi kuphunzira pa kompyuta ndi zina zotero
- Kuchotsa malipiro a mayeso a JCE ndi MSCE
- Kuonetsetsa kuti masewero m'sukulu zonse za sekondale akupita patsogolo poonjezera zipangizo zosewerera, ndi kukonza mabwalo ndi zipangizo zina zosewerera.

**Maphunziro a ku sukulu za ukachenjede**

- Kukuza zipangizo zogwiritsa ntchito m'sukulu za ukachenjede poika malo okwanira ophunzirira, maofesi ndi malo ogona ana asukulu.
- Kuonetsetsa kuti sukulu zonse zaukachenjede zili ndi zipangizo zapamwamba zophunzirira kapena kuphunzitsira ndi kuchitira kafukufuku, zolingana ndi zipangizo zimene ophunzirawo akakumane nazo kumafakitale akatsiriza sukulu yao
- Kukuza maphunziro ochita kuyendera ndi kuphunzira pa kompyuta m'sukulu za boma ndi zomwe sizaboma
- Kukhazikitsa Open University of Malawi
- Kuonetsetsa kuti ophunzira onse akupindula ndi ngongole kapena ndalama zowathandiza, ndi kuthandizanso ophunzira amene akupanga maphunziro a dipuloma ndi maphunziro a pakompyuta (Open Distance and e-Learning)
- Kumaliza kumanga sukulu ya ukachenjede ya Inkosi ya Makhosi Mmbelwa University imene boma la DPP inayamba kumanga, koma boma la Kongeresi linasiya kugwira ntchitoyi.
- Kuonjezera malo ogona ophunzira mu sukulu za ukachenjede potsatira pologalamu ya Public Private Partnerships
- Kuonjezera chiwerengero cha ophunzira amene ali ndi maulumali osiyanasiyana. Sukulu iliyonse idzakhala ndi zipangizo zoyenera ophunzira otero, ndi kuika chipinda chapadera momwe mudzaikidwe zipangizo zamakono
- Kuonetsetsa kuti sukulu za ukachenjede zikutsata ndondomeko zoyenera zimene zinaikidwa ndi bungwe loona za ndondomeko
- Kuyendetsa ndondomeko za Malawi Qualifications Framework
- Kuunikanso maphunziro a kusukulu za ukachenjede ncholinga choti akafikire zosowa ku mafakitale a makono, ndi kukwaniritsa zokhumba za dziko zimene zinaikidwa mu Ndondomeko ya Malawi 2063 ndi maluso amene adzafunike


MALAWI UNIVERSITY OF SCIENCE AND TECHNOLOGY



m'zaka makumi atatu zikubwerazi
- Kulimbikitsa kalembera ndi kutsimikizika (Registration and Accreditation) wa sukulu zonse za ukachenjede zoyendetsedwa ndi boma ngakhale anthu wamba
- Pofuna kukweza ukadaulo wa anthu pantchito za sayansi ndi makina ndi kuchita zinthu zachilendo, boma la DPP lidzakuza malo opangirapo bizinezi, ntchito zachilendo, ndi ntchito za makina m'sukulu zonse za ukachenjede. Poonjezera apo, boma lathu lidzaphunzitsa ndi kuwalimbikitsa anthu a zasayansi, ochita za makina ndi makompyuta, ndi anthu ochita zachilendo, ndi mabizinezi. Izi zidzathandiza kuti nthambi yoona ntchito zaboma (public service) mukhale anthu odziwa ntchito komanso ogwira ntchitoyo bwino.
- Kukweza kafukufuku ndi chitukuko poonetsetsa kuti thumba la National Research Fund limene boma la DPP linakhazikitsa mwaikidwa ndalama zokwanira kugwira ntchito imeneyi.
- Boma la DPP lidzaonetsetsa kuti mapologalamu a m'sukulu za ukachenjede ndi otha kuthandiza pa zosowa zam'mafakitale athu ndi chuma cha dziko lino. Choncho DPP idzaonetsetsa kuti pali kulumikizana pakati pa sukulu za ukachenjede ndi mafakitale, zomwe zidzapangitse kuti mafakitale ndi malo ena opanga zinthu akhale odalilika.

**Maphunziro a aphunzitsi ndi zoonjezera nzeru zina**

DPP ikudziwa kuti mtundu wabwino wa maphunziro umatengera mtundu wabwino wa aphunzitsi. Pachifukwa cha ichi boma la DPP lidzatsogoza maphunziro, kulemba ntchito ndi kutumiza aphunzitsiwo ku madera okagwira ntchito. Mwachindunji, boma la DPP lidzachita izi:
- Kuonetsetsa kuti makoleji ophunzitsira aphunzitsi ndi odzadza ndi ophunzira molingana ndi muyeso wa koleji
- Kukhazikitsa maphunziro a dipuloma ndi digiri kwa aphunzitsi ophunzitsa ku pulaimale.
- Kumanga Instituti yapadera yophunzitsirako aphunzitsi oona za maphunziro a ana amene ali ndi maulumali osiyanasiyana (Special Needs Institute); ndi kukhala ndi pologalamu m'mene muli kabukhu (Module) kophunzitsira za special needs m'makoleji onse a uphunzitsi.
- Kukhazikitsa ndondomeko ya maphunziro omwe aphunzitsi amaphunzirabe akugwira ntchito zawo (Continuing Professional Development Framework), ngati chinthu chokhazikika kwa aphunzitsi onse.
- Kuthandiza aphunzitsi athu kukagwira ntchito maiko a kunja.

**Makoleji a umisiri ndi maluso a kumadera**

Mu zaka za 2014 mpaka 2019 boma la DPP linakhazikitsa makoleji oti achinyamata azikaphunzirako ntchito zamanja ndi maluso ena m'maboma ndi ma konsitichuwense onse m'Malawi muno poona kuchuluka kwa ulova ndi kusowa kwa maluso pakati pa achinyamata. Pologalamu imeneyi imapereka mwayi kwa achinyamatawa kuti akathe kupeza ntchito kapena kulemba achinyamata enanso ntchito. Ndi zomvetsa chisoni kwambiri kuti boma la Kongeresi silinathandize kuti makolejiwa apitirize kugwira ntchito zawo. Chifukwa cha ichi, boma la DPP lidzachita izi pakati pa 2025 ndi 2030:
- Kuonjezera thandizo lopita ku sukulu zaumisiri ndi maluso za TEVET, ndi kumanga makoleji ena m'madera onse a a phungu m'dziko lino.
- Kumanga koleji yophunzitsira aphunzitsi omwe amaphunzitsa mu makoleji amenewa (Technical Teachers Training College) ndi cholinga choti aphunzitsi a TEVET akhale odziwa bwino ntchito zawo.
- Kuthandiza ophunzira amene atsiriza maphunziro a TEVET kukhala ndi ndalama zoyambira ma bizinezi
- Kuika zipangizo zamakono zophunzitsira ndi kuphunzirira m'makoleji a ntchito zamanja
- Kuthetsa kusalumikizana kwa maluso a anthu amene akuphunzitsidwa m'makolejiwa ndi maluso amene akufunikira ku mafakitale

- Kuika zonse zokhuza ntchito zamanja ndi maluso mu Unduna umodzi

**Maphunziro a msukulu za achikulire**

Kuchokera 2025 kufika 2030 ndi kupyola apo, boma la DPP lidzaonetsetsa kuti pali ndondomeko zabwino zothetsera kusadziwa kulemba ndi kuwerenga pakati a Malawi, pochita izi:

- Kumanga malo ophunzirapo anthu achikulire omwe sanapite kusukulu, ndi kulembetsa ophunzira okwana 500,000 pachaka
- Kulemba ntchito aphunzitsi a m'sukulu zimenezi ndi kuona kuti akulipidwa malipiro osachepera pa muyeso wa boma wa minimum wage.
- Kuphunzitsa aphunzitsi a m'sukulu zimenezi pa maphunziro okhuza ntchitoyi nthawi ndi nthawi
- Kulemba anthu ntchito mu maudindo onse amene mulibe anthu ogwira ntchito kuti pakhale kugwira bwino kwa ntchito ndi kulumikizana pakati pa maofesi oona za ntchitoyi
- Kuunikanso maphunziro a anthu achikulire ndi cholinga choti maphunzirowa azigwirizana ndi maluso amene akufunika ku mafakitale ndi kwina kotero.
- Fuko losaphunzira silingathe kuthandiza pantchito zokweza chuma cha dziko lawo mofulumira. Mzaka zisanu zapitazi, chiwerengero cha ana ndi achikulire osadziwa kulemba ndi kuwerenga chakula pomwe chiwerengero cha anthu oyamba sukulu za kwacha chakhala chochepa, poyerekeza ndi mlozo umene unaikidwa mu malamulo.

## 5.5.2 UMOYO, KADYEDWE NDI UKHONDO

DPP ikudziwa kuti umoyo wabwino wa anthu umapangitsa kuti dziko liziyenda bwino pa chuma ndi chitukuko. Choncho umoyo wabwino wa dziko ndi wofunika kuti tikwaniritse masomphenya a Malawi 2063. Tikudziwa kuti zinthu zina zimene zimabweretsa matenda kapena imfa pakati pa anthu nthawi yao isanakwane ndi zotha kupeweka. DPP idzagwira ntchito yothana ndi zinthu zimene zimabweretsa matenda ndi imfa za chonchi.

**Umoyo wabwino kwa onse**

Tikudziwa kuti maiko ndi mabunngwe otithandiza pantchito za umoyo ayamba kutopa. Choncho pofuna kupitiriza ntchito zabwino zimene tinayamba kale kuchita, boma la DPP lidzachita izi:

- Tidzaika ndalama zokwanira mu ntchito zopewa matenda
- Tidzakokomeza ndondomeko ya zaumoyo kwa aliyense "Health in all policies" mu ndondomeko zathu zonse zoyendetsera dziko
- Tidzalimbikitsa kagwiritsidwe ntchito kabwino ka ndalama potumikira anthu pa ntchito zaumoyo
- Kuonetsetsa kuti palibe kuonongeka kwa ndalama ndi zinthu zina pogula ndi kugwiritsa ntchito katundu
- Kuonetsetsa kuti a Malawi onse ali ndi chiphatso cha unzika kuti boma lizidziwa anthu ake bwino
- Kuonetsetsa kuti onse ogwira ntchito m'zipatala ndi mbali zina zokhuza umoyo wa anthu ndi ophunzira bwino ndi a maluso ndi cholinga choti anthu atumikiridwe bwino pankhani zaumoyo.
- Kulimbikitsa ndi kukhazikitsa mfundo ya "One Health agenda," imene imalumikiza mbali zitatu zaumoyo monga umoyo wa anthu, umoyo wa nyama ndi umoyo wa chilengedwe mdera limene anthu ali, pakupewa ndi kuyendetsa bwino ntchito zopewa matenda. Izi zidzachitika m'madera amene anthu akukhala ndi m'sukulu zosiyanasiyana. DPP ikudziwa za kulumikizana kwa zinthu zimenezi popewa ndi kuyendetsa nkhani zokhuza matenda monga kutupikana, kolera ndi matenda ena ambiri.

**Malamulo ndi ulamuliro**

Boma la DPP lidzachita izi:

- Kuunikanso ndi kutsirizitsa malamulo a zaumoyo monga Public Health Act of 1948 ndi Food and Nutrition Bill.
- Kutsirizitsa ntchito yokhazikitsa malo oona zaumoyo wa anthu otchedwa Public Health Institute of Malawi (PHIM)
- Kupanga zoti zipatala zazikulu m'dziko muno zikhale zoima paokha (Central Hospital Autonomy)
- Kuonetsetsa kuti ntchito zaumoyo wa anthu zili m'manja mwa makhonsolo
- Kulimbikitsa pologalamu yokhala ndi Ofesi yoona za madandaulo a anthu (Hospital Ombudsman)
- Kulimbikitsa makomiti olangiza zaumoyo (Health Centre Advisory Committees)
- Kulimbikitsa ntchito zaumoyo poika ndalama ndi ogwira ntchito okwanira, komanso zipangizo zoyenera ndi zokwanira, ndi cholinga choti ntchitozi ziziyenda bwino
- Kukhazikitsa ndi kulimbikitsa ubale wabwino pakati pa dziko lino ndi maiko ndi mabungwe amene amatithandiza pantchito zaumoyo.

**Umoyo ndi kusintha kwa nyengo**

DPP imadziwa kuopsa kwa kusintha kwa nyengo pa umoyo wa anthu. Kuyambira 2025 kufika 2030 boma la DPP lidzachita izi, mwa zinthu zina:

- Kutumiza akatswiri odziwa za chilengedwe m'makhonsolo onse kukachita kafukufuku wokhuzana ndi kuopsa kwa kusintha kwa nyengo m'madera amenewo ndi kupeza njira zothandiza kuchepetsa mavuto amene amadza chifukwa cha kusintha kwa nyengo kumudzi komanso kutauni
- Kuika ndalama mu mphamvu ya chilengedwe ngati mbali imodzi ya pologalamu ya "Power to Healthcare" mzipatala za dziko lino.  DPP idzakhazikitsa mphamvu ya magetsi ku theka la zipatala kumene kulibe magetsi.




LOCATION
Strengthening Primary Health Care in Cyclone Freddy affected districts
OBJECTIVE
To reduce morbidities and mortalities of Children in tropical Cyclone Freddy affected districts
INTERVENTIONS
•Integrated mobile clinics
•Procurement of buffer drugs
•Hygiene promotion
STRATEGY
Implemented through government stakeholders and community structures in target districts
OUTPUT

- Kuonetsetsa kuti ndondomeko zabwino ndi zovomerezeka zikutsatidwa pa nkhani ya madzi okumwa
- Kuonetsetsa kuti zonyansa zochokera m'matauni ndi makhonsolo zikutayidwa malo oyenerera mu njira zoyeneranso
- Kupereka madzi okumwa abwino ndi zipangizo zabwino ku zipatala zonse

**Malo ogwira ntchito aukhondo ndi otetezeka**

Pa zaumoyo wa pamalo ogwira ntchito, DPP idzachita izi:

- Kukwaniritsa ndondomeko ndi mapulani abwino othandiza pantchito yolimbikitsa umoyo wabwino pa malo ogwirira ntchito molingana ndi malamulo a kagwiridwe kantchito
- Kuonjezera ntchito zimene zinayambika kale zokhuzana ndi umoyo wa pamalo antchito kuti malo ogwirapo ntchito akhale aumoyo wabwino, komanso osachititsa ngozi
- Kukonzekeretsa ogwira ntchito kuti azikhala odzidalira ndi kudziwa chochita pamalo ogwira ntchito pakapezeka chiopsezo cha umoyo mwadzidzidzi kudzera mu ngozi kapena kubuka kwa nthenda
- Kulimbikitsa njira zopewera nthenda zopatsirana [Infection Prevention and Control (IPC)] m'zipatala, kudzera mu njira zosiyanasiyana za umoyo wapantchito

**Kumanga fuko lathanzi**

Boma la DPP lidzachita izi:

- Kuika ndondomeko zokhuza umoyo mu mapologalamu ndi mapulani oyendetsera ntchito zam'mizinda ndi matauni, kuti pakhale kulumikizana kwa nkhani zaumoyo wa anthu ndi ntchito zina zonse zokhuza miyoyo ya anthu
- Kuika patsogolo njira zamayendedwe abwino m'matauni ndi kuzionetsa izi mu ma pulani a tauni kapena mzinda
- Kukonza bwino njira zomwe oyenda pansi kapena opalasa njinga a misinkhu yonse akhoza kugwiritsa ntchito m'mizinda ndi m'matauni
- Kukhazikitsa malo osapereka chiopsezo kwa anthu oti akhoza kugwiritsa ntchito poyenda, kukwera njinga, kuona chilengedwe, kusewera, ndi cholinga choti anthu akakhale a moyo wabwino komanso nthawi yomweyo akuchepetsa kugwiritsa ntchito kwa mphamvu yochokera m'mafuta a petulo kapena dizilo ndi zinthu zina
- Kukweza ndi kukuza malo a poyera a chilengedwe (public and green open spaces) amene anthu a misinkhu yonse angamagwiritse ntchito pocheza, kusewera, kupumula ndi zina zotero m'mizinda ndi m'matauni

**Kulimbitsa kukhala kwa umoyo wabwino ndi chisamaliro chopewa**

Ife tidzachita izi:

- Kukuza chidziwitso cha anthu pa zinthu ndi chikhalidwe zimene zimathandiza anthu kukhala ndi umoyo wabwino monga, kadyedwe kabwino, machitachita olimbitsa thupi, ndi makhalidwe ena. Tidzaphunzitsanso anthu njira zopewera matenda opatsirana ndi osapatsirana
- Kuonetsetsa kuti anthu onse m'madera amene akukhala akudziwa malamulo a mowa ndi mankhwala ozunguza bongo
- Kuonjezera kupezeka kwa chithandizo kwa anthu amene akhuzidwa ndi matenda okhuza umoyo wa m'malingaliro (mental health) kuyambira ku dera limene anthu amakhala mpaka ku malo ndi zipatala zina
- Poonjezera apo tidzaonetsetsa kuti takweza mulingo wothandiza anthu kupeza chithandizo cha malo amene angathe kupeza chithandizo

**Kumvetsa zosowa za anthu pa zaumoyo**

Boma la DPP lidzachita izi:

- Kugwiritsa ntchito miyeso ya dziko lapansi pofuna kudziwa mavuto amene tili nawo pa zaumoyo ndi njira zothetsera mavutowo
- Kuika ndondomeko zoonetsa poyera zosowa za anthu pa zaumoyo ndi njira zofalitsira mauthengawo
- Kuika ndalama zokwanira mu kafukufuku wa zaumoyo. Khonsolo iliyonse ya boma idzauzidwa kuika ndalama zosachepera 2 peresenti ya ndalama zogwirira ntchito zawo (ORT), pantchito ya kafukufuku wa zaumoyo ndi cholinga choti ziganizo zimene zikuchitika zikhale zochokera pa umboni wa kafukufuku ameneyi

**Kupereka chithandizo cha chipatala kwa anthu**

Boma la DPP lidzachita izi:

- Kukhazikitsa ndalama zapadera zothandizira ntchito za umoyo
- Kulimbikitsa kuti ndalama za mu dera la phungu (CDF) zikhale zothandizira ntchito za umoyo monga kugulira galimoto zokwera odwala (ambulansi) ndi kukonzera zipatala zazing'ono
- Kulimbikitsa mgwirizano (Service Level Agreement) ndi Christian Health Association of Malawi, Islamic Health Association of Malawi ndi makampani omwe siaboma
- Kudzera mu ndondomeko yokhuza a Malawi okhala kunja kwa dziko lino, boma la DPP lidzaitana ndi kulimbiktsa madokotala, anamwino, ndi akatswiri ena a zaumoyo kubwera ku Malawi ndi kuikiza chuma ndi maluso awo mu ntchito zaumoyo
- Kutukula ntchito za mankhwala a zitsamba kuchokera ku kafukufuku ndi kakonzedwe ka mankhwalawo
- Kukhazikitsa dongosolo loti dziko lizitumiza ogwira ntchito m'zipatala za maiko akunja
- Kuchita mgwirizano wa PPP mu madera a Digital Health, Medical Waste Disposal, Diagnostic Services (Laboratory and Radiology etc), ndi kumanga nyumba za ogwira ntchito zaumoyo m'madera osiyanasiyana a dziko lino
- Kuika ndondomeko zoti dziko la Malawi likhale limodzi mwa maiko omwe anthu akhoza kumabwerako pofuna chithandizo cha mankhwala (Medical Tourism), kwenikweni m'madera awa:
  - Za nthenda ya khansa (kufufuza ndi kuchiza)
  - Kupanga kwa mankhwala
  - Za nthenda ya mtima
  - Za matenda a maso
  - Za matenda a mu ubongo
  - Za kuthyoka kwa mafupa
  - Zokhuza chikhodzodzo (Renal and urology services)
  - Ndi ukadaulo wina wotero
- Kukhazikitsa njira zachilendo ndi zamakompyuta ndi makina pothandiza anthu pa nkhani zaumoyo
- Kukweza kapezekedwe ka mankhwala m'malo onse operekera chithandizo cha zaumoyo
- Kulimbitsa ntchito za bungwe loona za mankhwala la Pharmacy Medicine Regulatory Authority ndi mabungwe ena kuti khalidwe lakuba mankhwala m'zipatala za boma lithe, ndi kuonetsetsa kuti m'zipatalamo muli mankhwala okwanira

**Zipatala zomwe zimangidwe**

Zipatala zonse zatsopano (kwenikweni za kumidzi) zidzakhala ndi nyumba za ogwira ntchito, madzi ndi magetsi. Boma la DPP lidzachita izi:

- Kumanga zipatala kumadera amene kuli anthu ambiri monga ku Blantyre (Chilomoni, Bangwe, Mpemba, Limbe, Ndirande ndi madera ena), Lilongwe (Nathenje, Kawale, Area 25, Area 18, Mtsiriza/Mtandire, ndi madera ena), Zomba, ndi Mzuzu.
- Kumanga chipatala chatsopano cha pa Chikwawa ndi Dowa,

- Kumanga zipatala za kudera monga ku Ntaja, Thekerani, Chapananga, Jenda, Malomo, Chambe, Chitekesa, Nyungwe, Nthalire, Kameme, Makhuwira, Bwanje, Luchenza, Usisya ndi Bua,
- Kumanga zipatala zazing'ono (health centres) zokwana 229 m'dziko lonse (health centre imodzi pa dera la phungu lirilonse).
- Kumanga nyumba 458 za ogwira ntchito zaumoyo m'Malawi monse.
- Kukonza kapena kupereka galimoto yonyamula odwala pa chipatala chaching'ono chilichonse
- Kugula zipangizo za ntchito ya chipatala monga makina osungira mpweya (Oxygen plant) m'zipatala za Zomba Central, Mangochi District, Kasungu District ndi Chikwawa District.
- Pofuna kuthana ndi mavuto amene amapangitsa anthu kupempha boma kuti liwatumize ku zipatala zakunja, tidzamanga chipatala cha makono cha khansa, nthenda ya mtima, chipatala chokhuza mafupa, chokhuza maso ndi nthenda zina.
- Kumanga zipinda zothandizira anthu amene ali ndi mavuto okhuza malingaliro (Mental Health Units) ku QECH ndi ku KCH kuti anthu ambiri athe kupeza chithandizo pa matenda amenewa
- Kukhazikitsa ntchito zothandiza anthu pakagwa ngozi kapena matenda a dzidzidzi (Emergency Medical Services, Ambulance services) pakati panseu wa Lilongwe ndi Mzuzu, komanso nseu wa Blantyre mpaka Mangochi.
- Kukweza ntchito za Malawi Blood Transfusion Service kuti magazi ndi zina zofunikira zizikhalapo nthawi zonse
- Kuphunzitsa ndi kupereka ma satifiketi kwa anthu amene amathandiza pankhani zangozi mothandizana ndi bungwe la Red Cross Society

**Kulimbikitsa gulu logwira ntchito zaumoyo**

Boma la DPP lidzachita izi:

- Kuonetsetsa kuti mfundo za utsogoleri wabwino ndi kugwira ntchito mokhulupirika m'madera onse a ntchito zaumoyo zakhazikitsidwa m'zipatala monse, ndi kuthetsa kagwiridwe ka ntchito kosalumikizana pakati pa anthu ogwira ntchito zaumoyo
- Kukhazikitsa ndondomeko yotumiza ogwira ntchito zaumoyo athu ena ku maiko akunja pamene tikulandira akatswiri akunjanso, pogwiritsa ntchito mgwirizano umene uli mu ndondomeko ya a Malawi okhala kunja kwa dziko lino (Diaspora policy)
- Kuika ndalama zokwanira mu maphunziro ndi kulemba anthu ntchito
- Kumangira nyumba anthu ogwira ntchito zaumoyo kwenikweni kumidzi motere: nyumba ziwiri pa health post, nyumba 15 pa health centre, ndi nyumba 70 pa chipatala cha paboma (district hospital)
- Kuika ndalama zokwanira kugula zipangizo za chipatala ndi zina zokonzera zipangizozo ndi cholinga chotukula ntchito zaumoyo.

**Kugwiritsa ntchito makina pa ntchito zaumoyo**

Ife tidzachita izi:

- Tidzakhazikitsa ndondomeko zoti zipatala zathu zizigwiritsa ntchito makina a makono ndi cholinga choti pazichitika changu potumikira anthu
- Kukonza ndi kugwiritsa ntchito ndege zing'onozing'ono zopanda woyendetsa (drone) potumiza mankhwala ndi chithandizo china ku malo akumidzi
- Kuika m'malo dongosolo loti chilichonse chokhuza umoyo wa anthu chizidziwika pa makompyuta ndi kumawauza anthu zimene zikuoneka pa dashboard ya chipinda chounikira m'mene zinthu ziliri (Health Situation Room)
- Kuonjezera chiwerengero cha anthu amene mbiri ya umoyo

wao ili pa kompyuta
- Kukonza bwino kagwiritsidwe ka mbiri ya zaumoyo kuti ikathandize kupanga chiganizo choyenera monga kaperekedwe ka ndalama zogwirira ntchito ndi zinthu zofunika kuika patsogolo

**Ubale ndi kugwira ntchito mothandizana**
- Boma la DPP lidzachita izi:
- Kukhazikitsa mapolojeketi oyesera pogwira ntchito ndi anthu ena ndi cholinga chofuna kuona kumene kukufunika kuikako ntchito zaumoyo mofulumira, kusiyana ndi madera ena
- Kukhazikitsa ndi kuona njira zimene tingachite pothandiza malo amene akufunikira kutumikiridwa ndi kuonetsetsa kuti pali kugwira ntchito limodzi ndi onse amene akugwira ntchito zaumoyo m'deralo
- Kulimbikitsa mgwirizano wa maiko a m'chigawo chimodzi pankhani ya kafukufuku ndi chitukuko cha ntchito zaumoyo

**Kupewa kuononga kwa chisamaliro cha umoyo ndi kupititsa patsogolo changu ndi ukadaulo**

- Kulimbikitsa kugwiritsa ntchito chiphatso cha unzika m'zipatala ndi malo ena olandirako thandizo la zaumoyo
- Kuonetsetsa kuti pali kusintha kwa kagwiridwe ka ntchito zaumoyo monga izi: kugwira ntchito mwaluso, modziwa ntchitoyo, kudziwa malire a ntchitoyo, kuti wodwala asakhale pa chiopsezo, komanso kutumiza wodwala ku chipatala chachikulu moyenera ndi mofulumira (Human Resources for Health optimization). Mwa zina, padzafunika kulemba akatswiri odziwa za Family Medicine, Obstetrics ndi Gynecology, Pediatrics, Surgery ndi Internal Medicine m'zipatala za m'maboma pang'onopang'ono
- Kumanga zipatala mu madera a kutauni (Urban Community Hospitals)
- Kulimbikitsa chisamaliro cha odwala pa nthawi yonse imene akudwalayo
- Kuunika ndi kupeza mwayi woti tichite bwino pothandiza anthu pankhani zaumoyo
- Kugwiritsa ntchito mapulani a boma a inshuransi yaumoyo mu kayendetsedwe kathu ka zaumoyo
- Kubweretsa National Health Insurance m'Malawi muno potsatira ndondomeko zake
- Kuonetsetsa kuti mankhwala ndi zipangizo za chipatala zathu ndizosapereka chiopsyezo kwa odwala kapena dokotala, ndipo kuti zikugawidwa ndi kugwiritsidwa ntchito bwino

**Kadyedwe ndi umoyo**

Kusakwanira kwa chakudya lakhala vuto la chaka ndi chaka kuno ku Malawi. Choncho boma la DPP lidzaika chidwi pa izi:
- Kusintha kwa chikhalidwe pakati pa anthu pa zakudya
- Kulimbikitsa anthu kuti azidya zakudya zosiyanasiyana m'malo mongodya nsima ndi mpunga. Zakudya ngati nthochi, mbatata ya kholowa, chinangwa, mapira, mbatata ya kachewere ndi zina ndi zakudya zabwino.
- Kupanga mafuta ophikira kuchokera ku mpendadzuwa, soya, ndi mtedza
- Kukwera kwa mitengo ya zinthu zopangira ulimi, ndi kuikaponso zipangizo za ulimi wa mbeu zina osati chimanga chokha
- Kusintha kwa nyengo ndi mavuto amene amabwera chifukwa cha ichi, ndi kuyesa mtundu wina wa ulimi monga kuweta akalulu, mbira, nsomba, nkhuku ndi mazira. Boma la DPP limadziwa kuti anthu saweta zoweta zikuluzikulu monga ng'ombe kapena mbuzi kuti azidya pakhomo, koma kugulitsa kapena kufuna kuonetsa kuti munthu ali ndi chuma. Choncho mpofunika kuchita ulimi wa nyama zimene tatchulazi kuti anthu azidya m'makomo. Koma ziweto zikuluzikuluzi ngati ng'ombe zikhoza kupereka mkaka womwe anthu pakhomo

akhoza kumwa.
- Kusintha kwa nyengo kumene kumakhoza kubweretsa matenda monga kolera ndi schistosomiasis zimene zikhoza kuononga ntchito zokopa alendo

Tidzaika madyedwe mu ntchito zoteteza anthu ku umphawi monga ndalama zopereka kwa anthu' ndi ntchito zokonza miseu ndi zina zotero' ndi cholinga choti miyoyo ya anthu itukuke. Poonjezera apo tidzaika nkhani za madyedwe mu mapologalamu a kusintha kwa nyengo poonetsetsa kuti amayi akupatsidwa mphamvu, ndiponso mitengo ya zipatso ikudzalidwa ndipo malo otungirako madzi ndi otetezedwa.

### 5.5.3 ACHINYAMATA NDI MASEWERO

Achinyamata m'dziko muno ali pa muyeso wa 70 peresenti ya chiwerengero cha dziko. Choncho achinyamatawa ndi amene angathe kuyendetsa ndondomeko ya Malawi 2063. Koma pa zaka zisanu zimene zapitazi taona ntchito zimene zikanakhoza kutukula miyoyo ya achinyamata zisakusamalidwa. Ntchito zimene zikanatukula achinyamata komanso kuti athandize pa chitukuko cha dziko lino zinali zokhuza kulembedwa ntchito, kukhala ndi ndalama, kutukula kwa maluso, za masewero, za kayendetsedwe bwino ka mabungwe, za makina ndi makompyuta ndi kusasalana.

Chifukwa cha kukwera kwa umphawi ana osachepera 15,000 akuyenda miseu ya Lilongwe, Blantyre, Mzuzu ndi Zomba ngati amasikini. Ana amenewa amakhala panseu ndi kumachita zinthu zaumbanda ndi cholinga choti apeze thandizo. Mapeto ake anthu ambiri akuyenda mwa mantha m'matauni athu. Ambiri mwa anawa ndi oti anasiyira sukulu panjira, ndipo sanatsirize sukulu za pulaimale.

Chipani cha DPP ndi chokonzeka kukonza mavuto amenewa pokhazikitsa tsogolo labwino kwa achinyamata. Boma lathu lidzapereka mphamvu kwa achinyamata kuti akhale atsogoleri ochitachita pokonza madera awo ndi dziko lawo. Pofuna kuonetsa kuti chipani cha DPP chimadziwa kufunika kwa achinyamata, tidzaphatikiza unduna wa achinyamata, masewero ndi Unduna wa zantchito kukhala Unduna wa ntchito, achinyamata, masewero ndi ntchito za manja.

Tikulonjeza kudzachita zinthu izi pakati pa 2025 ndi 2030:

- Kupereka mphamvu kwa achinyamata pa zachuma ndi zaluso
- Kudzutsa ndi kukuza makoleji a zaumisiri ndi maluso a m'madera (Community Technical Colleges) pophunzitsa achinyamata maluso omwe angawathandize kupeza ntchito kapena kupanga ndalama paokha monga ulimi, za makina ndi makompyuta, mafakitale, ndi bizinezi ndi kuwalumikizitsa ku ntchito kapena mwayi wa mabizinezi.
- Kukhazikitsa Youth Enterprise Fund imene izidzapereka 100 miliyoni kwacha chaka chilichonse ku dera la phungu pa chiongola dzanja chotsika pa ngongolezo, kwa achinyamata amene atsiriza maphunziro awo ku ma koleji aumisiri a m'madera.
- Tidzakweza ndi kubweretsa maphunziro a makono olingana ndi mfundo zimene zili mu Ndondomeko ya Malawi 2063 ndi zofunika pa msika wa malonda, ndipo nthawi yomweyo tidzakhalanso tikuwapatsa mpamba wa zipangizo ndi upangiri/malangizo oyenera.
- Tidzakhazikitsa malo osiyanasiyana opangirako ntchito zokopa anthu ndi cholinga chofuna kupititsa mtsogolo ntchito zokopa anthu m'Malawi muno, kubweretsa mwayi wa ntchito ndi kukhazikitsa magulu a achinyamata olimbikitsa zokopa anthu mdera lirilonse la phungu.
- Tidzaphunzitsa ana oyendayenda m'miseu ndi achinyamata amene anasiyira sukulu za pulaimale panjira, ntchito zaumisiri ndi kuchita malonda kuti azipeza ndalama zothandiza pa

miyoyo yao.

**Kukweza za masewero ndi malo ochezera**

- Kuika ndalama zokwana 12 biliyoni kwacha mu thumba lokhuza masewero (Sports Development Fund) ndipo dera lirilonse la phungu lidzapatsidwa ndalama zokwana 50 miliyoni kwacha pa chaka.
- Kutsiriza mapolojeketi awiri a Griffin Saenda Sports Complex ndi Malawi Aquatic Centre
- Kuika malo a achinyamata (youth centres) mu maboma onse a dziko lino okhala ndi zipangizo za masewero ndi kucheza, malo owerengera kapena kusungira mabuku ndi makompyuta ndi makina.
- Kupitiriza ntchito yomanga mabwalo a mpira m'maboma ndi kumanga mabwalo aakulu a zamasewero ku Blantyre ndi Mzuzu.
- Kuika ndalama mu sukulu za masewero ndi kulemba ntchito osewera akale kuti aziyang'anira malo amenewo ndi cholinga choti azikathandiza kuona achinyamata amene ali ndi maluso mosavuta.
- Kuika ndalama mu bajeti yaboma zotukulira masewero a mpira wa miyendo ndi wa manja
- Kutsirizitsa kumanga ma bwalo a mpira a makalabu a Bullets ndi Wanderers.
- Kuonanso ndondomeko yoyendetsera masewero m'dziko muno ndi kumayamikira makampani amene akuthandiza chitukuko cha masewero m'dziko lino.
- Kuyambiranso masewero a mpira wa ku pulaimale ndi kusekondale kuti tikalimbikitse luntha la ana asukulu

**Ntchito zamanja ndi zachilendo**

- Kuteteza ntchito zaluso kudzera mu lamulo la umwini wa ntchito yaluso (patent ndi copyright)
- Kukonza mipikisano ya zisudzo, kuyimba, ndi kuvina kuti luso la achinyamata lioneke.
- Kupereka ngongole kwa anthu a maluso osiyanasiyana
- Kayendetsedwe ka dziko ndi kutengapo mbali kwa achinyamata
- Kusintha bungwe la National Youth Council (NYCOM) kuti likhale National Youth Commission ndi udindo wooneka wokhuza kukuza ntchito za achinyamata.
- Kugwira ntchito ndi achinyamata polimbana ndi mchitidwe wa ziphuphu
- Kuika m'maphunziro a sukulu za pulaimale ndi sekondale zinthu zokhuza chikhalidwe, umunthu ndi kudalirika ndi cholinga choti ana adziwe zimenezi ali achichepere.

**Za mauthenga, makompyuta ndi makina amakono**

- Kuika ndalama mu zipangizo za satellite ndi kuti tikweze ntchito zokhuza intaneti kumadera a kumudzi ndi cholinga choti intaneti idzakhale paliponse pofika chaka cha 2030.
- Kudzutsanso malo opangirako za intaneti m'madera a kumudzi (tele-centres) ndi cholinga chofuna kupititsa patsogolo ntchito za intaneti, maphunziro a ICT ndi malonda opanga mothandizidwa ndi Artificial Intelligence.
- Kutsitsa misonkho yoikidwa pa zipangizo za ICT ndi cholinga choti zinthu zoyendera makina ndi makompyuta zitsike mtengo.
- Kupereka ndalama zothandizira mapolojeketi achilendo omwe achinyamata angapange pa ulimi, zaumoyo ndi bizinezi

**Umoyo, kukhala bwino ndi chitetezo cha anthu**

- Kukhazikitsa kampeni yolimbana ndi kugwiritsa ntchito mankhwala ndi zinthu zozunguza bongo ndi kukhazikitsa malamulo okhwima pa mankhwala oletsedwa
- Kuonjezera ndalama zogwirira ntchito zokhuza

mapologalamu a umoyo wa achinyamata ndi umoyo wa kaganizidwe.
- Kuyendetsa pologalamu ya umoyo wa zogonana ndi ubereki msukulu za boma.
- Kuonjezera kaperekedwe ka madzi kwa anthu ndi kupereka udindo woona za kagwiritsidwe ntchito ka madzi ku makhonsolo a m'maboma.

**Kuika achinyamata mu kayendetsedwe ka zinthu ndi kupanga ziganizo**

- Kukonzanso lamulo loyendetsera maboma aang'ono (Local Government Act) ndi kulowetsa achinyamata awiri (wamkazi ndi wamwamuna) pa boma lirilonse ndi komiti ya pa wodi
- Kuika ndondomeko zoti achinyamata azitenga nawo gawo pogawa ndalama zogwirira ntchito pa boma.
- Kukhazikitsa mabungwe a achinyamata (Youth Advisory Councils) m'maboma kuti azipereka uphungu wokhuza mapulani a chitukuko.

**Kuteteza ndi kuthandiza achinyamata ovutika**

- Kuteteza achinyamata achialubino kudzera mu makomiti a chitetezo kumadera, ndi makampeni odziwitsa anthu za kuipa kopha anthu achialubino.
- Kupereka mwaulele mafuta omwe amagwiritsa ntchito anthu achialubino poteteza khungu ndi magalasi oteteza maso ku dzuwa.

DPP ikukhulupirira kuti achinyamata ndi atsogoleri lero ndipo akuyenera kutengapo mbali yokonza tsogolo la Malawi. Kudzera mu malonjezano amenewa, boma lathu lidzaonetsetsa kuti achinyamata apatsidwa mphamvu, akuoneka kufunika kwao, ndipo apatsidwa zida zopanga nawo chitukuko cha dziko lino. Tonse pamodzi tidzatha kumanga Malawi wabwino, wamtendere ndi wotukuka kwa aliyense.

### 5.5.4 MPHAMVU KWA AMAYI NDI KUCHITA ZINTHU MOSASIYANITSA PAKATI PA AMUNA NDI AMAYI

Ndondomeko ya Malawi 2063 ikuika patsogolo ntchito yopereka mphamvu kwa amayi ndi atsikana powapatsa mwayi wofanana ndi abambo, zinthu zowathandizira pamoyo wao, ndi kuwatumikira m'njira zoyenera, ndi cholinga choti atenge nawo mbali pa chitukuko, moyo wa tsiku ndi tsiku, ngakhale ndale zimene. Boma la DPP likudziwa kuti fuko limene liri losakondera mbali imodzi ndi limene limatsamira pa mphamvu za anthu onse, posayang'anira kuti ndi mwamuna kapena mkazi.

DPP imadziwa ntchito yofunika imene amayi amagwira pachitukuko cha dziko. Komanso DPP imadziwa zopysinja zimene amayi amakumana nazo chifukwa choti ndi amayi, monga mwayi wochepa wa maphunziro, zaumoyo, kuchepa kwa ndalama zochitira ma bizinezi ndi kusalidwa pantchito za ndale. DPP ikutsindika kuti idzaonetsetsa kuti amayi akupatsidwa mphamvu ngati ufulu wao, ndiponso ngati mfundo yofunikira potukula chuma cha dziko lino. Choncho kuyambira chaka cha 2025 mpaka 2030 DPP idzalimbikitsa ntchito yotukula amayi molingana ndi ndondomeko ya Agenda 2063 motere:

- Kukweza chiwerengero cha amayi mu ndale, mu Kabineti ndi ntchito zina zofunikira mogwirizana ndi kampeni ya 50-50 komanso migwirizano ndi maiko ena, pankhani yoonetsetsa kuti pakhale kufanana pakati pa amayi ndi abambo pakagwiridwe kantchito.
- Kuika pamodzi ndi kutsatira malamulo okhuzana ndi kagwiridwe ntchito kosasalana pakati pa amayi ndi abambo, monga kukhazikitsa kwa thumba la ndalama lothandiza amayi (Women Economic Empowerment Fund) kuti zifulumizitse ntchito ya 40:60 quota pankhani ya kupezeka kwa amayi ndi abambo muntchito zosiyanasiyana, zomwe



zili mu lamulo loti pasakhale kusiyana kwa kagwiridwe ka ntchito pakati pa amayi ndi abambo (Gender Equality Act ya 2013).

- Kukhazikitsa ndi kuika ndalama zokwana 100 miliyoni kwacha mu Women's Economic Empowerment initiative and entrepreneurship development ku dera la phungu
- Kuunika ndi kuyendetsa ndondomeko zothana ndi maukwati a ana achichepere yotchedwa National Strategy for Ending Child Marriage , ndi pulani yothana ndi nkhanza zochitika pakati pa anthu aamuna ndi aakazi yotchedwa National Plan of Action to Combat Gender-Based Violence.
- Kupitiriza kumanga malo ogona atsikana kuti tionjezere chiwerengero chawo pa maphunziro.
- Pogwirana manja ndi mabungwe ndi maiko otithandiza, kukweza kaperekedwe ka madzi abwino ndi njira zaukhondo.
- Kukhazikitsa mgwirizano wabwino pakati pa boma, ndi mabungwe ndi makampani omwe siaboma kuti maukwati a pakati pa ana athe, ndi kupititsa patsogolo kagwiridwe kantchito kokomera abambo ndi amayi.
- Kuunikanso ndi kulimbikitsa malamulo opereka mphamvu kwa amayi pantchito za chitukuko yotchedwa Legal and Policy Framework on Women's Empowerment poonetsetsa kuti ndi la chikwanekwane poika amayi mu ndondomeko zoyendetsera dziko ndi mapulani a dziko.
- Kuika m'malo njira zokhazikika zoteteza amayi ku mavuto, zimene zinathandiza amayi oposa 1.5 miiliyoni nthawi ya ulamuliro wa DPP m'mbuyomu, kudzera mu mapologalamu osiyanasiyana. Mwachitsanzo, ndondomeko yopereka ndalama inali yopambana kwambiri moti 73 peresenti ya anthu amene analandira ndalama zimene zija anali amayi oyendetsa makomo awo paokha
- Kuonetsetsa kuti mabungwe amene akugwira ntchito zoteteza anthu pamavuto osiyanasiyana akugwira ntchito molumikizana kuti anthu onse akalandire chithandizo mofanana, ndi kukwezanso chiwerengero cha anthu olandira chithandizocho
- Kupitiriza ntchito yoti amayi a kumidzi azichita ntchito zobweretsa chuma pa miyoyo yawo monga malonda ochita ndi maiko ena (trans-border), ulimi wa bizinezi, ndi mabizinezi ang'onoang'ono ndi okulirapo (SMEs)
- Kuonetsetsa kuti ntchito zoteteza anthu ku umphawi zikuchitika bwino, monga kaperekedwe ka ndalama zokwanira ku ntchitozo, komanso kugwiritsa ma kompyuta ndi makina pa ntchitozi kuti zizichitika mosavuta.
- Kuphunzitsa amayi maluso oti awathandize pa ntchito zawo, kudzera mu maphunziro a umisiri ndi cholinga choti azitenga nawo gawo pa chitukuko ndi kukhala ndi kuthekeka kodziimira paokha.
- Kulimbikitsa ulimi wobweretsa ndalama pakati pa amayi. Kotero tidzachita chotheka kuti amayi akhale ndi minda, misika ndi zipangizo za makono zowayenereza amayiwa kuchita ulimi wa ndalamawu.
- Tidzalimbikitsa kaganizidwe koona kufunikira kwa amayi pa kutengapo mbali pa kupanga ziganizo, ndi utsogoleri m'madera osiyanasiyana a dziko.
- Kukonza mapologalamu a daladala othandiza kuthetsa mavuto amene amayi ndi atsikana amakumana nawo kaamba ka kusintha kwa nyengo, monga kusefukira kwa madzi ndi namondwe.

### 5.5.5 ANTHU OSOWA, ACHIKULIRE NDI AMAULUMALI

Ndondomeko ya Malawi 2063 ikukhumba kufikira muyeso wopanga chuma kudzera mu nzeru. Uyu ndi Malawi amene adzakhala ndi ogwira ntchito amene ali ndi maluso apamwamba poyerekeza ndi ena onse a padziko lapansi. Tikudziwa kuti tikhale ndi chuma chokwanira aliyense ndi kudzidalira pa chuma chochokera m'mafakitale pokwana chaka cha 2063, sitingasiye m'mbuyo anthu achikulire ndi awo amene ali ndi maulumali osiyanasiyana. Achikulire kapena okalamba ambiri achitidwa nkhanza zosiyanasiyana, ndipo nthawi zina kunamiziridwa kuti ndi mfiti, popanda umboni. Pakati pa 2020



ndi 2025, pafupifupi amayi 160 aphedwa powaganizira kuti ndi mfiti m' Malawi muno.

Zinthu zambiri monga nyumba, miseu ndi njira zoyendera m'Malawi muno sizinamangidwe molabadira zosowa za anthu a maulumali. Anthu a maulumali ndi okalamba ayenera kulumikizana ndi mitundu ina yonse ya anthu nkupanga fuko limodzi, ndi kutenga nao mbali pa chitukuko. Ayeneranso kukhala ndi chitetezo ku mavuto osiyanasiyana ndi kusawasankha mu zochitika za m'dziko.

Bungwe la maiko onse loona za ufulu wa anthu a maulumali lotchedwa UN Convention on Rights of Persons with Disability limalimbikitsa mfundo za ulemu, kusawasankha, kuwalola azichita nawo zinthu, kuchita zinthu mofanana ndi kuwapatsa mwayi anthu otere.

Nkhani za kudzipha zikuchulululukirabe, ndiponso zafika pamuyeso wokhala ngati mliri. Mwachitsanzo, anthu 153 adzipha mchigawo choyamba cha chaka cha 2025 chokha. Anthu 80 mwa anthu 100 a gulu limeneli (80 peresenti) ndi amuna. Lamulo loti ukadzipha waswa lamulo likupangitsanso ambiri kuti alephere kufikira anthu ena kuti awathandize akakumana ndi zopysinja.

Ana oyendayenda m'miseu yathu ya m'matauni akuchulukira, kwenikweni chifukwa cha kuchuluka kwa umphawi ndi kusowa kwa thandizo kwao. Ambiri mwa ana amenewa sanatsirize sukulu ya pulaimale, ndipo salinso pantchito. Choncho amangolowerera njira zaumbanda kuti azipeza chowathandiza. Akagwidwa amamenyedwa kapena kuphedwa kumene.

Chipani cha DPP chimakhulupirira kuti ngati wina aliyense atenga nawo mbali, chuma chathu chidzapita mtsogolo. Potero, tidzathana ndi mavuto ambiri amene anthu okalamba, aulumali ndi achialibino, ndi ana oyendayenda m'miseu amakumana nawo.

Kuchokera m'chaka cha 2025 mpaka 2030, DPP idzachita izi:

- Kuika ndalama zochuluka mu mabungwe oona mavuto amene anthu aulumali amakumana nawo monga, Disability Trust Fund ndi Malawi Council for Disability Affairs (MACODA) pofuna kuti mapologalamu ndi ntchito zawo ziziyenda bwino.
- Kuthandiza okalamba amene amakhala okha kupeza malo okhala ku nyumba za anthu okalamba (old people's homes). Ndalama zochitira izi zidzachokera ku khonsolo ya paboma.
- Kuthandiza anthu okalamba ndi ovutika ndi mankhwala, zovala, chakudya ndi malo okhala.
- Kuchita machawi polongosola ndi kupereka ndalama za anthu opuma pantchito
- Kubweretsanso ntchito zimene anthu amagwira ndi kulandirapo ndalama za boma
- Kumanga nyumba ndi zinthu zina mokomera anthu okalamba, aulumali ndi achialibino
- Kupereka zithandizo kwa anthu amene ali ndi HIV ndi AIDS ndi enanso amene akhuzidwa
- Kuchotsa misonkho pa katundu wothandiza anthu amene ali ndi maulumali ndi ena ovutika, ndi cholinga choti anthu ambiri akathandizidwe
- Kunonetsetsa kuti malo ophunzirirapo anthu a maulumali akupatsidwa ndalama zokwanira ndipo akugwira ntchito nthawi zonse
- Kuthandizira ntchito za bungwe la National Coordination Committee on Disability Issues
- Kuunikanso mfundo za TEVET ndi ndondomeko zina
- Kugwira ntchito mogwirizana ndi mabungwe ena muno m'Malawi, m'chigawo chino cha Africa ndi m'maiko ena
- Kuonetsetsa kuti ntchito za njuga zikutsata malamulo
- Kuonetsetsa kuti anthu osowa akulandira chilungamo chofanana ndi anthu ena onse

- Kuyendetsa bwino ndondomeko zoteteza anthu achialubino
- Kukhazikitsa ndondomeko zabwino ku midzi, m'chigawo ndi m'dziko lonse posankha anthu amene ali ndi ulumali pa maundindo a ndale, ndi kusintha zinthu zina mokomera anthu a ulumaliwa
- Kuphunzitsa ana oyendayenda m'tauni umisiri ndi maluso ena, kuti athe kumagwira ntchito ndi kupeza ndalama.
- Kuchotsa ana oyendayenda pamseu ndi kuwaika m'malo a chisamaliro.

## 5.6 NKHANI ZOSAMALA CHILENGEDWE NDI KUPEWA NGOZI ZODZA MWADZIDZIDZI

Kusintha kwa nyengo ndi kuonongeka kwa chilengedwe sizilinso patali; zinthu izi zili pakati pathu tsopano, ndipo zikukhuza miyoyo yathu pa nkhani za umoyo, chuma, ndi madera amene tikukhala, ndi zinthu zachilengedwe. Mpweya umene tikupuma, madzi amene tikumwa, ndi nthaka imene tikugwiritsa ntchito, zonse zili pa chiopsyezo, osati kuchokera ku ngozi zachilengedwe zokha, komanso kuchokera mu zochita za anthu.

### 5.6.1 KUSINTHA KWA NYENGO

Kusintha kwa nyengo kumene kwadza chifukwa cha kuotcha tchire , kudula mitengo ndi njira zina zosasamalira chilengedwe, zikupangitsa kutentha kwakukulu. Zimenezi zikubweretsa mavuto ambiri monga kusefukira kwa madzi, mphepo yamkuntho, zilala, moto wolusa, ndi zina zotero. Zinthu zimenezi zikuopsyeza miyoyo ya anthu, kuononga chuma ndi kupangitsa kusamuka kwa anthu ambiri amene ali ovutika kale, omwenso sanathandizire kwenikweni pa kusintha kwa nyengoyo.

DPP imadziwa mavuto amene amakhuza nyengo ndi madera amene kumakhala anthu ndi zolengedwa monga, kutentha kwa dziko lonse, kuonongeka kwa zinthu zachilengedwe, kuonongeka kwa chuma, kuonongeka kwa mpweya, chilungamo chokhuza chilengedwe, nkhani za ndondomeko, za makina, sayansi ndi makompyuta, nkhani za ndalama zogwirira ntchito za kusintha kwa nyengo ndi kuchulukana kwa anthu padziko, mwa zina.

Choncho, pakudzipereka kwathu pa zatsogolo la dziko lapansi kuti likhale labwino kufikira mibadwo imene ilinkudza, Chipani cha DPP chikuima pa chikhulupiriro choti chuma chopangidwa mosaononga chilengedwe nchotheka ndiponso chofunikira. Pamodzi ndi a Malawi onse, titengapo mbali yoteteza chilengedwe kuti tichepetse mavuto obwera ndi kusintha kwa nyengo, ndi kukhala ndi dziko la chilungamo komanso lokhazikika.

Mwachindunji boma la DPP lidzachita izi:

- Kutukula ntchito zobwezeretsa chilengedwe
- Kuika ndalama zokwanira mu ntchito zoteteza chilengedwe
- Kuika ndalama zokwanira mu zipangizo zopangira mphamvu ya magetsi am'bwereza
- Kukhazikitsa ndondomeko zogulitsa mpweya woipa wa carbon
- Kulimbikitsa njira zokhazikika zopangira ulimi, kusunga madzi ndi kagwiritsidwe ntchito ka nthaka;
- Kulimbikitsa chuma chobwerezabwereza kuopa kuonongeka kwa chuma
- Kuletsa mchitidwe wopanga ma plastic ogwiritsa ntchito kamodzi nkutaya
- Kugwiritsa ntchito njira zochepetsa kuonongeka kwa mpweya ndi madzi chifukwa cha mankhwala a m'mafakitale;
- Kukhazikitsa malamulo a mphamvu, oletsa kuonongeka kwa mpweya, nthaka ndi madzi
- Kulimbikitsa kuika ndalama zokwanira mu zipangizo zosaononga chilengedwe monga malo ochezera (parks), madenga ndi nyumba zodya bwino mphamvu zamagetsi.

- Kuonetsetsa kuti nyumba zatsopano za m'mataunni zikumangidwa potsatira ndondomeko za kusunga ndi kuteteza chilengedwe.
- Kukonza, kuyendetsa ndi kulimbikitsa mfundo zamphamvu zoteteza chilengedwe
- Kulimbikitsa ulimi wotsatira mfundo za kusunga chilengedwe ndi kuteteza nyengo
- Kulimbikitsa njira zabwino zotayira zinyalala
- Kuika ndalama zokwanira ndi anthu odziwa ntchito zokhuzana ndi kusunga bwino mitengo ndi tchire
- Kulimbikitsa ndi kuikapo mtima pa pologalamu yobzala mitengo mdziko lonse
- Kuonetsetsa kuti maphunziro a ana a ku pulaimale ndi sekondale muli zokhuzana ndi chilengedwe ndi kusintha kwa nyengo
- Kulimbikitsa ndi kuthandiza magulu amene akuchita ntchito yokhuzana ndi chilengedwe, kapena kusintha kwa nyengo

## 5.7.2 KUPEWA NGOZI ZOGWA MWADZIDZIDZI

Dziko la Malawi likukumana ndi mavuto ogwa mwadzidzidzi ambiri; ena mwa awa ndi obwera mwa chilengedwe pomwe ena ndi opangidwa ndi anthu. Mavutowa ndi kusefukira kwa madzi, chilala, mvula yamphepo, mphepo yamkuntho, chivomerezi, kukokoloka kwa nthaka, tizilombo toononga mbeu, matenda ongobuka, moto ndi ngozi, mwa zina. Mavuto a dzidzidziwa akhala akuchulukira m'zaka zimenezi chifukwa cha kusintha kwa nyengo, kuchulukana kwa anthu, kuchuluka kwa anthu m'matauni ndi kuonongeka kwa chilengedwe.

Mwachitsanzo, kusefukira kwa madzi ndi chilala zikuchulukira komanso kuchitika mwamphamvu. Cyclone Idai amene anaomba mu miyezi ya Malichi ndi Meyi wa chaka cha 2019, anakhuza anthu 868,900; Ndipo anthu 86,980 anasamukira madera ena ndipo anafuna chithandizo. Mwa anthuwa, 45,000 anali amayi.

Dziko lino linakhuzidwanso ndi namondwe wa Freddy mu Malichi wa chaka cha 2023. Mphepo iyi inali yoopsya kwambiri mu mbiri ya kum'mwera kwa Africa ndi Malawi. Namondweyi anapangitsa kuti anthu 1.4 miliyoni achoke malo awo okhala ndi kuthawira madera ena m'maiko asanu ndi limodzi kum'mwera ndi kum'mawa kwa Africa. Chiwerengero ichi ndi kawiri ka chiwerengero chimene chidakhuzidwa ndi namondwe wa Idai mu 2019. Ndipo anthu oposa 659,000 adakhuzidwa kuno ku Malawi, chimene chili chiwerengero chokwera kwambiri kuyambira chaka chimene tinayamba kulemba ndi kusunga mbiri ya zinthu ngati izi mu 2009. Miseu, milatho ndi zipangizo za magetsi zinaonongeka, kwenikweni kumidzi ndi kubweretsa mavuto ambiri pa kuperekera kwa chakudya ndi chithandizo kwa anthu okhuzidwa. Izi zinapangitsa kuti vuto la chakudya likhale lalikukulu kwambiri. Kuonjezera apo, nkuti dziko la Malawi likungoyamba kumene kuchira kuchokera ku mavuto amene anabwera ndi Namondwe wa Ana ndi Gombe m'chaka cha 2022.

Monga m'mene kulili kusefukira kwa madzi, chilala ndi vuto limene limadza kawirikawiri m'Malawi muno. Chilala chabweretsa kusowa kwa chakudya ngati m'zaka za 2005, 2012, ndi 2016/2017 chifukwa cha Namondwe wa El Nino. Chilala cha 2016/2017 chinaika anthu okwana 6 miliyoni pa njala, ndipo kunafunika kuwapatsa chithandizo. Ponena zoona, mavuto ogwa mwadzidzidziwa amaononga njira zimene anthu amakhalira ndi moyo. Amaononganso miyoyo, chakudya cha anthu, zipangizo zofunika pa miyoyo ya anthu, ndipo anthu amapsyinjika pa nkhani ya za chuma ndi chitukuko cha dziko. Mavuto ogwa mwadzidzidzi amabweretsanso umphawi kwa anthu a m'tauni ndi kumudzi komwe, ndipo amachotsa kuthekeka kwa dziko kuti liike chuma chake mu ntchito zomwe zingathandize pa chitukuko cha dziko ndi kupanga chuma.

Zinthu zimene zimalimbikitsa mavuto ogwa mwadzidzidzi ndi kusintha kwa nyengo, ndi machitidwe monga awa: kuchepa

kwa njira zochenjezera anthu mu nthawi yabwino; kukonzekera kosakwanira; zipangizo zosakwanira; umphawi ndi kuchita kakasi; kupanda mgwirizano wabwino pakati pa mabungwe ogwira ntchitoyi, kuchepa kwa ndalama zogwirira ntchitoyi; kudula mitengo ndi kuononga kwa chilengedwe; kusakwanira kwa zipangizo za chipatala pamene ngozi yagwa; kusaika ndondomeko zothana ndi mavutowa mu ma pulani a boma a chitukuko, ndi kudalira kwambiri pa chithandizo chakunja.

Choncho pakufunika kuti pakhale ndondomeko zabwino zothana ndi mavuto odza ndi ngozi za dzidzidzi ndi cholinga choti pakhale chitukuko cha miyoyo ya anthu ndi chuma chabwino, kudzera mu kusintha kwa kayendetsedwe ka ntchito zolimbana ndi vutoli, mwa zinthu zina.

Pa chifukwa cha ichi, boma la DPP lidzachita izi:

- Kuika patsogolo kusintha kwa kayendetsedwe ka ntchito zolimbana ndi mavuto ogwa mwadzidzidzi;
- Kukhazikitsa bungwe loona ngozi zogwa mwadzidzidzi lotchedwa National Disaster Risk Management Authority;
- Kuyendetsa thumba logwirira ntchito za ngozi zogwa mwadzidzidzi lotchedwa Disaster Risk Management Fund;
- Kuika ndondomeko za kupewa ngozi zogwa mwadzidzidzi mu Ulimi, Maphunziro, Umoyo, Mtengatenga, zomangamanga, mapulani a m'matauni ndi chitukuko ndi mu zokopa alendo.
- Kukhazikitsa mwezi wochita za fuko lopilira kungozi zogwa mwadzidzidzi (National Disaster Resilience Month);
- Kukonzanso ntchito za ngozi zogwa mwadzidzidzi m'maboma aang'ono;
- Kumanga fuko lopirira ku ngozi zogwa mwadzidzidzi
- Kuika patsogolo mapologalamu ochepetsa ululu wodza ndi kusintha kwa nyengo;
- Kulimbikitsa njira zabwino zoyendetsera malo amene anthu, nyama ndi zomera zimakhala
- Kupereka kuthekera kwa asirikali a chitetezo pa nkhani za ngozi zogwa mwadzidzidzi molingana ndi ukatswiri ndi zipangizo zofunikira pantchitoyi
- Kupereka chidziwitso kwa anthu onse za ngozi zogwa mwadzidzidzi ndi kusamala kwa chilengedwe
- Kuunikanso maphunziro a m'sukulu za pulaimale ndi sekondale ndi kuikamo nzeru ndi maluso okhuzana ndi ngozi zogwa mwadzidzidzi
- Kukhazikitsa njira zochenjezera anthu mu nthawi yake za ngozi zogwa mwadzidzidzi;
- Kumanga malo othawirako anthu mu nthawi ya ngozi zogwa mwadzidzidzi m'madera amene izi zimachitika kawirikawiri.

## 5.7 MABUNGWE OMWE SIABOMA: ATOLANKHANI, MABUNGWE ENA NDI ZIPEMBEZO

Ndondomeko za Malawi 2063 zikunena za kukhumba kokhala ndi dziko lomwe anthu onse, ali ndi chuma, lodzidalira, ndipo la pakati ndi pakati pa chitukuko chothandizidwa ndi ntchito za mafakitale pokwana chaka cha 2063. Ndipo ndondomeko yomweyo ikunena za masomphenya a Malawi wogwirizana, wamtendere ndi wa anthu onyada, mothandizidwa ndi kayendetsedwe kadziko kabwino, ndi kusintha kwa kachitidwe ka zinthu.

Chipani cha DPP chikudziwa udindo wa anthu olemba ndi kufalitsa nkhani, mabungwe oona za anthu wamba, ndi a zipembedzo pomanga dziko. Magulu amenewa amathandizira anthu kulankhulapo pa zochitika m'dziko, kufalitsa nkhani, kunenapo za kayendetsedwe ka dziko, ndi kulimbitsa mchitidwe wogwira ntchito molimbika ndi umodzi pakati pa anthu.

DPP imalimbikitsa ufulu wa kulankhula monga chinthu chofunikira mu boma la demokalase, ndi kulola kuti nkhani zizifalitsidwa mosavuta. Pakati pa 2014 ndi 2019 boma la DPP linaonetsa kudzipereka pa ntchitoyi posainila lamulo loti anthu azipeza nkhani mosavuta kudzera mu lamulo lotchedwa Access to Information Bill m'chaka cha 2017. Chipanichi chimakhulupirira mu ufulu wa atolankhani popewa kumanga




SONY
Canon

olemba nkhani ndi kulola nyumba zoulutsa ndi kulemba nkhani kugwira ntchito zawo popanda zipysinjo.

Poonjezera apo, boma la DPP limazindikira udindo wa mabungwe a chipembezo pothandiza anthu kukhala ndi chikhalidwe chabwino ndi kusintha miyoyo ya anthu, pamene mabungwe oona za anthu wamba ndi ofunikiranso kuthandiza boma kuchita zinthu motsata malamulo a dziko. Kuyambira chaka cha 2025 mpaka 2030 DPP idzaonetsetsa kuti Malawi ndi waufulu, ndi wopita mtsogolo pochita izi:

- Kutsatira lamulo la Access to Information ndi kutsegula nyumba zoulutsa nkhani zimene zinatsekedwa chifukwa cha ndale
- Kukonzanso ntchito za Malawi Communications Regulatory Authority (MACRA) ndi kubwezeretsa likulu lake ku Blantyre.
- Kuonetsetsa kuti pali ufulu wa atolankhani powalola kugwira ntchito zawo popanda kuvutitsidwa ndi boma.
- Kuteteza ufulu wa olemba ndi kufalitsa nkhani kudzera m'njira zonse za manyuzipepala, wailesi, kanema ndi njira za kompyuta.
- Kukonzanso ntchito za Malawi Broadcasting Corporation (MBC) ndi kuona njira zina zothandizira ntchito zake pa ndalama zochokera m'thumba lotchedwa Content Creators Fund
- Pakugwiritsa ntchito ndalama za mu Content Creators Fund, tidzachotsa kulengeza kwa malonda pa MBC ndi cholinga choti makampani omwe siaboma azikachita izi popanda mpikisano kuchokera ku bungwe loti limalandira ndalama zaboma zochitira ntchito zake.
- Kukhazikitsa metro stations pogwiritsa ntchito ndalama zochokera mu Content Creators Fund m'madera awa: Mzuzu, komwe mapologalamu akakhala m'Chitumbuka, Chitonga ndi Chingoni; ku Mangochi komwe mapologalamu akakhala m'Chiyao; ku Mulanje komwe mapologalamu akakhala m'Chilomwe, ndi ku Nsanje komwe mapologalamu akakhala m'Chisena. Ma siteshoni amenewa azikalimbikitsa nkhani za chikhalidwe ndi chinenero cha kumeneko.
- Tidakhazikitsanso wailesi ya ana pogwiritsa ntchito ndalama za mu Content Creators Fund. DPP ikudziwanso kuti ana ndi amene adzatengere dzikoli ku chaka cha 2063 ndi kupyola apo.
- Kulimbikitsa ufulu wa ndale poonetsetsa kuti mabungwe onse akutengapo mbali pa ndale, chuma, umoyo wa anthu ndi ntchito za chikhalidwe chathu
- Kugwira ntchito ndi mabungwe a chipembezo kuti tikathe kukhazikitsa kufunikira kwa kukonda dziko lathu, kugwira ntchito molimbika, ndi kukhulupirika ndi ulemu wa fuko la Malawi
- Kuonetsetsa kupezeka kwa atsogoleri a mipingo m'magawo onse opangiramo ziganizo zokhuza anthu
- Kupereka mpata kwa mabungwe omwe siaboma wophunzitsa anthu za maufulu a anthu ndi kayendetsedwe kadziko kabwino.
- Kugwira limodzi ntchito ndi mabungwe omwe siaboma pochita chitukuko cha dziko lino
- Kupanga mgwirizano ndi anthu ndi mabungwe omwe sali mbali imodzi ya boma pantchito za mabungwewa, monga atolankhani ndi mabungwe a chipembezo.

## 5.8 NTCHITO ZA MALUSO

DPP ikudziwa kuti ntchito za anthu a luso zikhoza kubweretsa ndalama zochuruka ku chuma cha dziko lino. DPP ikudziwa kuti tikati ntchito zaluso tikunena zinthu izi: kulemba nthano zopeka ndi zosapeka, kulemba nyimbo, kukonza ndi kujambula nyimbo mu studiyo,kuimba pagulu, ndakatulo, zisudzo, makwaya, kuvina, zopenta, ziboliboli, kujambula kwa pa kompyuta, kujambula zithunzi, mafashoni ndi kusoka, zomangamanga, kanema ndi zina zotero.

DPP idzachita izi pokweza ntchito zimenezi ndi kuthandiza anthu alusowa kupeza ndalama ndi kuthandizira kukula kwa chuma cha dziko potere:

- Kukambirana ndi TickTock, YouTube, Instagram ndi ena otero kuti azipereka ndalama kwa a Malawi amene ntchito zawo zimagwiritsidwa ntchito pa masamba a mchezo amenewa
- Kukhazikitsa thumba la National Content Creator Fund lokwezera ntchito kapena nkhani za chikhalidwe.
- Kukhazikitsa situdiyo yamakono yopangirako kanema. Situdiyo imeneyi idzayendetsedwa pa ndondomeko za Public-Private Partnership pamenenso ikugwira ntchito ngati malo ophunzirirapo kapangidwe ka kanema kwa achinyamata athu. Ophunzirawo adzakhalanso kuti alembedwa ntchito ya pa ola ku Situdiyo'yo.
- Kukhazikitsa Situdiyo yojambulira nyimbo ku sukulu ya ukachenjede ya Malawi University of Science and Technology pa ndondomeko ya Public-Private Partnership pamenenso ikugwira ntchito ngati malo omwe achinyamata athu azikaphunzirapo kujambula kwa nyimbo. Ophunzirawo adzakhalanso kuti alembedwa ntchito ya pa ola ku Situdiyo'yo.
- Kupeza kampani imene ingathandize kukonza ndi kuyendetsa Blantyre Cultural Centre pa ndondomeko za Public-Private Partnership.
- Kupeza kampani imene ingathe kumanga ndi kuyendetsa malo opangirako ntchito za luso ku Lilongwe ndi ku Mzuzu.
- Kukhazikitsa ndondomeko za public-private partnerships pomanga ndi kuyendetsa malo opangirako ntchito za luso ku maboma ndi ma tauni.
- Kukhazikitsa mapologalamu a anthu olemba mwaluso pa mulingo wapamwamba ku sukulu zaukachenjede, ndi kuti zolembazo zikakhale pa levulo yotha kupikisana pamsika ndi zolemba zakunja.
- Kuunikanso lamulo la Copyright ndi cholinga choti amene amakonza nkhani (content creators) azipindula ndi ntchito zawo muno m'Malawi komanso kunja kwa dziko lino.

**KUMEMEZA AMALAWI NDI ABWENZI ATHU ONSE**

6

# KUMEMEZA AMALAWI NDI ABWENZI ATHU ONSE



Tikutsimikizira a Malawi onse kuti: Kuvotera Chipani champhamvu cha DPP pa 16 Sepitembala 2025 pano, chidzakhala chinthu chokhacho chokomera dziko la Malawi. DPP ili ndi mbiri yoposa mbiri ya zipani zonse pakuyendetsa bwino ntchito za chuma m'Malawi muno. Choncho DPP ndi yokonzeka kubwezera chuma cha dziko lino m'chimake ndi kuika ndondomeko zimene zichotse dziko lino pamoto wa umphawi chifukwa cha utsogoleri wosadziwa kuyendetsa chuma umene ulipo pano. Povotera DPP mukupulumutsa dziko la Malawi ku chionongeko chachikulu chomwe sichinaonekeponso.

***Kwa anzathu a maiko ena, maiko ndi mabungwe othandiza dziko lino, mabungwe ogwirizana nafe paubale wauwiri kapena ochurukirapo ndi ena otero:***

Tikukutsimikizirani za kubweretsanso utsogoleri wodalirika ndi wokhulupirika pakagwiridwe kantchito za boma; kotero kuti tikhoza kuchita malonda limodzi. Boma la DPP lidzakambitsana ndi abwenzi ake onse moona mtima ndi kukwaniritsa zonse zimene tagwirizana mu mapangano athu.

***Kwa atolankhani:***

Tikupempha kuti mugwirane manja ndi DPP pamene tikukhazikitsa boma lina limene lidzabwezeretsa ndi kulemekeza ufulu wa atolankhani; boma limene silidzatupysa atolankhani, kapena kuwamanga poyankhula za kukhosi. Monga mukudziwa, mbiri yathu pa nkhani ya ufulu wolemba ndi kuulutsa nkhani ndi yabwino kwambiri.

***Kwa atsogoleri a zipembezo:***

Ife a DPP tikukutsimikizirani kuti boma lathu lidzatsata ubale wodalirana ndi kupereka ulemu pakati pa boma ndi magulu onse a zipembezo. Tikubweretsa boma limene lidzagwira ntchito ndi onse a zipembezo kuti titumikire bwino anthu amene inunso mumawatumikira ku mbali ya chipembezo.

***Kwa ogwira ntchito za boma:***

Tikudziwa kuti ntchito zimene mumagwira ndi moyo ndi magazi amene amayendetsa boma. Tikudziwa kudzipereka kwanu potumikira Mayi Malawi. Tagwira nanu ntchito ndipo tikudziwa m'mene mumadziperekera pantchito yanu. Boma la DPP limene likubwera pa 16 Sepitembala lidzakuchitirani zabwino zimene boma liripoli lalephera kukuchitirani m'zaka zisanu zapitazi, poyamikira kudzipereka kwanu ndi kudzipereka kwanu nsembe pogwira ntchito.

***Kwa inu ana asukulu:***

Taona m'mene mwazunzikira m'zaka zisanu zapitazi chifukwa cha kulephera kwa boma limene liripoli. Ife a DPP tikudziwa zoti tichite kuthandiza kuti mukhale ndi malo ophunzirira osapereka chiopsezo ku miyoyo yanu, komanso othandizira kuti maphunziro anu ayende bwino. DPP yakonzeka kuthana ndi mavuto amene mukukomana nawo ndi nkhawanso zimene muli nazo.

***Kwa inu a mabungwe ndi anthu ena oimilira anthu wamba, mwa magulu ena:***

Ife a DPP tikulonjeza kuti tidzapereka malo okwanira ndi oyenera kuti muzitha kugwira ntchito zanu mwaufulu. Tidzaika ndondomeko zoti mudzagwiritse ufulu wanu wakuyankhula pa nkhani zimene zikukhuza anthu amene mumawaimilira, ndi cholinga choti a Malawi amve kukoma maufulu onse amene ali m'Malamulo a dziko lino. Ife sitidzaletsa ufulu wakukumana ndi kupereka mavuto amene mukukumana nawo kwa adindo kudzera mu zionetsero (demonstrations), ngati zimene boma ili likuchita. Ife a DPP tili ndi mbiri yachikhalire pakulola a Malawi kuyankhula za kukhosi kudzera mu mademo.

Choncho tikumemeza aliyense amene ali ndi zomuyenereza kuvota kuti pokavota pa 16 Sepitembala 2025 pano, akavotere Chipani champhamvu cha Democratic Progressive Party, ndi Mtsogoleri wake wabwino kwambiri, mlerakhungwa, wokonda anthu, wodekha, tate wa fuko, woyendetsa bwino chuma cha dziko, wokonda mtendere, His Excellency Professor Arthur Peter Mutharika.

***KUVOTERA DPP NDI NJIRA YODALIRIKA YOIKA DZIKO LA MALAWI PA MSEU WA KUPAMBANA. IFE A DPP TIMALONJEZA ZOMWE TIDZATHE KUCHITA, NDIPO TIMACHITA ZOMWE TINALONJEZA!***

***VOTERANI DPP! BOMA LA A PETER!***
***APM WOYEEE! DPP WOYEEEE! MALAWI WOYEEEE!***




WACHITUKUKO,WACHIKONDI
OWOPA MULUNGU

